**Hakîkat Kitâbevi Publications No: 1**

# CHIKHULUPILIRO NDI CHISILAMU

**Lolembedwa ndi**
**MAULANA DIYA AD-DIN KHALID AL-BAGHDADI**
**(1778-1826)**

**Lotanthauzidwa m'chi Turkish ndi:**
**HÜSEYN HİLMİ IŞIK**

**Lotanthauzidwa m'chi Ngelezi ndi:**
**Hakikat Kitâbevi**

**Shagon Littattafai na Hakikat**
Darussefeka Cad. 53/A PK: 35
34083 Fatih, ISTANBUL/TURKEY
Tel: 90.212.523 4556 Fax: 90.212.523 3693
www.hakikatkitabevi.com
e-mail: info@hakikatkitabevi.com
Januwale 2024

# Zam’katimu

MLEMBI ..... 3
CHILOLEZO CHOSINDIKIZA ..... 3
MAU OYAMBA ..... 5
CHIYAMBI ..... 11
IMAN NDI CHISILAMU ..... 17
NSICHI ZA CHISILAMU (1) ..... 21
NSICHI ZA IMAN (2) ..... 27
KUFUNIKA KOGWIRITSA NTCHITO NJIRA ..... 81
ALLAHU TAALA ALIKO NDIPO NDI MMODZI ..... 89
“SALAFIYYA” ..... 97
MATANTHAUZO A MAWU ENA ..... 114

# MLEMBI

Mlembi wa bukhu ili, lotchedwa **Itiqad-nama**, yemwe ndi Maulana Diya ad-Din Khalid al-Baghdadi al-uthman (quddisa sirruh)[1] anabadwira kudera la Shahrazur ku mpoto kwa Baghdad m'chaka cha 1778/1192[2] ndipo anamwalira m'chaka cha 1826/1242. Iye ankatchedwa Al-uthman chifukwa anali wobadwa kuchokera kwa Uthuman Dhun Nurain, Khalifa wa chitatu (Allahu Taala asangalale naye). Pophunzitsa **hadith al-jbril** kwa mng'ono wake Hazrat Maulana Mahmud sahib, mchimwene wake anamupempha kuti alembe ndemanga ya Hadith imeneyo. **Hadith al-jbril** ndi yodziwika bwino, yomwe ndi hadith Sharif yachiwiri (zonena za mtumiki Muhammad alaihi-salam). Maulana Khalid, pofuna kukondweretsa mtima wa m'bale wakeyo, anavomera pempholo ndipo anafotokoza hadith yolemekezekayi mchiyankhulo cha chi Persia m'bukhu lotchedwa **Itiqad-nama**. Kutanthauzila kwake m'chiyankhulo cha chi Turkey ndi **Herkese lazm Olan Iman.** Bukhu la chi Turkey ili, linamasuliridwa m'Chingelezi ndipo mutu wake ndi **Belief and Islam**. Tsopano tikulimasulira bukhuli m'Chichewa ndi kulisindikiza ndi mutu woti **Chikhulupiliro ndi Chisilamu.** Bukhuli linanthauzidwiranso m'chi French -**Foi et Islam,** komanso mu chi Germany -**Glaube und Islam** mchaka cha 1969. Kenako, m'zinenero zina zingapo, monga chi Tamil, chi Yoruba, Hausa, Malayalam ndi chi Danish. Allahu Taala adalitse achinyamata osalakwa powerenga bukhuli ndi kuphunzira itiqad (iman, zikhulupiriro) zolondola zoperekedwa ndi akatswiri a Ahl as-Sunna!

# CHILOLEZO CHOSINDIKIZA

Aliyense wofuna kusindikiza bukhuli mosasintha kanthu kapena amene akufuna kulimasulira m'chinenero chilichonse ali ololedwa kutero; ndipo amene achita ntchito yabwinoyi adzavomerezedwa ndi madalitso omwe tikupempha kwa Allahu Taala m'dzina lawo komanso tikuwafunira mafuno abwino moyamika ndi tikuwathokoza kwambiri. Koma chilolezochi chidzatengera kuti kumasulira kwake ndi kolondola komanso kowona ndipo pepala logwiritsa ntchito posindikiza ndi labwino kwambiri. Kakhonzedwe ndi kayalidwe ka zilembo kakhale koyenera komanso kaudongo popanda kulakwitsa.

---

[1] Manenedwe a ulemu a ma Wali kutanthauza kuti, 'Allahu Taala apange zinsinsi zake Mkukhala zabwino, zopatulika ndi zodala'.

[2] Chiwerengero cha zaka chaperekedwa kalendala ya Gregorian, kenako mu kalindala ya Chisilamu -Hijra.

**Chidziwitso:** Mamishonale amayesetsa kufalitsa Chikristu; Ayuda anafalitsa ziphunzitso za Talmud, ndipo a Freemason amayesetsa kuwononga zipembedzo zonse. Hakikat (Zenizeni) Publishing, mu Istanbul, imayesetsa kufalitsa Chisilamu.

Munthu amene ali ndi nzeru, kudziwa ndi chikumbumtima amamvetsa bwino pakati pa izi, ndi kuthandiza pofalitsa zabwino, kumabweretsa chipulumutso kwa anthu onse padziko lapansi lino ndi dziko ilo liri mkudza.

Pemphero la "**Subhanallahi wa bi-hamdihi subhanallahil adhim**," (lotchedwa 'kalimat tanzih') limachititsa kuti munthu akhululukidwe machimo ake ndi kumuteteza kuti asachimwenso ngati litanenedwa ka zana limodzi m'mawa ndi chiwerengero chomwecho madzulo. Pemphero ili latchulidwa m'makalata 307 ndi 308 a bukhu la **Maktubat** la waali wamkulu yemwenso ndi katswiri wamaphunziro al-Imam ar-Rabbani (quddisa sirruh).

Ya Rahman, ya Rahim ya Afuwwu, ya Kareem (kuwerenga Mayina a Allahu Taala awa kumamukumbutsa munthu Chisomo, Chifundo, kukonda kukhululukira, Kuwolowa manja kwa Allahu Taala).

**Hakikat Publishing**, yomwe ili ku Fatih, Istanbul, yadzipereka kuphunzitsa za chikhulupiriro chathu cha Chisilamu, kupangitsa kuti Chisilamu chiyamikiridwe. Allahu Taala asangalale ndi amene atithandiza! Amin.

Okondedwa awerengi, Assalam alykumu wa rahmatullah wa barakatuhu.

Zolemba zonse m'bukuli zamasuliridwa kuchokera m'mabuku olembedwa ndi akatswiri achisilamu. Palibe chawonjezeredwa ndi womasulira. Tagwira ntchito iyi ndi cholinga chotumikira anthu ndi kupeza chisamaliro cha omwe amateteza ufulu wa anthu. Mukawerenga zolembendwa ndi katswiri odziwika wamkulu izi ndi chidwi ndi kulingalira mwakuya, mudzapeza chidziwitso cha kuthupi ndi cha ku uzimu zomwe ziri zothandiza, insha-Allahu Taala (ngati Allahu Taala afuna). Tikupereka malonje ndi chikondi kwa inu. Allahu Taala akudalitseni ndi moyo wathanzi komanso akupatseni moyo wautali waphindu! Amin.

(Swalahat [Pemphero] lobwereza matamando ndi madalitso kwa Mtumiki Muhammad alaihi-salam): "Wa sallallahu ala Sayyidina Muhammadin wa ala Al-i- Muhammad wa barik ala Sayyidina Muhammadin wa ala Al-i- Muhammad. Allahumma Rabbana atina fid-dunya hasanatan wa fil-akhirati-hasanatan wa qina adhaban-nar bi-rahmatika ya Arhamar-Rahimin! Amin."

**Hakikat Publishing**

# MAU OYAMBA

***Tiyambe bukuli ndi Bismillah,***
***Pakuti dzina la Allah ndiwo mthunzi wopambana.***
***Zokoma zake ndi zosayezeka komanso zosawerengeka,***
***Iye ndi Mlengi wokonda kukhululuka, wachifundo chambiri.***

Allahu Taala ali ndi chifundo pa anthu onse a pa dziko lapansi powalengera zinthu zothandiza ndi kuzitumiza kwa aliyense ndi kuwawonetsa njira ya Chisangalalo Chosatha. Amamuongolera ku njira yoongoka yemwe Iye Wamufuna mwa anthu amene anasiya njira yoona ndi kutsata njira ya kufr (kusakhulupirira, kukana Choonadi cha Chisilamu); omwe anapatuka ponyengedwa ndi ma nafs awo (mphamvu yoyipa mwa munthu yomwe Ndi mdani wa Allahu Taala), potsatira magulu oipa, mabuku ndi zina zofalitsadwa zomwe zili zowononga ndi kuwapulumutsa ku chiwonongeko chamuyaya.

Allahu Taala sapereka madalitso amenewa kwa ankhanza ndi opyola malire, kumawasiya kukhala m'njira ya kufr, zomwe amakonda ndikulakalaka. M'dziko lakudzalo, Allahu Taala Adzakhululukira aliyense adzasankhidwa mwa okhulupirira olakwa amene anayenera kupita ku Jahannama, ndipo adzawalowetsa ku Paradiso. Allahu Taala yekha amalenga cha moyo chilichonse, amasunga cholengedwa chilichonse nthawi zonse ndi kuziteteza ku mantha ndi ku chiopsyezo. Mokhulupirira m'dzina lolemekezeka la Allahu Taala, ndi chiyembekezo cha thandizo lake, timayamba kulemba bukhu ili.

Kuyamika ndi Matamando zikhale kwa Allahu Taala! Mtendere ndi Madalitso apite kwa Mtumiki Wake wokondedwa Muhammad alaihi-salam, akubanja lake ndi kwa aliyense wa Maswahaaba ake olungama ndi odzipereka (Swahaba al-Kiram).

Liu loti **hamd** limatanthauza kukhulupilira ndi kunena kuti Allahu Taala amalenga ndipo ndi amene amatumiza zabwino zonse. Pomwe **shukr** imatanthauza kugwiritsa ntchito zabwino zonse mogwirizana ndi Chisilamu.

Mabuku zikwi ofunika kwambiri onena za chikhulupiriro cha Chisilamu alembedwa pamodzi ndi malamulo ake ndi zoletsedwa zake. Ambiri mwa iwo amasuliridwa mu zilankhulo zakunja ndi kugawidwa ku dziko lililonse. Kumbali inayi, ma zindiq (osakhulupirira onamizira kuti ndi Asilamu), anthu oyipa ndi oganiza moperewera omwe ndi mbuli m'chipembedzo, akhala akusokeretsedwa ndi akazitape aku Britain omwe akhala akuukira zofunikira

kwambiri komanso malamulo osavuta a chisilamu. Iwo ayesetsa kuwononga ndi kusintha komanso kunyenga Asilamu.

Koma ndi zoyamikika kwambiri kuti pafupifupi m'dziko lililonse, akatswiri a Chisilamu akuyesetsabe kufalitsa ndi kuteteza chikhulupiriro cha Chisilamu. Akatswiri a njira yowongokawa atamva uthenga kuchokera kwa ma Swahabah al-Kiram, analemba za Chisilamu m'mabuku omwe ndi a **Ahl as-Sunna**. Ngakhale izi ziri choncho, zolankhula komanso zolemba zosokoneza zikupezeka zomwe zimanenedwa kuti ndi zochokera mu **Quran al-Karim** ndi Hadith Sharif, koma ziri zomasulidwa molakwika ndi anthu amene sanawerenge kapena kumvetsa mabuku olembedwa ndi akatswiri a Ahl as-Sunna.

Koma zolankhula ndi zolemba zimenezi zakanika kusokoneza iman ya abale athu a chisilamu ndipo sizinawapatse chikaiko koma mmalo mwake zangoonetsera poyera umbulu wa anthu omwe akutumikira polankhula ndi kulemba izi.

Munthu amene akuzitcha kuti ndi Msilamu kapena wawonedwa akuswali mu Jammah, ayenera kuonedwa ngati Msilamu. Koma ngati pambuyo pake, m'kulankhula kwake, zolemba zake kapena makhalidwe ake zikusiyana ndi chidziwitso cha chikhulupiriro monga momwe adafotokozera akatswiri a Ahl as-Sunna, adzayenera kuuzidwa kuti kumeneko ndi kupatuka kapena ukafiri. Ndipo adzayenera kuuzidwa kuti aleke kuchita zolakwazo ndi kulapa. Ngati atakana kutero chifukwa cha kuganiza kwake koperewera ndi a nkhwizi, zidzadziwika kuti iye ndi opatuka kapena **murtadd** (munthu woukira chipembezo) kapena kuti ndi m'modzi mwa amene wazigulitsa kwa osakhulupirira a ku Britain. Ngakhale atapitiriza kuswali, kuchita Haji ndi kupembedza **(Ibada)** ndi ntchito zina zabwino,sadzapulumuka chiwonongeko pokhapokha atasiya kuchita zinthu za ukafiri ndi kulapa. Kupanda kutero iwo sadzakhala Asilamu. Pophunzira bwino zinthu zomwe zimayambitsa kusakhulupirira, Msilamu aliyense ayenera kudziteteza kuti asakhale opatuka m'chipembezo. Ayenera kuwazindikira anthu osakhulupirira ndi abodza amene amanamizira kuti ndi Asilamu, makamaka akazitape a ku Britain, ndi kupewa za haram zawo. Mtumiki "swallaallaahu 'alayhi wa aalihi wa sallam" adanena mu hadith sharif kuti matanthauzo olakwika ndi onama adzachotsedwa mu **Qur'an al-Karim** ndi **Hadith Sharif**, ndipo potero magulu 72 achinyengo adzawonekera. Hadith sharif iyi yalongosoledwa m'mabuku otchedwa **al-Bariqa** ndi **al-Hadiqa**, amene analembedwa ndi ulamuliro wa mabuku awiri olemekezeka a Hadith a **al-Bukhari** ndi **Muslim.**

Tisakhulupirire mabuku ndi ulaliki wa anthu omwe ali m'magulu ampatukowa, omwe amabwera m'mayina onga 'katswiri wamkulu wa

Chisilamu' kapena 'pulofesa wa chipembedzo'. Tikhale tcheru kuti tisagwere mmisampha ya mbava za chikhulupiriro, anthu ofuna kusocheretsa ena. Kupatula mbuli za Chisilamu, ma Kominisiti, ma freemason ndi amishonare achi khristu, palinso ma Wahhabi omwe anadzigulitsa kwa achiwembu aku Britain ndi a Yuda a Zion omwe akuyetsetsa kusocheretsa ana a Chisilamu m'njira zosiyanasiyana. Akuyetsetsa momwe angathere kuti awononge Iman ndi Chisilamu pofalitsa nkhani zabodza, kujambula mafilimu onama, kuchita zisudzo zonama pa wailesi ndi mawayilesi a kanema komanso pa ma webusayiti pa intaneti. Akugwiritsa ntchito ndalama za nkhaninkhani pa ntchito imeneyi. Akatswiri a Chisilamu (rahimahumu'llah) akhala akuyankha pa zabodzazi ndipo akhala akuwonetsa chipembedzo cha Allahu Taala, chomwe ndi njira ya chisangalalo ndi chipulumutso. Kuchokera mwa akatswiri enieni achisilamu amenewa, tasankha bukhu lotchedwa **Itiqad-nama** lolemba Maulana Diya ad-Din Khalid al-Baghdadi al-Uthmani (quddisa sirruh), yemwe anali katswiri wa Chisilamu wolemekezeka. **Itiqad-nama** poyamba linamasulidwa m'Chituruku ndi malemu wolemekezeka Haji Faizullah waku Kemah, Erzincan, ndi mutu woti **Faraid al-fawaid** ndipo linasindikizidwa ku Egypt mchaka cha Hijri 1312. Kumasulira kuno kwachitika mofewetsa ndi mutu wakuti **Chikhulupiriro ndi Chisilamu**. Kusindikiza koyamba kuchitika mchaka cha 2022. Pofuna kusiyanitsa pakati pa mau a bukhuli ndi ndemanga, ndemanga zathu zakutilidwa m'mabulaketi a mtundu uwu. Tikuthokoza kosalekeza kwa Allahu Taala chifukwa chotifewetsera ntchito yosindikiza bukhuli. Bukhu loyamba la **Itiqad-nama** liri mu chi Persia ku nyumba yowerengera ma bukhu ya University ya Istanbul (Ibnul Emin Mahmud Kemal Dept. F. 2639).

Kumapeto kwa nkhani ya (Ukwati wa Osakhulupirira) m'bukhu la **Durr al-mukhtar** lolembedwa ndi Alauddin Haskefi "rahimahullahu taala" zalembedwa motere: "Ngati mtsikana wa Chisilamu apanga nikkah[1] asakudziwa Chisilamu pamene iye watha msinkhu, nikah yake imakhala yosavomerezeka pa malamulo ndipo iye amakhala wopatuka mchipembezo. Ayenera kuphunzitsidwa zizindikiro za Allahu Taala, ndipo ayenera kubwereza ponena kuti, (Izi ndimakhulupirira)." Pofotokoza izi, Ibn Abidin "rahimahullahu taala" anati: "Ngati mtsikanayo ali wosatha msimkhu, ndiye kuti ali m'chikhulupiriro cha makolo ake; iye ndi Msilamu. Akafika pakutha msinkhu, iye salinso wa chikhulupiriro cha makolo ake. Moti akatha msinkhu asakudziwa za Chisilamu, amakhala wopatuka. Pokhapokha ataphunzira ndi kukhulupirira nsichi zisanu ndi imodzi za iman ndi kukhulupirira kuti ndi kofunikira kukhala motsatira malamulo a Chisilamu. Ngakale atanena **kalimat at-tawhid**, yomwe ndi **(La**

[1] Nikkah -pangano la ukwati molingana ndi malamula a chisilamu

**ilaha illaallah, Muhammadun Rasulullah),**[1] sangakhale msilamu ngati saphunzira ndi kukhulupirira msichi zisanu ndi imodzi za iman. Ndi koyenera kwa iye kuphunzira ndi kukhulupirira msichi zisanu ndi imodzizi zomwe ndi "Amantu bi'llahi ...," ndipo ayenera kunena kuti, 'Ndikuvomereza malamulo a Alla taala ndi zomwe analetsedwa Iye." Kulongosola uku kwa Ibn Abidin kukusonyeza kuti kafiri amakhala Msilamu akangonena kalimat at-tawhid ndi kukhulupirira tanthauzo lake. Koma, monga Msilamu wina aliyense, mosazengereza ayenera kuloweza pa mtima nsichi za (**Amantu)** (Izi ndi nsichi zisanu ndi imodzi, zomwe ndi mfundo za iman, zalongosoledwa m'mutu wakuti "Zofunika (Nsichi) za Iman'', tsamba 26). Izi zili mchiganizo chotsatirachi, phunzirani bwino lomwe tanthauzo lake ndi zomwe zikhuphunzitsa za Chisilamu: **"Aamantu billah wa Malaykatihi wa Kutubihi wa Rusulihi wal Yawmil aakhir wabil Qadari khayrihi wa sharrihi min-Allah ta'alawal ba'athu ba'adal mawt haqqun. Ash-hadu an laa ilaaha illallahu wa ash-hadu anna Muhammadan Abduhu wa rasooluhu."** Komanso, ngati mwana wa chisilamu saphunzira nsichi zisanu ndi imodzizi ndi ziphunzitso za Chisilamu ndipo sakunena kuti amazikhulupirira, iye amakhala wopatuka akakwana zaka za kutha msinkhu. Akaphunzira ndi kukhulupirira ndikukhala ndi Iman, ndikokakamizidwa kwa kufufuza ndi kuphunzira **ziphunzitso za Chisilamu** zomwe ndi malamulo (**ma fardhi**) ndi zoletsedwa (**ma haramu**); momwe angayeretsere (**Udhu** ndi **ghusl**) ndi pemphero la mwambo (**Swalah**), ndi momwe angaziphimbire ziwalo zake za thupi (za maliseche). Munthu ukafunsidwa za ziphunzitso izi, ndi fardh kwa iye kuziphunzitsa kapena kulangiza bukhu lowona la chisilamu loti munthu wofunsayo awerenge. Ngati palibe munthu womufunsa kapena palibe bukhu loona, ndi fardh kwa iwe mwini kufufuza choonadi. Munthu amasanduka wosakhulupirira ngati sakusaka maphunzirowo. Kungokhala osafunafuna sikungakhale chifukwa chokwanira chosadziwira ziphunzitsozi. Msilamu yemwe sapanga zinthu zokakamiza **(fardh)** mu nthawi yake kapena yemwe akupanga zinthu za haram adzazunzidwa ku moto wa Jahannam. Ntchito iyi ili ndi mfundo zakuya za msichi zisanu ndi imodzi za iman. Msilamu aliyense awerenge bukhuli bwino ndipo ayesetse kuti ana awo ndi ena onse odziwana nawo aliwerenge.

M'bukhuli matanthauzo a ma ayah aperekedwa ngati **maal** (Matanthauzo ngati momwe ananenera akatswiri a **tafsir**; sayansi ya kafotokozedwe ka **Quran al-Karim**). Matanthauzo a ma ayah ankawamvesa ndi Mtumiki "swallaallaahu 'alayhi wa aalihi wa sallam" yemwe anaphunzitsa matanthauzowo kwa

[1] Kutanthauza kuti: Allahu taala alipo ndipo ndi Mmodzi. Muhammad alaihi salam ndi Mtumiki wotumidwa ndi Allahu Taala Ilah.

Swahaba wakekudzera mu ma Hadith. Akatswiri awa a tafsir anasiyanitsa ma Hadith awa pochotsa abodza opekadwa ndi anthu omwe amazitche a chipembedzo koma opanda madhhab, ma munafiq ndi zindiq, omwe anazigulitsa kwa ma British osakhulupirira. Pamene samapeza Hadith iliyonse yotanthauzira ayah, iwo amapereka tanthauzo la ayah powagwiritsa ntchito (m'maonekedwe) sayansi ya tafsir. Zomwe amamva anthu omwe amalankhula Charabu koma osaphunzira sayansi ya Chisilamu ndipo opanda tafsir sizingatchedwa tafsir ya **Quran al-Karim**. Kunena zoona, Hadith sharif imati: "**Munthu wotanthauzira Qur'an al-Karim malinga ndi kumvetsetsa kwake amakhala wosakhulupirira**.''

Kalozera wa mawu achi Arabu ndi mawu ena omwe si a Chichewa wawonjezeredwa kumapeto kwa bukhuli pofuna kuthandiza awerengi pa mau omwe sakudziwa matanthauzo ake.

Tipemphe Allahu Taala kuti atisunge tonse m'njira yoongoka yomwe aonetsa akatswiri a **Ahl as-Sunna**! Atiteteze kuti tisakhulupirire za chinyengo, za mabodza za mbulu za Chisilamu ndi anthu osatsatira madhhab ndi ma **munafiku** omwe akugwiritsa ntchito mau oti 'akatswiri kwambiri a Chisilamu' monama!

Mabuku onse osindikizidwa ndi **Hakikat Publications** akufalitsidwa pa dziko lonse la pansi m'zilankhulo zosiyanasiyana kudzera pa intaneti komanso pogawa mabukuwo.

Makono, Asilamu pa dziko lonse lapansi agawika m'magulu atatu. Gulu loyamba ndi la Asilamu enieni amene akhala akutsatira mapazi a ma Swahaba. Iwo amatchedwa **Ahl as-Sunna** kapena **Asilamu a Sunni** kapena **Firqat an-najiyya**, kutanthauza kuti gulu la omwe adzatetezedwe ku moto wa Jahannama. Gulu lachiwiri ndi la adani a ma Swahaba, ndipo amatchedwa **Shias** (ma Shia) kapena **Firqat ad-dhalla** (gulu lopatuka). Gulu lachitatu ndi lodana ndi onse ma Sunni ngakhalenso ma Shias. Iwo amatchedwa ma **Wahabi** kapena ma **Najdi**, chifukwa anawonekera koyamba mtawuni ya Najd ku Arabia. Amatchedwanso **Firqat al-maluuna** (gulu lotembereredwa), chifukwa, monga zalembedwa m'mabuku athu a **Endless Bliss** ndi **The Rising and the Hereafter**, iwo amawatcha Asilamu kuti ndi anthu 'osakhulupirira', ndipo Mneneri wathu anatemberera aliyense yemwe amawatchula Asilamu kuti ndi anthu osakhulupirira. Kugawikana kwa Asilamu m'magulu atatuku kunadza chifukwa cha Ayuda ndi ma British.

Nthawi zonse Msilamu aliyense azinena kuti, “**La ilaha illaallah**” poyeretsa (tazkiya) ma nafs[1] ake. Uku ndikudziyeretsa ku machimo ndi umbuli, umene uli mu chibadwa cha munthu. Nthawi zonse azibwereza mau oti **“Astaghfirullah**” pofuna tasfiya (kutsuka) mitima yawo. Potero adzadzipulumutsa ku uchimo ndi kusakhulupirira, zomwe zimachokera ku ma nafs awo, kwa Shaitwani, abwenzi oipa ndi mabuku oipa. Mapemphero a munthu yemwe amamvera Chisilamu ndi kulapa amavomerezeka ndi Allahu Taala. Ngati munthu saswali, amayang’anitsitsa akazi osavala mozilemekeza ndi omwe amawonetsa ziwalo zofunika kuphimbidwa komanso munthu yemwe amadya ndi kumwa zomwe zili za haramu, adzakhala otsimikizika kuti iwo samvera Chisilamu. Mapemphero awo sadzavomerezeka.

| **Gregorian** | **Hijri Solar** | **Hijri Lunar** |
|---|---|---|
| 2023 | 1402 | 1444 |

[1] Mphamvu yoyipa mwa munthu yomwe ndi mdani wa Allahu Taala.

## -1-

# CHIYAMBI

[Pofuna kuyamba kwabwino ndi kodalitsika, Maulana Khalid al-Baghdadi (quddisa sirruh) anayamba bukhu lawo potengera zolembedwa za mu kalata ya 17 m'buku la chitatu la **Maktubat** lolembedwa ndi al-Imam ar-Rabbani Ahmad al-Faruqi as-Sirhindi "rahmatullahi alaih" omwe anamwalira mchaka cha 1624/1034). Iwo analemba kuti:

Ndikuyamba kalata yanga ndi Bismillah. Ulemerero wopanda malire ndi kuyamikidwa konse kukhale kwa Allahu taala yemwe watikondera ife pa zonse ndi kutilemekeza potipanga kukhala Asilamu. Yemwe watilemekeza potipanga kukhala Umma wa Muhammad "swallaallaahu 'alayhi wa aalihi wa sallam", lomwe ndi dalitso la pamwamba kwambiri.

Tiyenera kusinkhasinkha ndi kuzindikira kuti Allahu Taala yekha ndi amene amatumiza chisomo chili chonse pa aliyense. Iye yekha ndi amene amalenga chili chonse. Iye yekha ndi Yemwe amasunga chili chonse pa nthawi iliyonse. Kupambana ndi makhalidwe abwino a anthu onse ndi madalitso ndi chisomo Chake. Moyo wathu, kuganiza, kuzindikira, mphamvu, kuona, kumva ndi zolankhula zathu, zonse zimachokera kwa Iye. Iye ndi Yemwe amatumiza madalitso ndi chisomo chosawerengeka nthawi zonse. Iye ndi amene amapulumutsa anthu ku mavuto ndi ku masautso. Amene amavomereza mapemphero, ndikuchotsa zodandaulitsa ndi ngozi za zidzidzi. Ndi Iye yekha amalenga zopatsa thanzi ndi kuzifikitsa kwa ife. Madalitso a Allahu Taala ndi wochuluka kwambiri kotero kuti sasiya kupereka zopatsa moyo kwa anthu ochimwa. Kuthekera Kwake pophimba machimo ndi kwa kukulu kwambiri kotero kuti Sayalutsa, kunyozetsa kapena kuonetsera pa mtunda ophwanya malamulo kapena opewa zoletsedwa. Ngati mwini kukhululuka, mwini chifundo chochuluka, Iye safulumira kulanga amene akuyenera chilango ndi mazunzo (adhab). Allahu Taala amapereka madalitso ndi mtendere kwa wina aliyense, okondedwa ndi adani omwe, palibe amene amamanidwa. Chisomo cha pa mwamba ndi cha mtengo wapatali kwambiri chochokera kwa Allahu taala ndicho chotisonyeza ife njira yolondola yopita ku chisangalalo ndi chipulumutso; ndikutilimbikitsa kuti tisasochere koma kuti tikalowe ku Mparadiso. Allahu Taala Watilamula kuti tidzisinthe ndi kukhala okonda Mtumiki "swallaallaahu 'alayhi wa aalihi wa sallam" kuti mwina tingapeze madalitso a muyaya ndi chisangalalo chosatha komanso chosaguga ku mParadiso ndikupeze chisomo ndi chikondi Chake. Choncho, madalitso Ake

ngoonekera monga dzuwa. Zabwino zirizonse zomwe zimachokera kwa anthu ena, ndithudi, zimachokera kwa Allahu Taala Komanso ndi Allahu Taala Yemwe amapanga ena kukhala amkhalapakati powapatsa chikhumbokhumbo, mphamvu ndi nyonga zochita zinthu zabwino. Ndi Allahu Taala Yemwe amatumiza madalitso ku malo ndi anthu alionse. Kuyembekezera zabwino kuchokera kwa wina aliyense osakhala Allahu Taala kuli ngati kupempha kanthu kwa olondera kapena kupempha za chifundo kuchokera kwa munthu wosauka. Osaphunzira kapena ophunzira, ouma mitu ndi anzeru ndi ena onse omwe ali ndi chidwi adzadziwa kuti zomwe tikunena pano ndi zoona zenizeni poti zomwe tikunena ndi za chiziwikire, sizikufunika kuziganiziranso.

Ndi udindo wa munthu aliyense kuyamika Allahu taala, momwe angathere. Kuthokoza Allahu taala, Yemwe watikondera ndi zabwino izi. Iyi ndi ngongole komanso ntchito yomwe mnzeru zimatilamula kuchita. Koma si chapafupi kupereka chiyamikochi kwa Iye mokwanira chifukwa munthu, yemwe analengedwa kuchokera popanda kanthu, ali wofooka, osowa, olakwa komanso wosalongosoka. Allahu Taala ndi wanthawi zonse ndipo ndi wamuyaya, wopanda kusalongosoka kulikonse. Ulemerero uliwonse ndi wake. Munthu sangafanane kapena kuyandikirana ndi Iye pa china chilichonse. Palibe chomwe munthu angafanane kapena kuyandikira kwa Iye. Kodi munthu yemwe ali otsika kwambiri angakwanitse kuthokoza Allahu Taala wolemekezeka m'njira yoyenera ndi Ulemu Wake? Pali zinthu zambiri zomwe anthu amaziona ngati zokongola ndi za mtengo wapatali, koma Allahu Taala amadziwa kuti zinthhuzo ndi zoipa, ndipo sakondwera nazo. Zinthu zomwe timazisilira kapena kuyamikira zitha kukhala zawamba zopanda pache. Pa chifukwa ichi, anthu, ndi kuperewera m'maganizo kwawo komanso ndi kupanda maso mphenya kwawo, sangathe kuzindikira zinthu zomwe zimathokoza ndi kulemekeza Allahu Taala. Ngati Allahu Taala satiwonetsa njira zomupembedzera, machitidwe athu omwe ali owoneka ngati kupembedza angakhale opanda pache.

Choncho, mlingo wa mayamikidwe ndi ntchito zoyenera kuchitidwa ndi chikhulupiriro cha munthu kwa Allahu Taala mu mtima, poyankhula ndi lilime komanso kupanga ndi thupi zinatanthauzidwa ndi Allahu Taala ndi kufika kwa munthu kudzera mwa Mtumiki Wake "swallaallaahu 'alayhi wa aalihi wa sallam"! Ntchito za munthu zomwe Allahu Taala anazionetsa ndi kulamulira zimatchedwa **Chisilamu.** Munthu amayamika Allahu Taala potsatira njira zome Mtumiki wake "swallaallaahu 'alayhi wa aalihi wa sallam" anaphunzitsa. Allahu Taala salandira kapena kukondwa ndi kulambira komwe kuli kosemphana ndi chiphunzitso cha Mtumiki kapena chosiyana ndi njira ya Mtumiki, chifukwa pali

zinthu zambiri zimene anthu amaona ngati zabwino kapena zokongola koma zomwe Chisilamu chimaletsa ndikuziwona zoyipa.

Choncho, poyamika Allahu Taala, anthu anzeru ayenera kutsata zomwe amapanga ndi kulamula Hazrat Muhammad alaihi-salam. Njira yake imatchedwa **Chisilamu**. Munthu wotsatira Muhammad alaihi-salam amatchedwa **Msilamu**.

Kuyamika Allahu Taala potsatira Muhammad alaihi-salam, kumatchedwa **ibadat** (kupembedza). Ziphunzitso za Chisilamu zili mbali ziwiri: za chipembedzo Ziphunzitso Zachipembedzo zili m'magawo awiri:ndi za sayansi[1].

1 - Ziphunzitso zomwe munthu ayenera kukhulupirira mu mtima, zotchedwa **usul ad-din** kapena ziphunzitso za **Iman**. Mwachidule, **iman** imatanthauza kukhulupirira msichi zisanu ndi imodzi zomwe anaphunzitsa Muhammad alaihi-salam, kuvomereza Chisilamu ndi kupewa kunena ndi kugwiritsa ntchito zisonyezo za ukafiri (kufr). Msilamu aliyense ayenera kuphunzira zizindikiro za ukafiri ndi kuzipe wa kuzigwiritsa ntchito. Munthu amene ali ndi iman amatchedwa **Msilamu.**

2 - Ziphunzitso za miyambo zomwe ziyenera kuchitidwa, ndi zinthu zimene siziyenera kuchitidwa ku thupi ndi mu mtima. Ziphunzitso zomwe ziyenera kuchitidwa zimatchedwa **fardh**, ndi zinthu zomwe zalamulidwa kuti zipewedwe zimatchedwa **haram**. Ziphunzitso izi zimatchedwa **furu ad-din** kapena **al-ahkam al-Islamiyya** kapena **Ziphunzitso za Chisilamu**.

[Chofunika choyamba kuti munthu aliyense achite ndi kunena **kalimat at-tawhid** ndi kukhulupirira tanthauzo lake. Kalimat at-tawhid ndi: "**La ilaha illaallah, Muhammadun Rasulullah,**" ndipo imatanthauza kuti: "Palibe opembezedwa mu choonadi koma Allahu Taala ndipo Muhammad alaihi-salam ndi Mtumiki Wake." Kukhulupirira mfundo imeneyi kumatanthauza "kukhala ndi iman," ndi "kukhala Msilamu." Munthu amene ali ndi iman amatchedwa (**Mumin** (Wokhulupirira)) komanso **(Msilamu).** Iman iyenera kukhala yokhazikika. Choncho ndikofunikira kupewa kuchita zinthu zomwe zimayambitsa kusakhulupirira kapena kugwiritsa ntchito zinthu zosonyeza kusakhulupirira.

**Quran al-Karim** ndi **Kalam al-Ilahi** (mawu opatulika, mawu a Allahu taala). Allahu Taala anatumiza Quran al-Karim kwa Muhammad alaihi-salam kudzera mwa mngelo wotchedwa Jubrail (Gabriel, alaihi-salam). **Quran al-Karim** ili

[1] Anthu omwe amazitcha Okonzanso zipembedzo amanena kuti ziphunzitso za chipembedzo zimatchedwa 'ziphunzitso za maphunziro ndipo ziphunzitso za sayansi zimatchedwa 'ziphunzitso zomveka'.

m’Chiyankhulo cha Chiarabu, ndipo mau ake anatsika m'ma ayah (mavesi) zilembo ndi mau osanjidwa bwino ndi Allahu taala. Manthauzo a zilembo ndi mau amenewa amapereka **Kalam al-Ilahi.** Zilembo ndi mawu awa amatchedwa **Quran al-Karim**. Matanthauzo omwe akuvumbulutsidwa mu **Kalam al-Ilahi** ndi **Quran al-Karim**nso. Qur'an al-Karim iyi yomwe ili **Kalam al-Ilahi** si chinthu cholengedwa choti chili ndi matero. Ndi yamuyaya monga zizindikiro zina za Allahu Taala. Kamodzi pachaka Jebrail alaihi-salam amatsika kudzawerenga gawo la **Quran al-Karim** yomwe idavumbulutsidwa kale potsatira momwe inalembedwara m’Buku la **Lawh almahfudh** (bukhu momwe mwalembedwa zinthu zonse ku m’Paradiso) ndipo Mtumiki wathu ankabwereza pambuto pa mngeloyo. M’chaka chimene Mtumiki anamwalira, Jebrail alaihi-salam anamuyendera kawiri ndi kuwerenga naye Quran al-Karim yonse. Mtumiki wathu alaihi-salam ndi ambiri mwa ma Swahaba anali ataloweza Quran al-Karim yonse. Mtumiki alaihi-salam, Abu Bakr as-Siddiq yemwe anali Khalifa (mtsogoleri wa ma Swahaba Mtumiki atamwalira), anasonkhanitsa onse omwe analoweza **Quran al-Karim** pamodzi. Anasonkhanitsanso magawo a Quran omwe anali atalembedwa kale, ndi kupanga komiti yomwe inalemba **Quran al-Karim** yonse. Kotero bukhu lotchedwa **mus’haf** linalembedwa ndikutululutsidwa. Ma Sahaba zikwi makumi atatu ndi zitatu (33,000) anagwirizana kuti chilembo chilichonse cha mu bukhu la mus’haf ili chinali m’malo ake olondola.

Zoyankhula za Muhammad alaihi-salam zimatchedwa **Hadith sharif**. Zoyankhula zokhala ndi matanthauzo a Allahu Taala koma zokhala ndi mawu mwa Muhammad alaihi-salam zimatchedwa **Hadith qudsi**. Pali mabuku ambiri a Hadith koma **Al-Bukhari** ndi **Muslim** ndi amene ali odziwika kwambiri. Pa malamulo a Allahu Taala ziphunzitso zomwe ziyenera kukhulupiridwa zimatchedwa **iman**, zomwe ziyenera kuchitidwa zimatchedwa **fardh,** ndipo zoletsa zimatchedwa **haram**. Fardh ndi Haramu limopdzi zimatchedwa **ahkam al-Islamiyya.** Munthu amene amakanira ngakhale mu chikhulupiriro chimodzi mwa ziphunzitso za Chisilamu amatchedwa **kafir** (wosakhulupirira, wokanira choonadi cha Chisilamu).

Chinthu chachiwiri chofunikira kuti munthu achite ndikuyeretsa mtima. Mawu oti ‘mtima’ ali ndi matanthauzo awiri. Chiwalo cha mkati mwathu pa chifuwa chimatchedwa ‘mtima’ pafupifupi ndi munthu wina liyaense. Nyama nazo zili ndi mitima. ‘Mtima’ wachiwiri ndi mtima wosaoneka umene umakhala mu mtima wa kuthupi. Mtima wachiwiri uwu umatchedwa ‘mtima’ wauzimu. Ndi mtima uwu womwe walembedwa m'mabuku achipembedzo. Mtima uwu ndiye ndi malo a ziphunzitso za chisilamu. Komanso ndi mtima uwu womwe umakhulupirira kapena kusakhulupirira. Mtima wokhulupirira ndi woyera, mtima wosakhulupirira ndi wauve ndipo ndi ‘wakufa’. Ndi ntchito yathu

yoyamba kuyesetsa kwambiri kuyeretsa mtima wathu. Kupembedza, makamaka kuswali ndi kunena pemphero lililonse lotchedwa **istighfar**, poti izi zimayeretsa mtima. Kuchita za haraamu kumadetsa mtima. Mtumiki wathu anati: "**Nenani istighfar pafupipafupi! Ngati munthu anena istighfar mosalekeza, Allahu Taala amamuteteza munthuyo ku matenda ndi matsoka kapena ku ngozi zili zonse. Munthuyo amalandira chakudya kuchokera kumalo omwe sayembekezera n'komwe.**" Istighfar ikutanthauza kunena kuti, "**Astaghfirullah**" (Allahu taala Andikhululukire!). Kuti pempheroli livomerezedwe, wopemphayo ayenera kukhala Muslim, alape machimo ake ndipo apemphe akuidziwa tanthauza la pempheloli ndi kulikhulupirira. Mapemphero onenedwa ndi mtima wakuda salandiridwa. Komanso, ngati munthu anena kuti "**Astaghfirullah**" katatu kumapeto kwa Swala iliyonse ya Swala zisanu za pa tsiku, mtima wake udzayera ndipo mtimawo pawokha udzayamba kunena pempheroli. Pemphero longonena ndi lilime lokha, popanda kutsimikiza mu mtima ndi lopanda phindu.

Ziphunzitso za chipembedzo cha Chisilamu ndi zomwe zolembedwa m'mabuku a akatswiri a Ahl as-Sunna. Munthu amakhala osakhulupirira (kafiri) ngati sadakhulupirire zina mwa ziphunzitso za Iman (zikhulupiriro) ndi miyambo ya Chisilamu yophunzitsidwa ndi Akatswiri a Ahl as-Sunna, mu nass iliyonse (ma ayah a Qur'an ndi hadith sharif) ndi matanthauzo omveka. Munthu amene amabisa kusakhulupirira kwake amatchedwa **munafiq.** Koma munthu yemwe amabisa kusakhulupirira kwake ndikumanama kuti iye ndi Msilamu pofuna kunyenga Asilamu, iye amatchedwa **zindiq**. Chifukwa chokhulupirira ma ayah ndi mtima wonse, munthu ameneyo sadzakhala ku mazunzo a ku Gahanama kwa muyaya, koma adzapulumutsidwa ndipo adzalowetsedwa ku m'Paradaiso. Anthu amtundu uwu amatchedwa **ahl albida** (ampatuko) kapena magulu **dalala** (okumva za mmaluwa). Magulu amenewa alipo 72. Ndipo mapemphero, ubwino wawo ndi ntchito zao za chifundo sizidzalandiridwa ndipo sizidzawapindulira mu moyo omwe uli nkudza. Asilamu omwe ali ndi chikhulupiriro cholondola amatchedwa **Ahl as-Sunnat wa 'l-jamaa** kapena ma **Sunni**. Asilamu amatsata ma madhhab anayi pochita ntchito zawo zopembedza. Otsatira madhhab amodzi mwa madhhab anayiwa akudziwa kuti otsatira Madhhab ena atatuwo nawonso ndi a **Ahl as-Sunna**, ndipo amakondana wina ndi mzake. Munthu amene satsatira ena aliwonse mwa madhhab anayiwa si Msilamu wa Sunni. Munthu amene si **Ahl as-Sunna** ndiye kuti ndi kafir (wosakhulupirira) kapena wotsutsa (wa bid'at)[1]

[1] Izi zalembedwa m'makalata (Maktubat) a al-Imam ar-Rabbani "rahmatullahi alaih" makamaka m'kalata ya 286 ya bukhu loyamba,mu ndemanga ya at-Tahtawi ya bukhu la

Ngati munthu wopembedza motsata amodzi mwa madhhab anayi amenewa wachimwa kapena walakwitsa chilichonse m'kupembedza kwakeko ndipo walapa, iye adzakhululukidwa. Ngati salapa, Allahu Taala akhoza (ngati atafuna) kumukhululukira ndi kusamuika ku Gahena. Ngati Allahu Taala afuna, adzamuzunza munthu ameneyo molingana ndi utchimo wake koma kenako adzamasulidwa ku mazunzo. Yemwe sakhulupirira ngakhale chimodzi mwa ziphunzitso zofunika kuzikhulupirira m'Chisilamu, zomwe ndi zodziwika ngakhala kwa osaphnzira, adzaponyedwa ku ng'anjo ya moto kwa muyaya. Munthu ameneyu amatchedwa "**kafir**" (wosakhulupirira) kapena "**murtadd**" (wapatuka).

Pali mitundu iwiri ya ma kafiri: Ma kafiri omwe ali ndi bukhu lovumbulutsidwa la kumwamba, ndi amene alibe bukhu lakumwamba. Ngati munthu yemwe makolo ake ali achisilamu akusiya Chisilamu ndikukhala kafir, iye amatchedwa "murtadd". Ibn Abidin "rahimahullahu taala" analemba motere pa mutu wa 'amene ukwati wawo uli woletsedwa chifukwa cha shirk (komwe kuli kuphatikiza Allahu Taala ndi zinthu zina popembedza): "Murtadds, mulhids[1], ma zindiq, anthu opembedza moto, opembedza mafano, Agiriki akale ophunzira kwambiri, ma munafiq, otsatira magulu makumi asanu ndi awiri aja (72) omwe mamveramvera awo anawapatulitsa ku chikhulupiriro choonadi, (ma Brahma, ma Budda), ma Batina, ma Ibahata ndi ma drusa, onsewa ndi anthu sakhulupirira omwe alibe mabuku akumwamba." Ma Kominisiti ndi ma freemason, nawonso ndi osakhulupirira omwe alibe mabuku akumwamba. Ayuda ndi Akhrisitu ndi anthu osakhulupirara omwe ali ndi mabuku ovumbulutsidwa kuchokera kumwamba. Iwo ali ndi ma buku a **Taurat** ndi **Baibulo.** Anthu omwe ali ndi ma buku koma ndi kumapembedza zolengedwa zina amakhala ma **mushrik** (ophatikiza Allahu taala ndi zinthu zina). Zizindikira za Allahu taala za **Sifat ath-Thubutiyya** ndi **Sifat adh-Dhatiyya** zimatchedwa zizindikiro za **Uluhiyya** (Umulungu).

Ngati kafiri wokhala ndi bukhu kapena wopanda akulowa Chisilamu, munthu ameneyo adzazemba Gahena. Munthu ameneyo amakhala Msilamu woyera

---

Durrulmukhtar pa mutu wotchedwa Zabayikh komanso mu bukhu la al-Basair li-munkiri ttawassuli bi ahli l-maqabir, ndi makalata ake. Mabuku awiri omalizirawa ali mchilankhula cha Charabu. Lomaliziralo linalembedwa ndi kusindikizidwa ku India ndipo lasindikizidwa ndi a Hakikat Publications ku Istanbul pa makina amakono kuyambira mchaka cha 1975/1395.

[1] Mulhid kapena ma zindiq amazitcha kuti iwo ndi Asilamu. Mulhids ndi owona mtima ndi m'mawu awo; amakhulupirira kuti iwo ndi Asilamu ndipo ali pa njira yoongoka. Pomwe ma zindiq ndi adani a Chisilamu, omwe amadzipangitsa kuwoneka ngati Asilamu ndi cholinga choononga Chisilamu ali mkati mwa Asilamu powanyenga Asilamuwo.

wopanda tchimo. Koma munthu ameneyo ayenera kukhala Msilamu wa Sunni. Kukhala Msilamu wa **Sunni** kumatanthauza kuwerenga ndi phunzirani Buku lolembedwa ndi m'modzi mwa akatswiri a Ahl as-Sunna ndi kutsatira iman, zochita ndi mawu amene munthuyo waphunzira kuchokera m'bukulo. M'dziko la pansi pano, mau a munthu ndi zochita zake zomwe amachita mupanda kukukamizidwa ndi zomwe zimasonyeza ngati munthuyo ali Msilamu kapena ayi. Zimakhala zotsimikizika pomwe akumwalira ngati wapita kudziko linalo ndi Iman. Ngati Msilamu yemwe ali ndi machimo akulu alapa ndi mtima woyera, machimo ake ndithu adzakhululukidwa ndipo adzakhala woyera ndi wopanda tchimo. Zalongosoledwa mwatsatanetsatane m'mabuku a **ilm al-hal** kuti **tawba** (kulapa) ndi chani ndi momwe munthu angalapire.

## -2-

# IMAN NDI CHISILAMU

M'bukhu la **Itiqad-nama**, hadith sharif ifotokozedwa za momwe Mtumiki "sallallahu alaihi wa sallam" ananenera za **iman** ndi **Islam**. Ndili ndi chikhulupirira kuti kudzera mu mdalitso wa hadith sharif imeneyi, chikhulupiriro cha Asilamu chirimbikitsidwa pakutero adzapeza chipulumutso ndi mtendere. Ndikukhulupiriranso kuti zidzapangitsa kuti ine, Khalid [quddisa sirruh], amene ndili ndi machimo ochuluka ndipulumutsidwe. Ndikupempha Allahu taala, amene ine ndikukhulupirira kuti sasowa chilichonse, ndipo zabwino Zake ndi madalitso Ake ndi ochuluka, amene amamvera chisoni zolengedwa ngati ife anthu, akhululukire Khalid wosaukayu; amene ntchito zake ziri zochepa kwambiri ndipo yemwe mtima wake uli wakuda kwambiri chifukwa cha mawu ake osayenera. Allahu taala avomere pempho lake pa zolakwa zake. Allahu Taala atiteteze ife ku zoipa za achinyengo, ku bodza la Satana [kuti tisanyengeke ndi mau a bodza ndi olakwika komanso ndi zolembedwa ndi adani a Chisilamu]. Atipange ife kukhala osangalala! Iye ndi mwini chifundo chambiri ndi mwini kupereka zambiri.

Monga zananenedwera ndi akatswiri achipembezo cha Chisilamu, msilamu aliyense, mkazi kapena mamuna, yemwe wafika podziimira pa yekha (**mukallaf)**, kapena kutha msinku, akuyenera kumudziwa Allahu Taala. Ayenera

kudziwa ndi kukhulupirira as-Sifat adh-hatiyya[1] ndi as-Sifat ath-Thubutiyya[2] zomwe ndi zizindikiro za Allahu Taala molondola. Ichi ndi chinthu chokakamizidwa (fardh) kwa wina aliyense. Kusadziwa si chifukwa chozitetezera ku tchimo. Ine , Khalid ibn Ahmad al-Baghdadi ndalemba bukhuli, osati chifukwa chofuna kuonetsa kuzindikira kapena kukhala wa pa mwamba kapena kufuna kutchuka ayi, koma kufuna kukumbutsa ndi kusiya ntchito ya bwino. Allahu Taala athandize Khalid ndi asilamu onse kukhala wodzichepetsa ndi mphamvu zake, komanso kudzera mu mzimu wa Mtumiki wodalitsika alaihi salama, Ameen.

China chilichonse kupatula Allahu Taala chimatchedwa kuti **ma-siwa** kapena **alam**. Koma makono anthu molakwitsa amazitcha '**chilengedwe'.** Zolengedwa zonse kunalibe. Allahu Taala ndi amene analenga zonse. Zonse ndi **mumkin** (zomwe zingakhalapo kuchokera popanda kanthu ndipo zitha kuskhalapo zitakhalapo) ndi ma **hadith** (zomwe zinakhalapo popanda kukhalapo kaye). Hadith Sharif, yoti "**Allahu Taala analipo kale, ndipo china chilichonse panalibe",** ikuphereza mau pa nkhaniyi.

Umboni wina woti zolendedwa ndi hadith ndi mfundo yoti zimasanduka ndi zikusintha m'maonekedwe malinga ndi kudutsa kwa nthawi. Chilichonse chikusintha[3]. Koma chinthu chomwe chiri qadim (chopanda chiyambi)

---

[1] Zizindikiro zisanu ndi chi chimodzi (6) zomwe ziri zokhazikika pa dhat wa Allahu taala (umwini wake) zimatchedwa **as-Sifat adh-Dhatiyya.** Izi ndi **al- Wujud** (Allahu Taala kukhalapo mwa Iye mwini); **al-Qidam** (kukhala wopanda chiyambi ndi Umuyaya m'mbuyomu); **al-Baqa** (kusakhala ndi mapeto ndi kukhala wa muyaya) **al-Wahdaniyya** (kupanda mnzake kapena wofanana Naye mu ulemu wake); **al-Mukhalafatun li-l-hawadith,** (kusiyana ndi cholengedwa zonse mu zonse; ndi **al-Qiyamu bi nafsihi** (kukhalapo kwa Allahu Taala, kukhala wosasowa kalikonse mpaka muyaya. Palibe cholengedwa chomwe chili ndi zizindikiro zisanu ndi chimodzi izi, ndipo palibe ubale ndi izi. Akatswiri ena achisilamu amanena kuti **al-Mukhalafatun li-l-hawadith** ndi **al-Wahdaniyya** ndi zofanana ndipo kuti chiwerengero cha as-Sifat adh-Dhatiyya chiyenera kukhala zisanu.

[2] Zizindikiro zisanu ndi zitatu (8) za **as-Sifat adh-Dhatiyya** ndi: **Hayu** (wamoyo), **Ilm** (kudzindikira), **Sam** (kumva), **Basar** (kuona), **Qudra** (wa mphamvu yonse), **Kalam** (kuyankhula ndi mau), **Irada** (kufuna) ndi **Takwin** (kulenga). Chirichonse mwa zizindikiro za Allahu Taala ndi zo patulika ndipo zili mu mmalo mwake. Sizisintha. Koma chirichinse mwa izo zimasiyana ubale mchikhalidwe mwake ndi zolendedwa.

[3] Za chilengedwe zonse zimasintha mmaonekedwa ndi mmachitidwe malinga ndi nthawi. Mathupi amakula ndipo zochita zimasintha. Zimapezeka ndipo nthawi ikamatha zimasowa kapena kusintha kukhala chinthu china. Mankhwala nawo amasintha mkagwiridwe ka ntchito nthawi ikamatha. Ndichifukwa chake mankhwala ali ndi nthawi yosiyira kugwiritsa ntchito.

sichiyenera kusintha. Dhat (uyekha) wa Allahu Taala ndi chizindikiro cha qadim ndipo sichimasintha. Kusintha kwa zolengedwa, kusanduka kwawo kukhala chinthu china, sizingakhale zopanda chiyambi. Zikuyenera kukhala ndi chiyambi, ndikuti zinakhala kuchokera ku zinthu zosiyanasiyana, zomwe ziyenera kuti zinalengedwa kuchokera popanda kanthu.

Umboni wina woti dzikoli ndi mumkin lidachita kulengedwa kuchokera popanda kanthu, kuti linabadwa kuchokera popanda, ndi woti zolengedwa ndi hadith; zakhala zikukhala popanda kuchokera popanda.

Pali zokhalapo ziwiri: **mumkin** ndi **Wajib**[1]. Panakakhala kuti panali mumkin okha, kapena kuti wajib al-wujud kunalibe, kukanakhala kopanda kanthu[2]. Pachifukwa ichi, Mumkin siikanapezeka kapena kukhalapo pa yokha. Pakanakhala kuti panalibe mphamvu ina yomwe inakhudza mumkin, ikanakhala kulibe ndipo siyikanakhalapo. Poti mumkin siyikanadzilenga yokha, mwachidziwikire siyikanakwanitsa kulenga mumkin zina. Choncho chomwe chinalenga mumkin chikuyenera kukhala Wajib al-wujud. Kupezeka kwa dziko kukusonyeza kuti kuli Mlengi yemwe analenga dzikolo kuchokora popanda. Choncho Mlengi wa zonse ndi Wajib al-wujud yekha yemwe Sali hadith kapena mumkin, koma wakhala alipo ndipo ndi wamuyaya. 'Wajib al-wujud' ikutanthauza kuti kupezeka kwake sikunachokere ku china chilichonse. Allah wakhala alipo payekha ndipo sanalengedwe ndi wina. Zinakakhala kuti siziri choncho ndiye kuti akanakhala cholengedwa (mumkin ndi hadith) olengedwa ndi wina. Izi ndi zotsutsana ndi zomwe zaunikiradwa pamwambapo. Mu chilankhulo cha chi Persia, 'khuda' (dzina la Allahu Taala) limatanthauza kuti "Chopezeka pachokha, chamuyaya'.

Tikuwona kuti magulu a zinthu zokhalapo ali mozizwitsa, ndipo sayansi imatulukira zina za zozizwitsazi chaka chilichonse. Mulengi wa dongosolo ili

[1] **Wujud** imatanthauza **kukhalapo.** Pali mitundu itatu ya kukhalapo. Mtundu woyamba ndi **Wajib alwujud,** kukhalapo kofunika, komwe kumapezeka nthawi zonse. Kwakhala komwe kunalipo mbuyo monsemu ndipo kudzakhalanso kutsogolo konse. Uku ndiye kukhala komuyenera Allahu Taala yenkha. -Mtundu wachiwiri ndi **mumtani alwujud, k**omwe sikungakhalepo. Sikuyenera kupezeka nthawi iliyonse. Kupezeka kwa mzake wa Allahu Taala kapena kuti mulungu wina wothandizana ndi Allah kapena wofanana ndi Iye sangakhalepo. - Mtundu wachitatu ndi **mumkin al-wujud**, komwe kungakhalepo kapena kulibe. Ngati za mudziko, zolengedwa zonse popanda kupatulapo. Liu lotsutsa ku wujud ndi adam (kusakhalapo). Zolengedwa zonse zinali mwa adam, zili ndi chiyambi.

[2] Pakuti kusintha ndi kukhalapo kwachinthu kuchokera popanda, ndipo kutengera zomwe tikudziwa kuchokera mu physics, kusintha kuti kuchitike pa chinthu, payenera kukhala mphamvu yapadera, yomwe gwero lake liyenera kukhala loyamba chinthucho chisanakhale.

ayenera kukhala **Hayy** (Wamoyo Wosatha), **Alim** (Wodziwa Zonse), **Qadir** (Wamphamvu zonse), **Murid** (wofuna), **Sami** (Wakumva chilichonse), **Basir** (Woona Zonse), **Mutakallim** (Wolankhula Zonse) ndi **Khaliq** (Mlengi)[1], chifukwa imfa, umbuli, kulephera, kukakamidwa, kusamva, kusaona ndi kusayalankhula ndi zilema zomwe mulibe mwa Iye. Sizingatheke kuti zilema zotero zikhale mzizindikiro za Allahu Taala Yemwe analenga zolengedwa zonse. Yemwe analenga mwaukadaulo ndi mu ndondomeko yotere, ndi kuziteteza ku chiwonongeko.

Komanso, tikuwona zizindikiro za ungwirozi mu zolengedwa. Allahu Taala analenga zolengedwa zonse mwa ungwiro. Kukanakhala kuti zizindikiro za ungwiro mwa Iye mulibe, Akanalenga bwanji zolengedwa mwa ungwiro? Kukanakhala kuti zizindikiro izi mulibe mwa Iye, zolengedwazo zikanakhala zopambana kuposa Iye. Komanso, timathanso kuona luntha mu zolengedwa. Allahu Taala anaika nzeru mu zolengedwazi. Akanakhala kuti Allahu Taala alibe lunthu, sakanakwanitsa kuika luntha mu zolengedwazi. Ndipo zolengedwazi zikanakhala zopambana kuposa Iye[2].

Tiwonjezeranso kuti Mlengi wa zolengedwa izi ayenera kukhala ndi zizindikiro zonse za ungwiro ndi ukulu ndipo asakhale ndi zizindikiro za kusowa chilichonse, pakuti yense wokhala ndi zizindikiro za kusowa sangakhale Khuda, Mlengi.

Kupatula maumboni omveka awa, ma ayah ndi ma Hadith afotokoza momveka bwino kuti Allahu Taala ali ndi zizindikiro za aungwiro. Choncho, nkosaloledwa kukaikira. Kukayikira kumayambitsa kusakhulupirira. Zizindikiro

---

[1] Awa ndi ma Sifat ath-Thubutiyya asanu ndi atatu a Allahu Taala. Amatchedwanso Sifat al-Hakikiyya, izi ndi zizindikiro zomwe pambali popezeka mwa Allahu Taala, zimapezekanso pang'ono mu zolengedwa zake.

[2] Chilichonse, kuyambira kanthu kakang'ono kwambiri kufikira pa nyenyezi, zalengedwa powerengetsera bwino komanso mwa malamulo. Kukhazikika kwa izi m'malamulo a Physics, Chemestry, za ku Mitambo, ndi mu Biology zimadodometsa anthu. Ngakhala Darwin ananena izi pomwe anaganizira za mapangidwe ndi kakhalidwe ka diso moti ankaona ngati adwala misala. Mpweya ndi kusakaniza ka 78% nayitrogeni, 21% oxygen ndi 1% gasi. Ndi kasakaniza osati zimapangidwa. Mpweya wa oxygen utachulukirapo kuposa 21%, mapapo anthu atha kupsya. Kungocheperako pang'ono pa 21% ndiye kuti chakudya chomwe tikudya sichingasungunuke mmagazi. Zikanakhala zosatheka anthu ndi nyama akhale ndi moyo. 21% imeneyi siisintha kwina kulikonse, ngakhale nthawi ya mvula. Ndipo awa ndi madalitso. Kodi sizikusonyeza Kukhalapo, mphamvu ndi chisomo cha Allahu Taala Kapangidwe ka diso si nkhani tikayerekezera ndi zodabwitsa za kasakanizidwe ka mphweyaka. Kodi n'zotheka kuti amene analenga zonse m'malamulo, powerengera mwakuya monga momwe timawonera m'maphunziro a sayansi angakhale ndi zizindikiro zolakwika?

zisanu ndi zitatu za ungwiro zomwe zatchulidwazi zimatchedwa as-Sifat ath-Thubutiyya. Allahu Taala ali ndi zizindikiro zisanu ndi zitatu za ungwiro. Alibe chilema, chisokonekera kapena kusintha mwa Iye, m'zizindikiro Zake kapena mu zochita. **As-Sifat adh-Dhatiyya** ndi **as-Sifat ath-Thubutiyya** zimatchedwa zizindikiro za Umulungu **(Uluhiyya)**. Ngati munthu akhulupirira kuti cholengedwa chiri ndi zizindikiro za umulungu, iye amakhala **mushrik** (womphatikiza Allahu Taala ndi zinthhu zina), ndipo ndi shirk.

## -3-

# NSICHI ZA CHISILAMU (1)

Mothandizidwa ndi Allahu Taala, Yemwe amasunga zolengedwa zonse kuti zikhale nthawi iliyonse, Yemwe amapezeka pali ponse nthawi zonse ndi kuyang'anira zonse, Yemwe amapereka zabwino zonse ndi mphatso kwa zolengedwa: tsopano tikuyamba kufotokoza zoyankhula zodalitsika za Mtumiki "sallallahu taala alaihi wa sallam"

Wokondeka wathu, achikulire Hazrat Umar ibn al-Khattab "radhiyallahu taala anh" , yemwe ndi ngwazi wa a silamu, mmodzi mwa abwenzi olemekezeka a Mtumiki wathu, yemwe anali wodziwika ndi chilungamo chake, adati: "Linali tsiku lomwe ena mwa ife, abwenzi, tinali kumutumikira Mtumiki Rasulullah "sallallahu alaihi wa sallam" Linali tsiku ndi ola lodalitsika, tsiku lofunikira kwambiri loti munthu ndi kumalakalaka litabweranso. Patsikuli, chinali chinthu cholemekezeka kukhala pafupi ndi Mtumiki, ndi kuona nkhope yake yodalitsika. Chinthu chomwe chinali chakudya cha uzimu ndi chisangalalo ndi chithondozo ku moyo. Pofuna kutsindika za phindu ndi ulemerero wa tsikuli, iye anati, "Lidali tsiku limenelo…." lingakhalepo tsiku lina lolemekezeka ndi la phindu loposa tsiku lomwe munthu angadzaone mngelo Jibrail (mngelo wamkulu Gabriel, alaihi-salam) atabwera mu thupi la munthu, kumva mawu ake ndi mzeru zomwe munthu amazifuna momveka bwino kudzera pa kamwa pa Mtumiki Rasulullah "sallallahu taala alaihi wa sallam"

"Pa nthawi imeneyo, mzibambo wina anatulukira ngati momwe umatulukira mwezi. Zovala zake zinali zoyera kwambiri, ndipo tsitsi lake lakuda kwambiri. Zizindikiro zoti anayenda mtunda wautali monga fumbi ku ma pazi ake ndi thukuta panalibe. Palibe angakhale mmodzi mwa ma Swahaba a Mtumiki "sallallahu alaihi wa sallam" amene anamuzindikira munthuyo. Anali munthu yemwe tinali tisanamuonepo ndipo sitimamudziwa. Anakhala pafupi ndi Mtumiki "sallallahu taala alaihi wa sallam" maondo ake atayika pafupi ndi maondo a Mtumiki". Munthu uyu adzadza mu thuphi la munthuyu anali mngelo Gabriel. Ngakhale kuti kukhala kwake sikunali kogwirizana ndi chikhalidwe

(adab), zinationetsa mfundo yofunikira kwambiri: osachita manyazi pophunzira za chipembezo, kudzikweza kapena kudzitukumula sikupangitsa munthu kukhala wodziwa. Mngelo Gabriel, anachita izi pofuna kuonetsa ma Swahaba kuti aliyense akuyenera kufunsa momasuka komanso mopanda manyazi kwa aphunzitsi. Pakuti sipafunika manyazi pophunzira za Chisilamu, kapena kunyozeka pochita, kuphunzitsa kapena kuphunzira udindo wako kwa Allahu Taala.

"Munthu wolemekezeka uja anaika manja ake pa maondo a Mtumiki "sallallahu taala alaihi wa sallam" Ndipo anamfunsa Mtumiki nati, 'Oh Iwe Mtumiki wa Allah! Tandiuza kuti Chisilamu ndi chiyani ndipo munthu angakhale bwanji msilamu.'"

Tanthauzo la **Chisilamu** ndi 'kudzipereka mogonjera'. Rasulullah "sallallahu taala alaihi wa sallam" anafotokoza kuti , liwu loti **Chisilamu** ndi dzina la gulu la zofunika (Nsichi) zisanu za Chippembezo cha Chisilamu zomwe ndi:

1 - Rasulullah "sallallahu taala alaihi wa sallam" anati, nsichi yoyamba ndi kunena "**Kalimah ash-shahada**"; munthu ayenera kunene kuti, **"Ashahadu an la ilaha illallah wa ashahadu anna Muhammadun Abduhu wa Rasulullah."** M'mawu ena, munthu wozindikira, yemwe watha msinkhu ndipo womatha kuyankhula ayenera kunena kuti, " **Pa dziko ngakhale mu mlengalenga mulibe chirichonse kapena wina woyenera kumupembeza kapena kumulambira mu choonadi kuposa Allahu Taala.** Mulungu wa choonadi ndi Allahu Taala. **Iye** ndi Wajib ul-wujud. Kupambana konse kuli mwa Iye. Mwa **Iye** mulibe chilema chilichonse. Dzina lake ndi Allah" munthu ayenera kukhulupirira izi ndi mtima wake wonse. Munthunso ayenera kunena ndi kukhulupirira kuti, "Muhammad ndi mtumiki wa Allahu Taala munthu wolemekezeka kwambiri wotchedwa Muhammad ibn Abdullah yemwe anali ndi nkhope yokongola kwambiri, maso ndi nsidze, wachipumi chotakasuka ndi chikongola, wa makhalidwe abwino yemwe mapewa ake sanagwepo pansi, woyankhula mowupeza ndipo amkatchedwa Arab chifukwa anabadwira ku Mecca si munthu ndipo mtumiki wotumizidwa ndi Allahu Taala." Mai ake a Mtumiki anali Hazrat Amina bint (mwana wa) Wahab. Kubadwa kwake ku Mecca kunadzetsa ulemerero dzikoli [mbandakucha wa lolemba limenelo la m'mwezi wa April m'chaka cha 571]. Ali ndi zaka 40, adauzidwa kuti iye ndi Mtumiki [linali lolemba m'mwezi wa Ramadhani chaka cha 610]. Chaka chimenecho chinatchedwa kuti ndi chaka cha **'Bi'tha'** (Mtumiki kutumizidwa kudzayitanira anthu ku njira yachiwongoko). Pambuyo pake, anaitanila anthu ku Chisilamu mu mzida wa Macca kwa zaka khumi ndi zitatu. Kenako anasamukila (Hijrah,) ku Madina molamulidwa ndi Allahu Taala. Kuchokera kumeneko, anafalitsa uthenga wa Chisilamu paliponse.

Patadutsa zaka khumi chisamukire ku Macca, Mtumikiyu anamwalira mu chaka cha 632 (lolemba pa 12 Rabi al- Awwal)[1].

2 - Nsichi yachiwiri ya Chisilamu ndi **kuswali kasanu pa tsiku**, **mu nthawi yake potsatira ndondomeko zake za machitidwe ake potsatira ma fardh.** Ndi zokakamizadwa kwa msilamu aliyense kudziwa nthawi ya **Swalah** komanso kuswali kasanu pa tsiku. Ndi tchimo lalikulu kutsatira makalendala opangidwa ndi anthu omwe satsatira madhhab aliwonse kapena yemwe si wa Sunni. Ndi tchimonso kuswali swalah nthawi yake isanakwane ndipo Swalah yoteroyo imakhala yosavomerezeka. Nthawi ya Swalah imadziwika ndi kuitana kwa mwazini. Mau a anthu osakhulupirira ndi a bidah komanso mkuwe wa zinkulisa mau sizingatchedwe azana al Muhammadi. Swalah iyenera kapempheredwa patsatira fardh, wajib komanso sunna [malamulo osiyanasiyana okhudzana ndi Swalah], nthawi yake yoikika isanathe ndipo popereka mtima wonse kwa Allahu Taal. Mu **Quran al-Karim,** pemphero limatchedwa **Swalah**, kutanthuza kuti munthu akupembedza, angelo akupanga istighfar (kupempha chikhulululuko kwa Allahu Taala) ndipo Allahu Taala amaonetsa chifundo. Mu Chisilamu, Swalah imatanthauza kupanga zinthu zina zake ndi kulakatula mau momnga zalembedwera m'mabuku a ilm al-hal. Swalah imayamba ndi **takbir al-iftitah**, ponena kuti '**Allahu akbar**'. Amuna akweza manja awo mpaka m'makutu, ndipo kenako agwire (dzanja la manja pamwamba pa dzanja la ku manzere) pa mimba cha pansi pa mchombo. Akazi aimike manja mpaka kulekeza mmapewa ndipo agwire (dzanja la manja pamwamba pa dzanja la ku manzere) m'mwamba mwa

[1] Malinga ndi olemba mbiri, Mtumiki analowa ku phanga m'phiri la Sawr cha ku madzulo a la chinayi pa 27 mwezi wa Safar mu chaka cha 622 (Gregory), pa msamuko wake (Hijra) kuchokera ku al- Makkat al-Mukarrama kupita ku al-Madinah al-Munawwara. Anachoka m'phangamo Lolemba usiku ndi kulowa mu Quba, chigawo chapafupi ndi Madina, Lolemba pa 8 mwezi wa Rabi ul-awwal (yomwe ndi 20 September mu kalindala ya Gregorian koma ndi pa 7 September mu kalindala ya Julian). Tsiku la chisangalaloli, lanadzakhala poyambira pa kalindala ya Asilamu ya Hijrah Shamsi (yotsatira mayendedwe a dzuwa). Kuyambika kwa kalindala ya Hijrah Shamsi yomwe imatsatilidwa ndi ma Shi'iah kunachitika mofulumirako ndi mwezi isanu ndi umodzi. Imayamba ndi chikondwelero cha Nawruz cha Majusi opembedza moto, pa 20 March. Mtumiki anakhala ku Quba mpaka la chinayi. Pa tsikuli kutalika kwa usana kunali kofanana ndi kwa usiku pa dziko lonse lapansi. Anachoka m'chigawocho la Chisanu ndi kulowa m'Madina tsiku lomwelo. Kuyamba kwa mwezi wa Muharram m'chaka chomwecho (Lachisanu, 16 July) kunavomerezedwa kukhala chiyambi cha Hijri Qamari (kalendala ya mwezi). Chaka cha Hijri Shamsi chomwe chaka cha Gregorian chikuyamba ndi chocheperako ndi zaka 622 pofanizira ndi chaka cha Gregorian chatsopano ndipo Chaka cha Gregorian chomwe chaka cha Hijri Shamsi chimayamba ndi chokulilapo ndi zaka 621 poyerekeza ndi chaka chatsopano cha Hijri Shamsi.

mabere awo. Pempheroli limatha ndi ma **salam** potembenukira ku manja komanso kumanzere munthu ali chikharire.

3 - Nsichi yachitatu ndi kulipira **Zakah pa chuma chako.** Tanthauzo la mawu oti zakah ndi 'chiyero, kuyamika ndi kukhala cha bwino ndi chokongola.' Pa Chisilamu, **Zakah** ndi yoyenera 'kwa munthu yemwe ali ndi chuma choposa chomwe iyeyo angachifune kuti agwiritse ntchito ndipo chapyola muyeso wotchedwa **nisab.** Munthu wotero ayenera kuchotsapo gawo lina la chuma chake ndi kupereke kwa Asilamu omwe **Quran al-Karim** yafotokoza kuti ndi oyenera kulandira choperekachi, ndipo achite izi posawachititsa manyazi olandirawo'. Zakah imaperekedwa kwa anthu a magulu asanu ndi awiri (7). M'Madhhab onse anayi, pali mitundu inayi ya Zakah. malingana ndi madhhab anayi: Zakah ya siliva ndi golide, Zakah ya katundu, Zakah ya ziweto za miyendo inayi zomwe zimadya kutchire koposa theka la chaka ndi Zakah ya zokolola zomera munthaka. Mtundu wa Zakah wa zokolola imatchedwa **ushr** ndipo imaperekedwa anthu akangomaliza kukolola. Mitundu ina itatuyi imaperekedwa ngati mulingo wafika pa Nisab.

4 - Nsichi yachinayi yachisilamu ndi 'kusala (kufunga) kudya tsiku lirilonse m'mwezi wa **Ramadan.**' Kusala kapena kufunga kumatchedwa **swaumu.** Swaumu ikutanthauza kuteteza chinthu ku chinthu china. M'Chisilamu Swaumu imatanthauza munthu kudziteteza ku zinthu zitatu [mu nthawi ya masana] m'mwezi wa Ramadan monga analamulira Allahu Taala: kudya, kumwa komanso kugonana. Mwezi wa Ramadan umayamba pamene mwezi waoneka. Mweziwu utha kuoneka potengera kuwerengera kwa nthawi za m'makalenda.

5 - Nsichi ya chisanu ya Chisilamu ndi kupita pa ulendo wa Hajji kamodzi pa moyo wa munthu kwa yemwe angakwanitse. Kwa munthu yemwe angakwanitse, zili zokakamiza kwa iye kupita kukapanga tawaf kuzungulira Kaaba komanso kupanga Waqfa pa chigwa cha Arafat. Zomkwaniritsa munthu kutero ndi kukhala ndi ndalama zokwanira kupita ku mzinda wa Macca ndi kubwererako, kukwanitsa kusiya zofunikira pa banja lake pamene iye ali pa ulendowo mpaka atabwera, ndipo kuti njira yoyendayo ili yabwino komanso kuti iye ali ndi umoyo wabwino.

"Atangomva mayankho awa kuchokera kwa Rasulullah "sallallahu taala alaihi wa sallam" munthu uja anati, 'Oh! Rasul-Allah! Wanena chilungamo.' Hazrat Umar "radiyallahu anh "anati ma Swahaba omwe analipo anali ozizwa ndi chikhalidwe cha munthuyu yemwe anafunsa funso komanso ndi kutsimikiza kuti yankho lake linali lolondola. Munthu amafunsa ndi cholinga chophunzira

zomwe sakuzidziwa; koma kunena kuti, “Wanena chilungamo,” zikusonyeza kuti ofunsayo akudziwa yankho.

Nsichi ya pa mwamba kwambiri pa zonsezi ndi kunena Kalimah ash-shahada ndi kukhulupirira tanthauzo lake. Ya chiwiri yake ndi kuswali kasanu pa tsiku. Yotsatira ndi kusala kapena kufunga chakudya. Kenaka, kupita ku Hajji ndipo yomaliza ndi kupereka Zakah. Ndi zotsimikizika kuti Kalimat ash-shahada ndi ya pa mwamba kwambiri. Akatswiri a Chisilamu amaperekanso ndondomeko yake monga tafotokozera pa mwambamo. Kalimat ash-shahada ndi imene inayambirira kukhala yokakamizidwa ku mayambiriro kwa Chisislamu. Swalah zisanu za pa tsiku zinakhala zokakamizadwa pambuyo pa Miraj m’chaka cha 12 cha Bi’tha; chaka ndi miyezi ingapo isanachitike Hijra. Kusala kudya m’mwezi wa Ramadan kunapangidwa kukhala faradh mu mwezi wa Shaban, m’chaka cha chiwiri cha Hijra. Kupereka Zakah kunakhala faradh m’mwezi wa Ramadan chaka chomwe kusala kunapangidwa kukhala fardh. Hajj inakhala fardh m’chaka cha 9 cha Hijra.

Ngati munthu akana, osakhulupirira, kunyogodola kapena kusalabadira za imodzi mwa nsichi izi. iye amasanduka kafiri (Allahu Taala atiteteze ku izi!). Chimodzimodzinso, munthu amene savomereza zomwe zavomerezeka kuti ndi za halal kapena za haraam,kapena yemwe amati halal chinthu cha haram kapena kunena kuti haram chinthu cha halal, nayenso amakhala kafiri. Ngati munthu akukana chimodzi mwa ziphunzitso za Chisilamu, iyeyo amasanduka Kafiri[1].

---

[1] Mwachitsanzo, kudya nkhumba, kumwa za kumwa zoledzeretsa, kuyenda njuga, mzimai kapena mtsikana kuonetsera thupi kwa ena wopanda chofunda m’mutu, tsitsi, mikono ndi miyendo komanso mamuna, kusaphimba gawo lapakati pa mawondo ndi mchombo, zonsezi ndi haram. Allahu Taala waletsa zinthu zimenezi. Madhhab anayi omwe **akufotokoza malamulo ndi zoletsedwa za Allahu Taala**, anafotokoza mosiyana za maliseche a mamuna. Ndi fard kwa Msilamu aliyense kuphimba ziwalo za thupi zomwe zafotokozedwa ndi madhhab omwe munthuyo akutsatira. Ndi haram kwa munthu yemwe akuyang'ana ziwalo za wina zomwe zanenedwa kuti ndi zobisika. Zalembedwa mu **Kimya as-Saada** kuti ndi haram akazi ndi atsikana kutuluka mnyumba asanaphimbe mutu, tsitsi, mikono ndi miyendo. Komanso ndi haram kutuluka atavuala chovala chopyapyala chokongoletsedwa, zothina ndi zothira mafuta onunkhiritsa.

Amayi awo, abambo awo, amuna awo ndi abale awo amene amalola kutuluka atavala izi nawonso adzagawana chimolo ndi chilango (adhab) chake; adzawotchedwa ku Jahena onse pa modzi. Koma ngati alapa, adzakhululukidwa ndipo sadzawotchedwa. Allahu Taala amakonda iwo olapa. M'chaka chachitatu cha Hijra, atsikana anzeru zawo omwe adafika zaka za kutha msinkhu ndi akazi, analamulidwa kuti asamadziwonetsere kwa amuna omwe ali namahram (omwe angate kukwatiwa nawo). Tisakhulupirire zonena za akazitape a ku Britain ndi anthu osadziwa amene adanyengedwa ndi iwo, kuti

kuvumbulutsidwa kwa Ayat ya kiziphimba (hijab) unali umboni kuti lamulo lophimba linali lopekedwa ndi akatswili a fiqh (sayansi ya Chisilamu).

Munthu amene amati ndi Msilamu ayenera kuonetsetsa kuti zochita zao zonse ziyenera kugwirizana ndi Chisilamu kapena ayi. Ngati asakudziwa ndiye kuti ayenera kuphunzira pofunsa akatswiri a Ahl as-sunna kapena powerenga mabuku awo. Zochita zawo ngati ziri zosagwirizana ndi Chisilamu, sadzalithawa tchimo kapena kusakhulupirira. Ayenera kulapa tsiku lililonse. Tchimo kapena kusakhulupirira komwe kwalapidwa ndithudi kudzakhululukidwa. Ngati salapa, adzalipira pa dziko lapansi pano komanso ku moto. Zilango zimenezi zalembedwa m'magawo osiyana m'bukhu lathu lino. Msilamu amene wachita tchimo lalikulu adzatulutsidwa ku moto atawotchedwa kaye molingana ndi tchimo lake. Iwo omwe sakhulupilira Allahu Taala ndi osakhulupirira omwe amayesetsa kuononga Chisilamu, ma Zindiq adzakhala ku moto kwa muyaya.

Zowalo zomwe amuna ndi akazi ayenera kuphimba nthawi ya Swalah kapena pa nthawi ina iliyonse

Pena paliponse zimatchedwa '**awrat**'(malo a chinsinsi). Ndi haram kuonetsa malo a chinsinsi ngakhale kuona malo a chinsinsi a wina. Ngati munthu anena kuti palibe chifukwa cholingalira za dzina la awrat mu Chisilamu, iye amakhala wosakhulupirira. Ngati munthu anena za 'halal' kapena sakulipira kufunikira kwake, ndiye kut iye saopa chilango choperekedwa (adhab) powonetsa kapena kuyang'ana maliseche malinga ndi mgwirizano (ijma) wa m'madhhab onse anayi ndipo munthu woteroyo amakhala wosakhulupirira. Chimodzimodzi mzimayi wonetsa madera awo a awrat kapena kuyimba kapena kulakatula Mawulidi (chikondwerero cha kubadwa kwa Mtumiki Muhammad 'alaihi-salam) pakati pa amuna.

Munthu amene amati ndi Msilamu ayenera kuphunzira ndi kulemekeza nsichi za Iman ndi Chisilamu pamwamba pa malamulo (fardh) ndi zoletsedwa (haram) zomwe zinalengezedwa m'madhhab onse anayi. Kusadziwa si chingakhale chifukwa chomveka ndipo ndi chimodzimodzi kusakhulupirira ngakhale akudziwa. Malingana ndi madhab zinayi onse, thupi la mkazi lonse ndi awrat kupatula manja ake ndi nkhope yake. Ngati munthu mosasamala awonetsa gawo la thupi lawo lomwe liri awrat pomwe palibe panenedwa ndi m'madhhab aliwonse kuto gawolo si awrat iye sadzakhala wosakhulupirira koma ndi tchimo la likulu malinga ndi madhhab omwe amawatsata. Chitsanzo cha ichi ndi cha mamuna kuonetsa ntchafu yake, gawo la pakati pa chiuno ndi mawondo. Ndi zokakamizidwa kuti munthu aphunzire zimene sakuzidziwa.

Munthu akangophunzira, ayenera kulapa ndi kudziphimba yekha. Kunama, miseche, mijedo, kunyogodola, kuba, kusakhulupirika, chinyengo, kuyika ena mmavuto, kumverera kwa wina, kuchita zoipa, kugwiritsa ntchito chuma cha wina popanda, kumumvetsa wina kuwawa, kuchita zosokoneza, kugwiritsa ntchito za eni popanda chilolezo, kusalipira ogwira ntchito kapena wakunyamulira katundu, kuwukira kapena kutsutsa malamulo ndi zigamulo za boma, ndi kusapereka sonkho ndi machimo, nawonso. Kuwachitira Osakhulupirira kapena kwa Osakhala Asilamu mayiko ndi haram. Si kufuru (Kusakhulupirira) koma ndi tchimo (fisq) kwa anthu osaphunzira kusadziwa ziphhunzitso zomwe siziri zofalikira kwa anthu omwe sanaphunzire.

## -4-

# NSICHI ZA IMAN (2)

"Munthu wolemekezeka uja anafunsanso. ' **Oh iwe Mtumiki wa Allah! kodi Iman itanthauza chiyani.'** Atafunsa kuti chisilamu ndi chiyani ndipo atayankhidwa, Hazrat Jibrail alaihi-salam adafunsa bwana wathu Rasulullah "sallallahu taala alaihi wa sallam" kuti afotokoze Tchutchutchu wa **Iman** ndi kuti mu Iman muli chani. Mawu oti Imani amatanthauza kumudziwa Allahu Taala kuti ndi wa choonadi ndiponso kukhulupirira mwa iye.

M'Chisilamu, Imani imatanthauza kukhulupirira kuti Rasulullah "sallallahu taala alaihi wa salam" ndi Mtumiki wotumizidwa ndi Allahu Taala ; kudziwa kuti izi ndi zoona komanso kunena ndi chikhulupiriro kuti iye ndi Nabi, Mtumiki wosankhidwa ndi Allahu Taala; kukhulupirira zonse zomwe ankanena kuchokera kwa Allahu Taala, ndi kunena Kalimat ash-shahada ndi pa kamwa momwe ungathere. Iman yeniyeni ikhale ngati mmene timadziwira kuti moto umaotcha, njoka imapha ndi poizoni wake, ndipo timadzipewa. Chomodzomodzi tiyenera kukhulupirira mwa Allahu Taala ndi zizindikiro zake, ndipo kuti ndi zopambana. Izi zikhala pa mtima poyetsetsa kupanga zinthu zovomerezeka (rida), kuthamangira ku zabwino Zake (jamal), kupewa mkwiyo Wake (ghadab) ndi chilango (adhab), ndikukhala ndi Iman yeniyeni mu mtima ngati chidindo chosachoka.

Iman ndi Islam zinaperekedwa ndi Muhammad alaihi-salam ndi zomwezo. Kukhulupirira mutanthauzo la Kalimat ash-shahada zili mu zonse ziwiri. Ngakhale zimasiyanako pozitchula ndi m'mafotokozedwe koma palibe kusiyana pakati izi mu Chisilamu. Kodi iman ndi chinthu chimodzi kapena ndi zigawo zophatikizana zingapo? Ngati ndi zophatikizana, ili ndi zigawo zingati? Kodi amal (zochita) kapena Ibadat (kupembedza) gawo limodzi la Iman kapena ayi? Ponena kuti, "Ndili ndi iman," kodi ndi bwino kuwonjezera mau oti **"Inshallahu taala"** (ngati Allahu Taala afuna) kapena ayi? Kodi pali kuchepetsa kapena kuchulukitsa Iman? Kodi iman ndi cholengedwa? Kodi ndi kotheka munthu pa yekha kukhulupirira, kapena pali mphamvu ina yokakamiza kuti munthu akhale ndi iman? Ngati pali mphamvu yokakamizayo, ndi chifukwa chiyani aliyense analamulidwa kukhulupirira? Zitha kutenga nthawi kuti kufotokoza zonsezi. Pa chifukwa ichi sindiyankha chimodzichimodzi panopa. Koma tikuyenera kudziwa kuti malinga ndi Ash'ari (imodzi mwa sukulu yoona za itikad ya malamulo a Chisilamu a Sunna, yomwe idayambitsidwa ndi Imam Abu al-Hasan al-Ash'ari, quddisa sirruh, motsatira madhhab a Shafi ndi Maliki) ndi Mu'tazila (limodzi mwa magulu 72 ogalukira a bid'at) sizotheka (jaiz) kuti Allahu Taala atilamule

ife kuchita chinthu chosatheka. Malinga ndi Mu'tazila, ndi zosatheka kuti Allahu Taala alamule chinthu chotheka koma chomwe munthu sangachikwanitse kuchita.

Malinga ndi Ash'ari, ndi zotheka koma Allahu Taala sanazilamule. Kulamula anthu kuwuluka mu mlengalenga ndi chitsanzo cha izi. Palibe pomwe Allahu Taala analamula munthu kuchita zomwe sangakwanitse kaya pa Imani ngakhale pa zochita. Pa chifukwa ichi, ngati munthu pomwe ali msilamu, adwala misala, kapena matenda oiyiwala iwala (ghafla), agona kapena amwalira, amakhalabe msilamu ngakhale ali mu kusazindikira.

Tanthauzo lenileni la Iman lisaganirizidwe potengera hadith sharif iyi chifukwa aliyense, ngakhale mbuli zomwe ku Arabia zimadziwa tanthauzo loti 'chitsimikizo, chikhulupiriro. Zachidziwikire kuti ma Swahaba al-kiram "radiyallahu taala anh"um ajmain amadziwa izi. Mngelo Gabriell alaihi-salam pofunsa Rasulullah alaihi-salam za tanthauzo la Imani mu Chisilamu, amafuna kuphunzitsa tanthauzo la Iman lenileni kwa ma Swahaba. '**Iman**' ikuthanthauza kukhulupirira ndi mtima wonse, ndi mzimu ndi kunena ndi pakamwa nsichi zisanu ndi imodzi potsimikiza kudzera mu kashf (osadziwika) kapena wijdah (chikumbumtima), pomvetsetsa kwa a nzeru kuchokera mu umboni kapena podalira kapena kutengera zonenedwa zovomerezeka. Rasulullah "sallallahu taala alaihi wa salam" anati iman ndi kukhulupirira mfundo zisanu ndi imodzi zomwe ndi:

1 - Choyamba ndi kukhulupirira kuti **Allahu Taala ndi Wajib al-Wujud (Wofunikira) ndipo ndi Mulungu woonadi (Maabud) Mlengi wa zonse.** Zikuyenera kukhulupiridwa kuti Iye yenkha ndiye amalenga chilichonse [ kanthu kalikonse, ma atomu, ma molekyu, ma elementi, ma kompaundi, tiziduswa tomwe timapanga thupi, moyo, imfa, zochitika zilizonse, mphamvu zonse, mayendedwe, mizimu, angelo, ndi china chilichonse chamoyo ngakhale chopanda moyo, ndipo amazipanga za moyozo kukhalabe ndi moyo], pa dziko pano ngakhale lomwe lili nkudza, ndipo analenga zonsezi kuchokera popanda kanthu. Poti analenga zonse za pa dziko[pa ka mwakamodzi kuchokera popanda], Iye [amalenga zina kuchokera ku zinzake, ndipo tsiku la chiweruzo likadzafika mwa kamodzi], adzaononga zonse. Iye ndi Mlengi, Mwini zonse, Wolamulira zolengedwa zonse. Ziyenera kukhulupiliridwa ndi kuvomerezedwa kuti palibe yemwe angalamulire kapena kukhala wapamwamba kuposa Allahu Taala. Kupambana kulikonse, zizindikiro za ungwiro zonse ndi za Iye yekha. Alibe chilema ndipo alibe zizindikiro za kuperewera kuli konse. Iye amapanga zomwe wafuna. Zomwe amapanga sapangira kuti apindule kapena kupindulira ena. Sapanga chinthu ndi cholinga choti alandire mphoto. Mu ziri zonse zomwe

amapanga pamakhala chifukwa chobisika (hikma), ntchito zake, madalitso ndi kukondera.

Allahu Taala sayenera kuchita za bwino ndi zofunikira kwa zolengedwa zake kapena kulipira anthu ena ndi kulanga ena. Zingakomera ulemerero wa Allahu Taala ndi chifundo chake ngati angabweze ochimwa onse ku m'Paradiso. Ndipo chingakhale chilungamo chake ngati ataika onse omumvera ndikumupembedza ku moto. Koma analengeza ndi kulamula kuti adzalowetsa Asilamu, omwe amamupembedza ku mparadiso ndi kuwakondera. Ndipo kuti adzalanga anthu osakhulupirira ku moto wa Gahena kwamuyaya. Iye sasintha zomwe wayankhula.

Palibe chingasinthe mwa iye za moyo zonse zitakhulupirira ndi kupembedza Iye, komanso palibe chingapunguke mwa Iye ngati zolengedwa zonse zitakana kukhulupirira, kapena Kusamvera Iye. Munthu akafuna kuchita kanthu, Allahu Taala amachipanga kuti chitheke ngati Iye wafuna kuti chichitike. Iye yekha ndi amene ali ndi kuthekela kwa chochitika chilichonse cha munthu kapena zolengedwa zake. Akapanda kufuna kapena kulenga, palibe chomwe chingayende. Ngati Iye sanafune, palibe yemwe angakhale osakhulupirira kapena wotayika. Amalola kusakhulupirira ndi utchimo kuti zichitike, koma sikuti amazikonda. Palibe yemwe angasokoneze ntchito za Allahu Taala Palibe yemwe ali ndi mphamvu kapena ufulu wofunsa kuti wapangiranji ichi kapena icho kapena kuyikira ndemanga za momwe angachitire chinthu. Kupatulapo Shirk (tchimo lomuphatikiza Allahu Taala ndi chinthu china), kapena kusakhulupirira mwa Iye. Allahu Taala akakhululuka ngati atafuna kutero munthu yemwe angamwalire wosalapa tchimo lake angakhale litakula, kupatula Shirk komwe ndi kuphatikiza Allahu Taala ndi chinthu china. Allahu Taala adzalanga (akafuna) munthu chifukwa cha machimo awo ang'ono. Allahu Taala akazunza ku moto Asilamu a **Ahl al-qibla** (opembedza ndipo amayang'ana ku Kaaba popemphera) koma omwe itiqad (iman ndi chikhulupiriro) chili chosakwanira pa **Ahl as-Sunna** ndipo akumwalira asanalape. **Asilamu otero, a bidah**, sadzakhala ku moto kwa muyaya.

Ndi zotheka kumuona Allahu Taala ndi maso pa dziko pano., koma sanaonekepo. Pa bwalo la nkumano (Mahshar) pa tsiku la chiweruzo, osakhulupirira ndi Asilamu ochimwa adzaomuona wankhanza ndi wokwiya. Koma Asilamu Oopa Allah ndi olungama adzamuona wachifundo ndi wokongola. Ku mParadiso okhulupirira adzamuona kukongola kwake. Angelo ndi azimayi nawo adzamuona. Anthu wosakhulupirira adzamanidwa izi. Palinso malipoti ena omwe amanena kuti ziwanda sizikamuonanso Allahu Taala Malinga ndi ma Ulama ambiri, "Asilamu omwe Allahu Taala amawakonda akalemekezedwa poona kukongola (tajalli al-jamal) komanso powona (ruyat)

ya Allahu Taala ku mmawa ndi ku madzulo kulionse. Asilamu omwe amayeserako kuchita zabwino azikalandira ulemerero la chisanu lililonse ndipo akazi azikamuona nthawi zochepa pa chaka nthawi ngati za chisangalalo pa dziko lapansi[1].

Tiyenera kukhulupirira kuti Allahu Taala adzaonedwa, koma tisamaganizire kuti adzaoneka bwanji poti ntchito zake sitingazimvetse potengera ndi nzeru zathu. Ntchito zake ndi zosafanana ndi za dzikoli.. [Sizingawunikidwa ndi mphamvu ya kuthupi kapena ya mankhwala.] Sitingamufanizire ndi china chirichonse. Iye si chinthu chogwirika, kapena chosagwirika. Iye sangawerengeke kapena kuyezedwa. Mwa Iye palibe chomwe chimasintha. Amapezeka paliponse ndipo pa nthawi iriyonse. Alibe kale kapena mtsogolo, kumbuyo kapena kumaso, pansi kapena pa mwamba, ku manja kapena ku manzere. Choncho malingaliro amunthu, kudziwa kapena luntha sizingamvetse chilichonse cha Allahu Taala Kotero kaganizidwe kapena nzeru za munthu sizingamvetse za Allaha Taala. Munthu sangamvetse mmene Allahu Taala angadzaonekere. Mawu onga dzanja, phazi, mbali, malo ndi ena otero, omwe amapezeka mu ma ayah ndi m'ma hadith, sagwirizana ndi mmene alili Allahu Taala. Mauwa samagwiritsidwa ntchito ngati mmene tikugwiritsira ntchito lero. Ma ayah komanso ma hadith amenewa amatchedwa **mutashabihat** (mawu omwe ali ovuta kuwamvetsa, okhala ndi matanthauzo obisika). Tikuyenera kuwakhulupirira koma tisalingalire kwambiri kuti tiwamvetsetsa ndi mmene aliri. Atha kutanthauziridwa mu **tawil,** mwachidule kapena motambasula, kutanthauza kupatsidwa mathanthauzo omwe angagwirizane ndi Allahu Taala. Mwachitsanzo, liu loti 'dzanja' litha kutanthauziridwa ngati mphamvu.

Muhammad alaihi-salam adamuona Allahu Taala pa ulendo wa Miraj. Koma kuona uku sikunali koona ndi maso ake, ngati mmene tikuoneramu. Munthu

[1] Hazrat Sheikh Abd al-Haqq ad-Dahlawi yemwe anamwalira ku Delhi mu chaka cha 1642/1052] analemba m'buku lake la chi Perisia atchedwa Takmil al-iman motere: "Hadith Sharif ikunena kuti: **'Udzamuona Mbuye wako pa tsiku la chiweruzo monga momwe iwe uonera mwezi [wathunthu] monga muuuwonera pakati pa mwezi pa 14.'** Monga Allahu Taala akudziwikira mosamalizika m'dziko lino, Iye adzawoneka mosakwanira pa tsiku lomaliza. Akatswiri akuluakulu monga Abul- Hasan al-Ashari, al-Imam as-Suyuti ndi al-Imam al-Bayhaki ananena kuti nawo angelo adzamuona Iye ku m'Paradaiso. Al-Imam al-azam Abu Hanifa ndi akatswili ena adanena kuti majini (Zolengedwa zosaoneka za nzeru, zolengedwa kuchokera ku moto, za pamwamba pambuyo angelo) sanalandire thawab (malipiro operekedwa ku Tsiku Lomaliza chifukwa cha ntchito zabwino ndi kuopa Alla) ndipo sakalowa ku Paradiso; ndi okhulupirika okha sakalowa ku Gahena. Akazi adzaona Allahu Taala kangapo pa chaka monga ngati nthawi za zikondwerero pa dziko lapansi. Ma kamil (Okhulupirira Angwiro) adzidzamuwona Iye m'mawa ndi ma dzulo aliwonse pamwe ena adzidzamuwona Ia chisanu lokha.

amene anganene kuti waona Allah pa dziko pano, ndi zindiq (munthu wonamizira kuti ndi msilamu). Kuona komwe ankaona ma awliya (Allahu Taala apange ntchito zawo kukhala zoyera, zodalitsika komanso zopatulika ndi kupanga ntchito zawo zabwino ndi zodalisidwa) sikuli ngati kuona kwa dziko lapansi kapena kwa dziko lili mkudza. M'mawu ena, sikunali **ruyat** (kuona) koma **shuhud** [kuona zitsanzo kupyolera mu 'maso' a mitima yawo] zomwe anakumana nazo. Ma Awliya ena akuluakulu anati anamuona Allah koma amasokoneza ndi shuhud zomwe adakumana nazo pamene anali chikomokere (sakr), ya ruyat. Kapena awa ndi amodzi mwa mawu awo oti amvetsedwa pofotokoza.

**Funso**; "Zanenedwa m'mwambamu kuti ndi zotheka (jaiz) kumuona Allahu Taala ndi maso athu padziko pano. Ndi chifukwa chani munthu amene wanena chinthu choti ndi chotheka akutchedwa Zindiq? Wonenayo atakhala wosakhulupirira, tinganene kuti ndi zotheka?''

**Yankho**; tanthauzo la 'jaiz' ndi 'zotheka kuchitika kapena ayi.' Koma malinga ndi madhhab a al-Ashari [Abul-Hasan Ali ibn Ismail, yemwe anamwalira ku Baghdad mu chaka cha 941/330], kuthekera kwa ruyat (kuona) kutanthauza kuti ndi kotheka Allahu Taala kupanga munthu kuona mwamtundu wina, mosiyana ndi kuona kwa dziko lino. Kuona posadzera m'maso koma mnjira Yake malinga ndi kuthekera kwake. Mwachitsanzo, atha, ndipo ndi zotheka, kumuonetsa munthu wa khungu yemwe ali ku China, udzudzu womwe uli ku Andalusia (ku mmwera kwa Spain) komanso atha kuonetsa chiri chonse pa mwezi kapena pa nyenyezi kwa munthu woti ali pa dziko la pansi. Mphamvu zotere ziri ndi Allahu Taala yekha. Chachiwiri, kunena kuti "Ndamuona Allahu Taala pa dziko pano" ndi zosagwirizana ndi ma (ayah al-karima) komanso ndi zomwe ma ulama (akatswiri ophunzira a Chisilamu) amagwirizana pa nkhaniyi. Choncho munthu amene anganeno motero ndi **mulhid** kapena **zindiq**[1]. Pa yankho lachitatu, "Ndi zotheka kumuona Allahu Taala pa dziko pano," sizitanthauza kuti ndi zotheka kumuona Allahu Taala pogwiritsa ntchito maso a ku thupi. Koma, munthu yemwe akuti adamuona amatanthauza kuti adamuona ngati mmene aonera zinthu zina. Kuona uku ndi kosatheka. Munthu yemwe angatero ndi mulhid kapena zindiq. [ patayankhidwa izi, Hazrat Maulana Khalid adalemba kuti, "Samalani!" adakhazikika pa yankho la chiwiri lomwe limamveka mosavuta].

[1] Ma **mulhid** kapena ma **zindiq** amati iwo ndi Asilamu. Ma mulhid amanena zowona ndi mtima wonse; amakhulupirira kuti iwo ndi Asilamu ndipo ali pa njira yoongoka. Koma ma zindiq ndi adani a Chisilamu, omwe amadziwonetsera ngti Asilamu ndicholinga choononga Chisilamu ali mkatimo ponyenga Asilamu.

Kudutsa kwa nthawi, usana kapena usiku, sizingafananizidwe ndi Allahu Taala. Poti Iye sasintha, sizinganenedwe kuti Iye anali chonchi kale ndipo adzakhala chonchi mtsogolo. Sasanduka (hulul) kalikonse[1]. Saphatikizana ndi chilichonse. Alibe otsutsana naye,ofanana naye, wongwira naye ntchito kapena womuthandiza ngakhale mtetezi. Alibenso bambo, mayi, mwana kapena mkazi. Amapezeka nthawi zonse komanso pali ponse ndipo amayang'anira chilichonse. Ali pafupi ndi wina aliyense kuposa msempha wake waukulu wa magazi. Koma, kupezeka kwake, umodzi, chifupi ndi ife, kutizungulira kwake, sikuli ngati momwe ifeyo timadziwira. Kutiyandikira Kwake sikungamvetsetseke ndi nzeru za ophunzira, kapena a sayansi, kapena ndi kashf kapena shuhud za awliya (qaddas-Allahu Taala asrarahum ajmain). Kaganizidwe ka munthu sikangamvetse mathanthauzo ake akuya. Allahu Taala ndi wopatulika mu Dhat (mmene alili) komanso mu zizindikiro zake (Sifat). Palibe kusintha kapena kusiyana kumachitika mwa izi.

Mayina a Allahu Taala ndi a **tawqifi**, (kutanthauza kuti ndi mayina okhawo omwe asonyezedwa ndi Chisilamu omwe ali ololedwa kugwiritsidwa ntchito ndipo ndi kosaloledwa kuonjezera mau ena[2]. Mayina ake ndi opanda malire. Ndi zachidziwikire bwino kuti Iye ali ndi mayina 1001 omwe anawavumbulutsa kwa anthu. Mu Chisilamu anavumbulutsa mayina 99 omwe amatchedwa '**al-Asma al-husna'.**

**Sifat adh-Dhatiyya** (zizindikiro za umwini) za Allahu Taala zilipo zisanu ndi chimodzi (6). **Sifat ath-Thubutiyya** (zizindikiro za ungwiro) za Allahu Taala zilipo zisanu ndi zitatu (8) malinga ndi **Maturidiyya** (imodzi mwa sukulu za itikad zomwe ndi za Sunni, zoyambitsidwa ndi Imam Abu Mansur Al Maturidi 'quddisa sirruh, ndi kutsatiridwa ndi sukulu za malamulo za Hanafi ndi Hanmbali) ndipo zisanu ndi ziwiri (7) mu **Ash'ari**. Zizindikiro za Allahu Taala zomalizirazi ndi za muyaya ndipo zopanda malire ngati Iye mwini. Ndi

[1] Ma Shia omwe ali m'gulu lotchedwa 'Nusayri' amakhulupirira kuti Allahu Taala anasanduka Hadrat Ali. Chikhulupiriro cholakwika ichi chimapangitsa iwo akhale osakhulupirira.

[2] Mwachitsanzo, Allahu Taala atha kutchedwa 'Alim' (wodziwa zonse); koma sitingagwiritse ntchito liwu lakuti 'faqih' lomwe limatanthauzanso 'alim' (katswiri, munthu wophunzitsidwa mu sayansi ya Chisilamu), pakuti Chisilamu sichigwiritsa ntchito 'faqih' kwa Iye. Chimodzimodzi ndi kosaloledwa kunena kuti 'Mulungu' m'malo mwa Allahu Taala, chifukwa 'mulungu' amatanthauza 'fano' kapena 'milungu'; "Ng'ombe ndi mulungu wa ma Hindu," zimanenedwa choncho. Ndi zololedwa kunena kuti: "Allahu Taala ndi Mmodzi; palibe mulungu koma Allahu Taala Mawu ngati Dieu (chi French), Gott (chi German) ndi Mulungu akhoza ugwiritsidwa ntchito pa mafano kapena milungu, koma osati kwa Allahu Taala.

zopatulika. Siziri ngati zizindikiro za zolengedwa. Sitingazimvetse poganizira, kapena pofanizira ndi zolengedwa. Wapereka kwa anthu fanizo la chilichonse mwa zizindikiro zimenezi. Powona mafanizo amenewa, zizindikiro Zake zitha kumveka pa mlingo wina. Popeza munthu sangamumvetse, ndi kosaloledwa kuganiza kapena kuyesa kumuzindikira. Zizindikiro Zake zisanu ndi zitatu sizili zofanana ngati zina kupatula Dhati Yake; ndiko kuti, zizindikiro Zake Sizipanga Dhati Yake, ndipo siziri zina kama Iye. Zizindikiro zisanu ndi zitatuzi ndi: **Hayy** (Wamoyo Wonse), **Ilm** (kudziwa zonse), **Sam** (Kumva), **Basar** (Kuona), **Qudra** (Wa mphamvu zonse), **Kalam** (Kulankhula, Mawu), **Irada** (Kufuna), ndi **Takwin** (Luso lolenga). Mu madhhab a Ash'ari, Takwin ndi Qudra imapanga Chizindikiro chimodzi. Mashiyya (Chifuniro cha Mulungu) ndi Irada ndi zofanana.

Zizindikiro zonse, zisanu ndi zitatu za Allahu Taala ndi zolingana ndipo ndi zopatulika. Sizisintha, koma chirichonse mwa izo zambiri ku zolengedwa. Zoti chizindikiro cha Iye ndi chochuluka pofanizira zolengedwa kapena momwe chikukhuzira zolengedwa sizisitha kulingana kwake. Ngakhale analenga zolengedwa zosiyanasiyana ndikumaziteteza ku chionongeko nthawi zonse, Iye akanali Mmodzi yekha. Palibe kusintha komwe kumachitika mwa Iye. Cholengedwa chirichonse chimafuna Iye mphindi iliyonse mu chirichonse. Iye sanalira cholengedwa chilichonse.

2 - Chachiwiri mwa mfundo zisanu ndi chimodzi zomwe ndi zofunika kuzikhulupirira ndi **"ku khulupirirani angelo a Allahu Taala** 'Lilayika' (mngelo) amatanthauza 'nthumwi', 'wotumidwa' kapena 'mphamvu'. Angelo ndi zolengedwa koma ndi owala kwambiri (latif). Iwo ndi nurani (owala,mwauzimu). Ali ndi moyo ndipo ndi a nzeru (aql). Uchimo wa anthu siupezeka mwa angelo. Amatha kusintha m'maonekedwe awo ndipo atha kuoneka ngati chilichonse. Monga momwe mpweya umasandukira kukhala madzi ndi kuundana ndikukhala chinthu cha mawonekedwe, angelo nawo amatha kuzipanga ndi kukhala ndi manekedwe okongola. Angelo si mizimu yochokera ku mathupi a anthu ofunikira ayi. Akristu amaganizira kuti angelo ndi mizimu yotero. Mosiyana ndi mphamvu, iwo sali osaoneka. Anthu ofuna luntha (mafilosofa) ena akale ankaganiza kuti angelo anali osaoneka. Angelo onse amatchedwa **'malaika'.** Angelo analengedwa za moyo zonse zisanalengedwe. Kotero talamulidwa khulupirirani angelo tisanakhulupirire mabuku akumwamba, amene anatsika tisanakhulupirire aneneri; ndipo **m'Qur'an al-Karim** mayina a zikhulupiliro izi mundondomeko yotero.

Kukhulupirira mwa angelo kukuyenera kukhala motere: Angelo ndi zolengedwa za Allahu Taala Angelo si athandizi a Allah kapena ana ake akazi ngati mmene anthu osakhulupirira amanenera. Allah amakonda angelo onse ndipo iwo amamvera malamulo onse a Allahu Taala komanso samachimwa.

Angelo si akazi kapena amuna, sakwatiwa kapena kukwatira. Alibe ana ndipo ndi amoyo. Zomwe zanenedwa mu lipoti la Hazrat Abdullah ibn Masud ("radiyallahu taala anh") zoti angelo ena anali ndi ana, kuphatikizapo satana ndi majini, zayankhidwa m'mabuku ena mwatsatanetsatane. Pamene Allahu Taala analegeza kuti akufuna kulenga anthu, angelo anafunsa, "Oh Allahu Taala! Kodi mukufuna kulenga cholengedwa chomwe chidzaononge ndi kukhetsa mwazi pa dzikoli?'' Mafunso ngati awa, omwe amatchedwa '**zalla**' ochokera kwa angelo samasonyeza kuti angelo ndi olakwa pokayikira.

Mu zolengedwa zonse, angelo ndiwo ali ochulukitsa. Palibe yemwe amadziwa chiwerengero chawo kupatula Allahu Taala. Paliponse mulengalenga pali angelo akumpembedza Allah. Pali ponse pali angelo, ena pa ruku (kuwerama pa swala), ena pa sajda (kuika chipumi pansi). Mu mlengalenga, pa dziko, mu udzu, pa nyenyezi, mu cholengedwa cha moyo ndi chopanda moyo, mu dontho lililonse la mvula, tsamba la chomera, atomu, molekyu, mkuchita kulikonse, angelo ali ndi gawo. Amachita zomwe zotumidwa ndi Allahu Taala. Iwo ndi mkhala pakati pakati pa zolengedwa ndi Allahu Taala Ena mwa iwo ndi apamwamba poyerekeza ndi ena. Ena mwa iwo amkatenga uthenga kupititsa kw atumiki. Ena mwa iwo amabweretsa maganizo abwino m'mitima ya anhtu omwe amatchedwa **'ilham'** (kudzodza). Angelo ena anasiya kuzindikira kuti kuli anthu ndi zolengedwa kamba ka kukongola kwa Allahu Taala. Aliyense mwa angelo awa ali ndi malo awo ndipo sachoka pa malopo. Angelo ena ali ndi mapiko awiri, ena anayi ndipo ena kuposera apo[1].

Angelo aku m'Paradaiso amakhala ku m'Paradaiso. Wamkulu wawo ndi **Ridwan**. Angelo aku Gahena, ma **Zabani**, amachita zomwe analamula kuchita ku motoko. Iwo samapsya ndi Moto wa Gahena, monga nsomba zizivutika m'madzi. Pali ma Zabani otsogolera khumi ndi asanu ndi anayi (19). Mkulu wawo ndi **Malik**.

Munthu aliyense ali ndi angelo anayi omwe amalemba ntchito zake zabwino ndi zoipa. Awiri amabwera masana ndipo enawo amabwera usiku. Amatchulidwa '**kiraman katibin'** angelo (olemba opanda ziphuphu) kapena

[1] Monga momwe mapiko a mbalame ndi mapiko a ndege za mtundu uliwonse zili zopangidwa mosiyana ina ndi imzake, nawo mapiko a angelo ali ndi mawonekedwe awoawo. Tikamva dzina la chinthu chomwe sitinachiwone kapena chomwe tasakuchidziwa, talakwitsa poganiza kuti zili ngati zinthu zomwe timadziwa. Timakhulupirira kuti angelo ali ndi mapiko, koma sitidziwa momwe amaonekera. Zithunzi za azimayi a mapiko m'matchalichi, mu zofalitsa kapena m'mafilimu, zomwe zimatengedwa ngati angelo ndi zabodza. Asilamu sapanga zithunzi zotere. Tisakhulupirire zithunzi zabodza zojambulidwa ndi omwe Sali a chisilamuzi ndipo tisakhulupirire adani a Chisilamu.

**‘hafaza’** (osunga zolemba). Malinga ndi ma lipoti ena , angelo a hafaza ndi osiyana ndi a kiraman katibin. Mngelo yemwe amakhala ku manja kwa munthu ndi wa pa mwamba kuyerekeza ndi wa kumanzere ndipo amalemba ntchito zabwino za munthu. Wa kumanzere amalemba ntchito zoipa. Pali angelo omwe adzazunze anthu osakhulupirira komanso asilamu osamvera akakalowa mmanda. Ndiye pali angelo ofunsa mafunso omwe amatchedwa ‘**munkar**’ ndi ‘**nakir**’. Angelo ofunsa mafunso asilamu amatchedwa ‘**mubashshir**’ ndi ‘**bashir’** (obweretsa uthenga wa bwino).

Angelo amasiyana mu ukulu ndi ulemerero wawo. Angelo apamwamba kwambiri ndi angelo akulu anayi. Wopamwamba kwambiri ndi mwa iwo ndi **Jubrail** alaihi-salam. Ntchito ya Jubrail inali yobweretsa **wahy** (vumbulutso la umulungu) kwa atumiki, ku dzawadziwitsa malamulo ndi zoletsedwa. Wachiwiri mwa iwo ndi **Israfil** alaihi-salam, yemwe adzalize lipenga lomaliza lotchedwa '**Su**r'. Israfil idzaliza Sur kawiri. Likadzalira lipenga loyamba chamoyo chilichonse chidzafa[1]. Lipenga lachiwiri chiririchonse chidzaukitsidwa. Wa chitatu ndi **Mikail** alaihi-salam. Ntchito yake ndi kulongosola ndondomeko ndi mayendedwe a zinthu monga chuma kuti katundu atsike kapena akwere mtengo, achuluke kapena achepe; kudzetsa chitonthozo ndi kumasuka komanso kuyendetsa chinthu chilichonse. Wachinayi ndi **Izrail** alaihi-salam, amene amachotsa ‘ruh’ (mzimu) kuchokera ku matupi la munthu. Pambuyo pa angelo anayi awa, pali magulu anayi a angelo apamwamba: Angelo anayi a **Hamalat al-Arsh**, omwe adzakhala asanu ndi atatu pa tsiku la kuuka kwa akufa; angelo a mu kukhalapo kwaumulungu, otchedwa ‘**muqarrabun**’; atsogoleri a angelo ozunza, otchedwa ‘**karubiyun**’; ndi angelo achifundo omwe amatchedwa '**ruhaniyun**'.

Angelo apa mwambawa alinso pa mwamba pa anthu kupatula Atumiki “alaihimus-salawatu wat-taslimat”. Ma Sulaha (Asilamu oopa Mulungu) ndi ma awliya (mchulukitso wa Wali, wokondedwa ndi Allahu Taala) mwa Asilamu ndi apamwamba mu ulemerero kuposa angelo wamba. Ndipo angelo wamba ndi apamwamba kuposa Asilamu wamba, omwe samvera ndi ochimwa. Koma anthu osakhulupirira ndi otsika ulemerero kuposa zolengedwa zonse.

Likadzalira lipenga loyamba, angelo onse kupatula Hamalat al-Arsh ndi angelo akulu anayi adzawonongedwa. Kenako Hamalat al-Arsh ndi angelo akulu anayi aja adzawonongedwanso. Lipenga likadzalira ka chiwiri, angelo onse adzaukitsidwa koma Hamalat al-Arsh ndi angelo akulu anayi aja adzaukitsidwa

[1] Chonde onani bukhu la ‘The Rising and the Hereafter’, lopezeka ku Hakikat Publications ku Istanbul, Turkey

lipenga la chiwiri lisanalire. Kusonyeza kuti angelo amenewa adzawonongedwa za moyo zonse zitaonongedwa, poti analengedwa zonse zisanalengedwe.

3 - Chachitatu mwa zinthu zisanu ndi chimodzi zofunika pa Iman (Nsichi yachitatu) ndi "**kukhulupirira mabuku ovumbulutsidwa ndi Allahu Taala** Iye anavumbulutsa mabuku amenewa kwa atumiki ena kudzera mwa mngelo Jubriel yemwe amkawawerengera. Atumiki ena analandira mabuku atalembedwa pa magome, monga Mussa; ndipo kwa atumiki ena amamva uthenga wawo posadzera mwa mngelo pakati. Mabuku onsewa ndi Mawu a Allahu Taala (Kalam- Allah). Ndi mau opanda chiyambi komanso opanda mapeto. Mauwa si chilengedwa. Si mawu opangidwa ndi angelo, kapena atumiki. Mau a Allahu Taala ndi osiyana ndi chilankhulo chomwe timalemba, kukumbukira ndi kulankhula. Alibe nthawi mu kulemba, kuyankhula kapena mmalingaliro. Alibe zilembo kapena kutchula. Munthu sangamvetse mmene Allah ndi zizindikiro zake zilili. Koma munthu atha kuwerenga ndi kusunga mu mtima ndi kuwalemba mauwo. Amakhala hadith (zolengedwa pambuyo pake), cholengedwa, akakhala ndi ife. Ndiko kuti, Mawu a Allahu Taala ili ndi mbali ziwiri. Akakhala ndi munthu ndi Hadith[1] ndi cholengedwa. Akaganiziridwa kuti ndi Mawu a Allahu Taala, amakhala amuyaya (kadim).

Mabuku onse omwe antumizidwa ndi Allahu Taala ndi olondola komanso owona. Mulibe bodza kapena cholakwika chilichonse mwa iwo. Zinanenedwa kuti ndikotheka Iye kudzakhululuka ngakhale ananena kuti adzalanga ndi kuzunza. Izi zitha kukhala chonchi chifukwa kukhululuka kumeneku ndikotengera zinthu zomwe sitingazimvetse ndi luntha lathu kapena mu chifuniro chake komanso kusankha kwake, Kapena zikutanthauza kuti azakhululuka chilango chomwe anthu akuyenera kulandira. Pakauti kulengeza kwa chilangochi ndi mazunzo ake sikukufotokoza za chinthu, silingakhale bodza Iye akakhululuka.

Ndikofunikira kufotokozera ma Ayah ndi Hadith m'matanthauzo ake enieni, pokhapokha ngati pali chopinga kapena chosokoneza. Ndi zosaloledwa kupereka matanthauzo ena ofanana ndi matanthauzo enieniwa.[2] Ma Ayah otchedwa **mutashabihat** ndi ovuta kuwamvetsa chifukwa ali ndi matanthauzo

[1] Hadith' kutanthauza chomwe kunalibe chisanalengedwe ndi Allahu Taala ndipo sichidzakhalapo Iye atafuna kuchiononga.

[2] Quran al-Karim ndi Hadith Sharifs zili mu chi Quraish (chiyankhulo cha Chiluya cha fuko la Muhamadi alaihi-salam). Koma mawuwo atandauzidwe molingana ndi gawo la Hijaz (chigawo cha Arabia Peninsula pa gombe la Red Sea komwe kuli Mecca ndi Madina) zaka 1400 zapitazo. Sizolondola kutanthauzira pogwiritsa ntchito matanthauzo amasiku ano, zomwe ndi zotsatira za kusintha kwa zaka mazana ambiri.

obisika. Allahu Taala yekha ndi amene akudziwa matandauzo ake. Komanso akuluakulu ochepa omwe apatsidwa al-ilm al-ladunni atha kuzindikira matanthauzo ake malinga ndi mmene Allah awalolera. (Al-ilm al-ladunni ndi kuzindikira kouziridwa ndi Allahu Taala m'mitima ya ma waliya).

Palibenso wina angawamvetse. Pa chifukwa ichi, tikuyenera kukhulupirira kuti ma ayah a mutashabihat ndi mawu a Allahu Taala, ndipo tisasake matanthuzo awo. Ophunzira a Madhhab a Ash'ari anati ndi kololedwa kufotokozera(tawil) ma ayah awa pang'ono kapena mwakuya. **Tawil** ikutanthauza kusankha tanthauzo la liu kuchokera pa matandauzo angapo aliulo lomwe siliri lotchuka kwambiri. Mwachitsanzo pa ayah **"dzanja la Allahu ndi loposa lawo,"** omwe ndi mawu a Allahu Taala , tiyenera kungonena kuti, "ndikhulupirira zirizonse zomwe Allahu Taala akutanthauza ponena izi." Ndi koyenera kwambiri kunena kuti "sindingamvetse tanthauzo lake. Allahu Taala yekha ndiyemwe akudziwa." Kapena titha kunena kuti 'Kudziwa kwa Allahu Taala sikuli ngati kudziwa kwa ife. Chifuniro chake sichili ngati chifuniro chathu. Chimodzimodzi dzanja lake siliri ngati dzanja la munthu wolengedwa.'

M'mabuku omwe Allahu Taala anavumbulutsa, ma ayah ena anasinthidwa **(naskh)** m'matchulidwe kapena m'matanthauzo komanso mwina mu zonse, m'matchulidwe ndi m'matanthauzo momwe. **Quran al-Karim** idalowa m'malo mwa Mabuku onse ndipo inathetsa malamulo a m'mabukuwa. Sipadzapezeka cholakwika, choonjezera, choiwalika kapena gawo losowa mu **Quran al-Karim** mpaka dziko lidzathe. **Qur'an al-Karim** ili ndi kudziwa zonse zakale ndi zonse za mtsogolo. Pachifukwa ichi, Qur'an al-Karim ndi ya pa mwamba komaso ndi ya phindu kuposa mabuku onse. Muujiza[1] (chozizwa) chachikulu kwambiri cha Mtumiki "swallaallaahu 'alayhi wa aalihi wa sallam" ndi **Quran al-Karim**. Ngakhale anthu onse ndi geni atasonkhana pa modzi ndi kuyesa kunena zofanana ndi sura yaifupi kwambiri ya **Qur'an al-Karim**, sangakwanitse. Ndipo zinachitikadi, akadaulo odziwa kupeka ndi kulakatula a ku Arabia anasonkhana ndi kuliyesetsa kwambiri, koma iwo analephera kulemba china chake chofanana ndi ayah imodzi yaifupi kwambiri mu Quran. Adalephera kupikisana ndi **Quran al-Karim**. Anaoneka opusa kumapeto kwake. Allahu Taala amapanga adani achisilamu kukhala wosatha ndi wogonja pamaso pa **Quran al-Karim**. Kumveka bwino kwa **Quran al-Karim** ndi kopambana mphamvu za munthu. Anthu sangathe kulakatula monga momwe Quran ikuchitira. Ma Ayah a mu Qur'an al-Karim Sali ngati ndakatulo, chimangirizo kapena ma vesi oyimbika alembedwa ndi anthu. Komabe, zinanenedwa m'zilembo za chinenero choyankhulidwa ndi anthu ophunzira a ku Arabia.

[1] Chozizwitsa cholengedwa ndi Allahu Taala kudzera mwa Mtumiki.

Chiwerengero cha mabuku omwe anavumbulutsidwa kwa munthu ndi 104. Ndi zodziwika kuti ma **suhuf**[1] (mabukhu ang'onoang'ono) 10 anavumbulutsidwa kwa Adam alaihi-salam; ma suhuf 50 kwa Shis kapena kuti **Sheth**[2] alaihi-salam; ma suhuf 30 kwa **Idris**[3] (Enock) alaihi-salam; ndipo ma suhuf 10 kwa **Ibrahim** (Abraham) alaihi-salam; **Tawrat** (Torah) inavumbulutsidwa kwa **Musa** (Moses) alaihi-salam; **Zabur** kwa **Dawud** (David) alaihi-salam; Injil kwa **Isa** (Jesus) alaihi-salam ndi **Quran al-Karim** kwa **Muhammad** alaihi-salam.

Munthu akufuna kulamula kapena kuletsa chinthu; kupempha chinachake kapena kunena nkhani, amayamba kuganiza ndi kukhonzekera m'maganizo. Kuphika kwa izi m'maganizo kumatchedwa "**kalam nafsi,"** komwe sitinganene kuti ndi chi arabu, Chichewa kapena Chingerezi. Kufotokozedwa kwawo zilankhulo zosiyanasiyana sikusintha tanthauzo ayi. Mau amene amatuluka kufotokoza zomwe zaphikidwa m'maganizo amatchedwa "**kalam lafzi**." Kalam lafzi itha kufotokozedwa m'zilankhulo zosiyanasiyana.

Choncho, kalam nafsi ya munthu ndi gwiro, yosasinthika, ndipo ndi yayokha yomwe imakhala mwa iye mwini yeka monga zizindikiro zina ngati luntha, chifuniro, kuzindikira, ndi zina zotero. Kalam lafzi ndi gulu la zilembo zomwe zimalongosola kalam nafsi ndipo imatuluka pakamwa pa munthu poziyankhula ndipo zimamveka m'makutu. Chimodzimodzi Mawu a Allahu Taala ndi amuyaya, osatha, omveka komanso osalengedwa omwe ali ndi Umunthu Wake. Ndi chizindikiro chosiyana ndi Sifat adh-Dhatiyya nkomanso kuchokera mu Sifat ath-Thubutiyya ya Allahu Taala, monga luntha ndi kufuna.

Chizindikiro cha Kalam (Kulankhula, Mawu) sichisintha ndipo ndi cha ngwiro. Sichili m'malembo kapena mawu. Sichinganenedwe kuti ndi lamulo, choletsa, nkhani kapena kuti ndi chiyankhulo cha Chiluya, Chichewa Arabic kaya Chi Turk. Sichitenga mitundu yotere. Sichingatheke Kulembedwa. Sichifuna zida kapena njira zofalisira ngati luntha, khutu kapena lilime. Chikhoza kunenedwa m'chilankhulo chilichonse chomwe mukufuna. Kotero, ngati chiperekedwa mu

[1] Gawo la zolemba za chipembedzo za Chisilamu. Zolemba zimenezi zimakhulupiriridwa kuti zinavumbulutsidwa kwa Abrahamu kuchokera kwa Mulungu, zomwe zinalembedwa ndi iyeyo pa modzi ndi alembi ndi otsatira ake.

[2] Seth sanatchulidwe dzina mu Qur'an koma ofotokoza a Chisilamu akunena kuti anali mwana wa Adamu ndi Hawa (Hava), amene anapatsidwa utumiki pambuyo pa Adamu, ndipo mabuku angapo ochokera kwa Mulungu anavumbulutsidwa kwa iye. Zolembedwa zimenezi zimanenedwa kuti ndi "Zolemba zoyamba" kutchulidwa mu Quran sura 87 vesi 18.

[3] Idris -mneneri yemwe watchulidwa mu Qurai, yemwe Asilamu tiamakhulupirira kuti anali mneneri wachitatu pambuyo pa Sheti. Iye ndi mneneri wachiwiri kutchulidwa mu Quran.

Arabic chimatchedwa **Quran al-Karim**. Ngati zifotokozedwa m'Chi Heberi ndi Torat. Ngati linenedwa m'Chisiriya ndi Injil. [Zalembedwa m'buku lotchedwa Sharh al-maqasid, lolembedwa ndi Saduddin Taftazani, yemwe anamwalirira ku Samarkand mu 1389/792, kuti mawuwa m'Chigiriki Ndi Injil, ndipo m'Chisiriya ndi Zaburi.]

Kalam al-Ilahiyya (Mawu a Allahu Taala) amanena maphunziro osiyanasiyana; ngati mauwa akufotokoza zomwe zinachitika kapena zomwe zidzachitike, amatchedwa **khabar** (Zolongosola); ngati sichoncho, amatchedwa **insha**. Ngati akunena za zinthu zimene ziyenera kuchitika, amatchedwa **amr** (lamulo). Ngati akunena zoletsedwa, ndi **Nahy** (zoletsedwa). Koma palibe kusintha kapena kuwonjezeka komwe kumachitika mu Kalam al-Ilahiyya. Mabuku onse ndi masamba onse anavumbulutsidwa ndi ochokera m'chizindikiro cha Khalidwe la Kalam ya Allahu Taala; Kutanthauza kuti, ndi Kalam an-Nafsi Yake, ndipo mu Chiarabu ndi **Quran al-Karim**.

Wahy (zivumbulutso za Allahu Taala) zotumizidwa ngati ndime za ndakatulo ndipo zitha kulembedwa zilembo ndi kunena ndi kumveka komanso ndikusungidwa m'maganizo zimatchedwa Kalam al-Lafzi kapena **Quran al-Karim.** Poti Kalam al-Lafzi imakamba za Kalam an-Nafsi, ndikololedwa kuyitcha Kalam al-Ilahiyya kapena chizindikiro chopatulika. Poti mau ake onse amatchedwa **Quran al-Karim**, zigawo zakenso zimatchedwa **Quran al-Karim**.

Akatswiri ophunzira a njira yowongoka amagwirizana kuti za Kalam an-Nafsi si cholengedwa ndipo ndi yamuyaya. Koma palibe kuvomerezana zoti Kalam al-Lafzi inalengedwa kapena kuti ndi yamuyaya. Omwe amatenga Kalam al-Lafzi ngati cholengedwa anachenjeza kuti ndi bwino osanena kuti inalengedwa, chifukwa kutero kutanthauza kuti Kalam an-Nafsi ndi cholengedwa. Iyi ndi ndemanga yabwino pa nkhaniyi. Munthu akamva chinachake chomwe chikutanthauza kanthu, amakumbukira za tanthauzolo. Ophunzira Ahl as-Sunna omwe ananena kuti Quran al-Karim inalengedwa ankatanthauza kumveka ndi mawu omwe timayankhula ndi pakamwa. Ophunzira a Ahl as-Sunna anavomerezana kuti Kalam an-Nafsi ndi Kalam al-Lafzi ndi Mawu a Allahu Taala. Ngakhale kuti ophunzira ena amatenga ganizoli ngati chiyerekezo, zoti Kalam an-Nafsi ndi Mawu a Allahu Taala zitanthauza kuti ndi chizindikiro cha kuyankhula kwa Allahu Taala; ndipo zoti Kalam al-Lafzi ndi Mawu a Allahu Taala zikutanthauza kuti Allahu Taala ndiye adawalenga.

**Funso:** "Kuchokera mu zomwe zolembedwa m'mwambazi, zikumveka kuti Mawu a muyaya a Allahu Taala sangamveke. Kunena kuti, 'ndamva mawu Allahu Taala,' zikutanthauza kuti 'ndamva mawu akuyankhulidwa' kapena 'ndamvetsetsa mawu akuyankhulidwa ndi Kalam an-Nafsi yamuyaya.' Atumiki

onse komanso aliyense angathe kumva mu njira ziwirizi. Ndi chifukwa chiyani timatenga Musa alaihi-salam ngati **Kalim-Allah** (yemwe Allahu Taala adayankhula naye)?"

**Yankho:** Musa alaihi-salam adamva mawu amuyaya popanda zilembo mosiyana ndi mmene zimachitikira ndi opatulika ena. Iye anamva mu njira yomwe siyingafotokozeke, ngati momwe sitingate kufotokozera ndi kumvetsa momwe Allahu Taala akaonekere ku Mparadizo. Palibenso wina anamvako ngati mmene Musa alaihi-salam anamvera. Iyeyi anamva Mawu a Allahu Taala osati kudzera mmakutu ake okha, koma kudzera mu chilichonse cha thupi lake kuchokera ku mbali zonse. Kapena anamva kuchokera ku mbali yomwe kunali mtengo, koma osati kudzera mu mawu kapena mphepo kapena njira zina. Chifukwa choti anamva podzera mu imodzi mwa njira zitatuzi, Iye analemekezedwa ndi dzina loti 'Kalim-Allah'. Muhammad alaihi-salam naye anamva Mawu A Mulungu mnjira imeneyi mu usiku wa Mi'raj. Chimodzimodzinso kumva kwa Jebrail alaihi-salam mmene ankalandira **wahy**.

4 - Nsichi ya chinayi ya Iman ndi **"kukulupirira mwa aneneri omwe anatumizidwa ndi Allahu Taala**" kuti kulondolera anthu ku njira yakondeka ndi Allahu Taala. 'Rusul' (mmodzi) rasul (ambiri) anali 'anthu otumidwa, atumiki.' Mu Chisilamu, '**rasul'** amatanthauza 'wolemekezeka' munthu waulemu wake yemwe chibadwidwe chake,khalidwe lake, nzeru zake ndi kuzindikira kwake nkoposa wina aliyense mu nthawi yake ndipo yemwe alibe mchitidwe woyipa ngakhale khalidwe losasangalatsa.' Atumiki anali ndi makhalidwe a **isma**; ndiko kuti sanachimwepo asadapatsidwe utumiki ngakhale atapatsidwa utumiki wawo[1]. Pa nthawi yao yonse kuyambira pomwe anauzidwa za utumiki mpaka pomwe utumiki wao unadziwika ndi kufalikira, iwo sanakhalepo ndi ulumali uliwonse monga khungu, kusamva ndi zina zotero. Zikuyenera kukhulupiridwa kuti mtumiki aliyense anali ndi zinthu zisanu ndi ziwiri (7) izi: **amana** (kukhulupiririka), **sidq** (kudzipereka), **tabligh** (kupereka malamulo ndi kuitanira anthu ku chipembedzo cha Allahu Taala), **adala** (chilungamo), **isma** (kusachimwa), **fatana** (nzeru zakuya) ndi **amn al-azl** (chitetezo (chitetezo choti sangachotsedwe pa utumiki).

Mtumiki yemwe anabweretsa chipembedzo chatsopano (dongosolo la malamulo a miyambo) amatchedwa **"rasul"**, ndipo yemwe sanabweretse chipembedzo chatsopano koma kungoitanira anthu ku zipembedzo zakale

[1] Anthu ena osakhulupirira ena omwe amayesetsa kuononga Chisilamu ndi chinyengo amati: "Mtumiki, Muhammad alaihi-salam asanakhale mtumika amkapereka nsembe ya nyama kwa mafano" ndipo amapereka umboni wochokera mmabuku a anrhu opanda madhhabi. Ndime yomwe tangowerengayi ikuchitira umboni kuti izi ndi za bodza.

amatchedwa **“nabi”** [mau oti ‘mneneri’ ndi ‘Mumiki’ amagwiritsidwa ntchito kwa onsei.] Palibe kusiyana pakati pa iwo m’maperekedwa a malamulo ndi m’kuitanidwire ka anthu ku chipembedzo cha Allahu Taala. Tiyenera kukhulupilira, popanda kupatula kuti aneneri onse anali odzipereka ndi oona. Amene akukanira m’modzi wa iwo amatengedwa ngati wakana onse.

Munthu sangalandire Uneneri (Nubuwwa) chifukwa chogwira ntchito molimbika, kuvutika ndi njala kapena kusowa mtendere, kapena kupembedza kwambiri. Umaperekedwa kwa okhawo omwe Allahu Taala wa konda ndi kuwasankha. Zipembedzo zinatumizidwa kudzera mwa aneneri kuti akonze moyo wopindulitsa wa anthu m’dziko lino komanso m’dziko lotsatira ndi kuwatetedza ku zoipa kuti kupeze chipulumutso, njira yabwino, mtendere ndi chisangalalo. Ngakhale kuti anali ndi adani ambiri ndipo ankanyozedwa ndi kuchitiridwa nhanza ndi chipongwe, aneneri sanaope adaniwa ndipo sanazengereze kuuza anthu malamulo a Allahu Taala pa chikhulupiriro ndi machitidwe. Allahu Taala ankawathandiza aneneriwa ndi muujizas (zozizwitsa) kusonyeza kuti anali odzipereka ndi oona. Palibe amatha kutsutsa zozizwitsa zawo. Anthu amene amatsatira Mneneri amatchedwa '**umma**' wa mneneri ameneyo. Pa tsiku la chiweruzo Aneneri adzaloledwa kupemphera chikhululuko Uma wawo, makamaka kwa amene anachita matchimo akulu, ndipo mapemphero awo adzalandiridwa. Allahu Taala adzalolanso ma Ulama, Swlaha ndi ma awliya omwe anali pakati anthu kuti awapemphere anthu awo chikhululuko, ndipo mapemphero awo adzavomerezedwa. Aneneri “alaihimus-salawatu wat-taslimat” ali moyo m’manda mwawo, m’moyo womwe sitingathe kuudziwa; nthaka siyiwoletsa matupi awo odalitsika. Pa chifukwa ichi, Hadith sharif inanenedwa kuti: "**Aneneri amaswali ndi kuchita Haji m'manda mwawo**."[1]

---

[1] Makono, anthu otchedwa ‘Wahhabi’ ku Arabia samakhulupirira Hadith ngati iyi. Iwo amawatcha Asilamu owona amene amakhulupirira ma Hadith ngati iyi kuti ndi “osakhulupirira”. Chifukwa cha kutanthauzira kwawo molakwika ndi mosamveka bwino kwa ma Ayat ndi ma Hadith amenewo, iwo sakhala gulu la okhulupirira koma amakhala anthu a bidah. Iwo amawononga kwambiri Asilamu. Wahhabism inayambitsidwa ndi mbuli yomwe dzina lake ndi Muhammad bin Abd al-Wahhab wadela la Najd ku Arabia. Kazitape waku Britain wotchedwa Hemphera, ndi amene anamusocheretsa iye pogwiritsa ntchito maganizo a munthu wopatuka, Ahmad Ibn Taymiyya yemwe anamwalira ku Damasiko mchaka cha 1328/728. Wahhabism Inafalikira pakati pa anthu a ku Turkey ndi kwina kudzera m'mabuku a munthu waku Eguputu wotchedwa Muhammad Abduh yemwe anamwalira ku Egypt mchaka cha 1905/1323. Akatswiri a chipembedzo a Ahl as-Sunna anatsimikizira m’mabuku awo ambiri kuti Wahhabism si madhhab a chisanu ndipo kuti ma Wahhabi ndi anthu ampatuko otsatira Njira yolakwika. Zambiri za izi zalembedwa m'mabuku athu a **Endless Bliss**, **Confessions of a British Spy**,

Pamene maso odalitsika a mneneri akugona, diso la mtima wake siligona. Aneneri onse alaihimus-salam anali ofanana pa ka gwiridwe ka ntchito monga aneneri komanso pa ungwiro wawo wa Uneneri. Zinthu zisanu ndi ziwiri zomwe tatchula pa mwambazo zinalipo mwa Aneneri onse. Aneneri sanachotsedwe Uneneri. Awliya atha kulandidwa wu Awliya, (ulemu okhala wali, wokondedwa ndi Allahu Taala). Aneneri anali anthu, osati mizimu kapena angelo, omwe sangakhale Aneneri a anthu kapena kupeza ulemerero wa Mneneri.

Aneneri anali ndi kupambana komanso ulemo mosiyana. Mwachitsanzo, kupambana m'njira ya kuchuluka kwa umah omutsatira komanso kukula kwa dera lotumikira; kafalitsidwe ka nzeru ndi kudziwa kwake ndi momwe anauzira mmitima mwa awliya za dhat ndi Sifat ya Allahu Taala Kuchuluka kwa zozizwitsa zake ndikukhala zopitilira kugwira ntchito; ndi kupatsidwa mphatso ndi madalitso apadera. Mtumiki wa m'badwo waposachedwa, **Muhammad** alaihi-salam, anali wapambana kuposa Aneneri ena onse. Aneneri otchedwa 'Ulul-azm' anali apamwamba kuposa ena. Ma Rasul anali apamwamba kuposa ma nabis omwe sanali ma rasul.

Chiwerengero cha aneneri alaihimus-salam sichidziwika. Zimadziwika kuti anali oposa 124,000. Mwa iwo, 313 kapena 315 anali ma rasul ndipo a zisanu ndi chimodzi olemekezeka pakati pawo, otchedwa '**Ulul-azm**', anali: **Adam**, **Nuh** (Nowa), **Ibrahim** (Abraham), **Musa** (Moses), **Isa** (Yesu) ndi **Muhammad Mustafa** alaihimus-salatu was-salam.

Aneneri makumi atatu ndi mphamba zitatu (33) otsatirawa ndi odziwika bwino lomwe: **Adam**, **Idris** (Enoch), **Sheth** (Shis), **Nuh** (Nowa), **Hud** (Heber), **Salih** (Methusaleh), **Ibrahim** (Abraham), **Lut** (Loti), **Ismail** (Ishmael), **Ishaq** (Isaac), **Yaqub** (Jacob), **Yusuf** (Joseph), **Ayyub** (Yobu), **Shuaib** (Jethro), **Musa** (Moses), **Harun** (Aaron), **Khidir**, **Yusha ibn Nun** (Joshua), **Ilyas** (Elias), **Alyasa** (Elisha), **Dhul-kifl** (Ezekiel), **Shamun**, **Ishmoil** (Ismail), **Yunus ibn Mata** (Yonah), **Dawud** (David), **Sulaiman** (Solomon), **Luqman, Zakariyya** (Zachariah), **Yahya** (John the Baptist), **Uzair** (Ezra), **Isa ibn Mariam** (Yesu), **Dhul-qarnayn** (Zulqarnayn) and **Muhammad** alaihimus-salatu was-salam.

Mayina a Aneneri 28 okha ndi omwe alembedwa mu **Quran al-Karim**. Sheth, Khidir, Yusha, Shamun ndi Ishmoil sadalembedwe. Sidzikudziwika bwino bwino ngati Dhul-qarnain, Luqman ndi Uzair anali Aneneri kapena ayi. Monga zalembedwera mu kalata ya 36 mu bukhu lachiwiri la **Maktubat** la M. Mathum,

---

ndi **Advice for the Muslim**. Tipemphe Allahu Taala kuti ateteze achinyamata omwe akutumikira Chipembedzo chao kuti asagwere mu Wahhabism, yomwe inakhazikitsidwa ndi ma British! Atitetedze kuti tisapatuke ku njira ya akatswiri a Ahl as-Sunna, amene amayamikiridwa mu Hadith zambiri!

malipoti oti Khidir alaihi-salam anali Mneneri anali owona. Ndipo mu kalata ya 182 zalembedwa kuti, “kupezeka kwa Khidir alaihi-salam ngati munthu ndikumachita zinthu zina sizionetsa kuti iyeyo ali moyo. Allahu Taala wawupatsa mzimu wa Khidir alaihi-salam ndi mizimu ya Aneneri ena komanso ma wali chilolezo chobwera ndi kuoneka ngati munthu. Kutha kuwaona iwo sizisonyeza kuti ali moyo. ”Dhul-kifl alaihi-salam ankatchedwanso ‘Harqil’, yemwenso ankatchulidwa kuti Ilyas, Idrisa kapena Zakariyya.

Ibrahim alaihi-salam anali Khalil-Allah[1], chifukwa mu mtima mwake munalibe chikondi cha cholengedwa china chirichonse koma Allahu Taala yekha. Musa alaihi-salam anali Kalim-Allah[2], chifukwa anayankhula ndi Allahu Taala. Isa alaihi-salam anali Kalimat-Allah[3], chifukwa analibe bambo ndipo anabadwa ponena Mawu al-Kalimat al-Ilahiyya (mau opatulika). ‘Chikhale’ ndipo chinakhaladi!’ Komanso ankalalikira mawu a Allahu Taala, omwe anali ndi mzeru za Umulungu ndipo ankawanena ku ma kutu a anthu.

**Muhammad** alaihi-salam , ndi Habiballah (Wokondedwa wa Allahu Taala). Zolengedwa zonse zinalengedwara chifukwa cha Iye ndipo ndi wa pamwamba kuposa zolengedwa zonse. Ndi wolemekezeka pa anthu onse. Pali umboni wochuluka wosonyeza kuti iye anali wa pamwamba kwambiri ndipo Allah ankamukonda kwambiri. Pa chifukwa ichi mawu onga adagonjetsedwa, sanganenedwe pokhudza Iye. Pa tsiku la chiweruzo adzauka kwa kufa wina aliyense asanauke. Adzakhala woyamba kupita ku bwalo la chiweruzo. Akayambiriranso kukalowa ku Mparadizo. Zozizwitsa zomwe ankapanga ndi zosawerengeka, tidzakometsera zolemba zathu pofotokoza zozizwitsa za **Mi’raj:**

Rasulullah alaihi-salam akugona ku al-Makkat alMukarrama mu Mecca, malo obadwira a mtumiki Muhammad ‘alaihisalam, mzinda wopatulika wa Asilamu, anadzutsidwa ndipo thupi lake linatengedwa mpaka kukafika ku mzikiti wa Aqsa ku Jerusalem **(Quds).** Kenaka anakwera kumwamba, ndipo atadutsa thambo wa 7 anafika ku malo komwe Allahu Taala anamutengera.

[1] Mnzake wa Allah.

[2] Yemwe anayankhula ndi Allah. Musa (as) anali Mneneri wamkulu wa Allah. Allah anamkonda kwambiri Musa (as) ndipo wamutchula iye m’Qur’an kuposa Mtumiki wina aliyense. Ndipo Mulungu adalankhulanso ndi Musa (as) mwachindunji, womwe ndi ulemu waukulu. Chifukwa cha ichi Musa (as) amadziwikanso kuti 'Kalim-Allah,' kutanthauza 'amene Mulungu walankhula naye’.

[3] Liu la Allah. Analibe bambo ndipo anabadwa Allah atangonena Liu lot ‘Chikhale’ ndipo chinakhala.

Tikuyenera kukhulupirira za Miraj m'njira imeneyi.[1] Iye ndi mngelo Gabriel anachoka ku Mecca ndi kukafika pa **Sidrat al-muntaha**, mtengo womwe uli pa thambo la 6 ndi la 7. Palibe chomwe chimapitirira apa kukwera. Mu Sidra, Rasulullah alaihi-salam anaona Gabrieli alaihi-salam m'maonekedwe ake enieni ali ndi mapiko okwana 600. Gabrieli alaihi-salam anatsala mu Sidra. Pa ulendo umenewu, Kuchokera ku Mecca kukafika ku Jerusalem, ndi kukwera ku mitambo, Rasulullah alaihi-salam ankwera chinyama chotchedwa **Buraq**,**.** Buraq ndi nyama **y**oyera**,** yothamanga kwambiri. Siyayimuna kapena yayikazi, ndipo siya pa dziko la pansi koma ndi ya ku Mparadizo, yooneka ngati bulu**.** Pa mzikiti **wa Aqsa**, Rasulullah alaihi-salam anaswali pa jamaah ndi aneneri ena, ndipo Rasulullah anali imam wotsogolera Swalah imeneyi. Lidali pemphero la usiku kapena la mbandakucha. Allah analola Mizimu ya aneneri kuoneka mu thupi lawo. Kuchokera ku Jerusalem kukafika ku thambo la 7 anakwezedwa ndi makwerero otchedwa **Miraj**. Mu njira yonse angelo anandanda mbali zonse ku manja komanso ku manzere ndipo amantamanda ndi kumuyamikira Iye. Pa thambo uliwonse, Jebrail alaihi-salam ankaulutsa kufika kwa Rasulullah alaihi-salam Pa thambo uliwonse anaona Mneneri ndipo anali kumupatsa salam. Ku Sidra, anaona zinthu zodabwitsa zambiri.

Anaona Madalitso aku Mparadizo komanso mavuto a ku Gahena. Iye sanayang'ane chirichonse pa madalitso a ku mParadiso mwakufuna kutero koma chifukwa cha chisangalalo choona Jamal (kukongola) kwa Allahu Taala Kupsyola mu Sidra, anapitirira yekha ndipo ankadutsa mu kuwala. Ankamva phokoso la zolembera za angelo. Anadutsa ma katani 70,000. Mtunda wochokera pa katani limodzi kufika pa lina unali ngati zaka 500. Kenako Rasulullah alaihi-salam anawona kuti **Rafraf** (bedi la silika) lobiriwira kwambiri laphimba m'mphepete mwake. Rasulullah alaihi-salam anakhala pa Rafraf ndipo Jebrail alaihi-salam anamusiya Mtumiki pamenepo. Andadutsa pa **Kursi** (mbali ya mitambo yomwe ndi kunja kwa ntambo womaliza ndipo mkati mwa **Arsh** komwe ndi kumapeto kwa mitambo). Anafika pa malo opatulika. Anakwezedwa kupsyola Arsh, ndi kuyandikira kwa Mbuye wake, komwe anamva Allahu Taala.

Anaona Allahu Taala mu njira yomwe siyingafotokozeke komanso kumvetsetseka, ngati mmene azaonedwere mu moyo omwe uli nkudza

[1] Ismaili ndi adani a Chisilamu, opatuka omwe amanyengezera kuti ndi akatswiri a Chisilamu ndikumayesetsa kunyenga achinyamata ponena ndi kulemba kuti Mi'raj sikunali kukwera ndi thupi koma mu uzimu (hal). Tisagule mabuku achinyengo amenewa; tisawalole kutinyenga. Momwe Mi'raj inachitikira zalembedwa mwatsatanetsatane m'mabuku ambiri ofunika, mwachitsanzo mu Shifa-i sharif lolembedwa ndi Qadi Iyad al-Maliki, yemwe anamwalirira ku Morocco mu 1150/544 ndi Endless Bliss.

popanda nthawi ndi malo. Adayankhula ndi Allahu Taala popanda zilembo kapena mawu. Iye adapembeza ndi kumukweza Allahu Taala Anapatsidwa mphatso ndi ma ulemu osawerengeka. Iye ndi Umah wake unalamulidwa kuswali zipindi 50 pa tsiku lirilonse, koma izi zinachepetsedwa pang'onopang'ono mpaka kufika pa zipindi zisanu patsiku. Izi zinatheka mothandizidwa ndi Musa alaihi-salam. Poyamba anthu ankaswali mmawa, masana kapena usiku. Pakutha pa ulendo wa utaliwu, atapatsidwa mphatso ndi madalitso osiyanasiyana komanso atamva ndi kuona zinthu zodabwitsa zambiri, anabwerera pa bedi lake lomwe linali dakafunda. Zomwe talemba apa mbali ina ndi zochokera mu ma ayah koma zina zochokera m'ma hadith. Si wajib kukhulupirira chirichonse. Koma poti ophunzira a Ahl as-Sunna adafotokoza izi, kuzikana ndiye kuti kuzipatula mu Ahl as-Sunna. Anthu osakhulupirira ma ayah kapena ma hadith amakhala wosakhulupirira.

Tiyeni tinene ma umboni ena osaonyeza kuti Muhammad alaihi-salam anali mtumiki wamkulu **(Sayyid alAnbiya).**

Pa tsiku la chiweruzo Aneneri onse adzakhala pa mthunzi wa dzina lake. Allahu Taala analamula Aneneri onse kuti akadzakhala ndi moyo mpaka nthawi ya Muhammad alaihi-salam, yemwe ndi wokondedwa wa Allahu Taala kuposa zolengedwa zonse, Aneneriwa adzamukhulupirira ndi kukhala athandizi ake. Ndipo Aneneri onse ankawauza umah wawo zomwezi m'mawu awo omaliza.

Muhammad alaihi-salam anali **Khatam al-Anbiya** (mtumiki womaliza); kunena kuti palibe mtumiki wina adzabwere atamwalira Iye. Mzimu wake wodalitsika unalengedwa aneneri onse asanalengedwe. Ulemerero wa Uneneri unayamba kuperekedwa kwa Iye. Uneneri unamalizidwa ndi kubwera kwake pa dziko. Dziko likadzatsala pang'ono kutha, mu nthawi ya Hazrat al-Mahdi, Isa alaihi-salam adzatsika kuchokera kumwamba kukafikira ku Damascus ndipo adzathandizira kufalitsa uthenga wa Muhammad alaihi-salam ndi Chisilamu.

[Kagulu kena kabodza ka ma **Qadiani**' kapena' **Ahmadis**' kanakhonzedwa ndi ma British ku India m'chaka cha 1880/1296. Kaguluka kamanena bodza pa zokhudza Isa alaihi-salam. Ngakhale amanamizira kuti ndi Asilamu , amayesetsa kuwononga Chisilamu kuchokera mkati. Fatwa (chigamulo chomwe chimapangidwa ndi Asilamu ophunzira za chipembezo pa nkhani zokhudza Chisilamu) inaperekedwa yonena kuti ma **Qadiani**' sanali Asilamu.

Gulu lina la ma zindiq lomwe likazikitsidwa ku India ndi gulu lotchedwa **Jamaat at-tablighiyya** (kapena **Tabligh Jamaah**). Gululi linayambitsidwa mu chaka cha 1926/1345 ndi mbuli ina yotchedwa Ilyas. Iye ankanena kuti Asilamu "asiya njira yoonadi ya Chisilamu, ndipo kuti iye analota atalamulidwa kuti ateteze Asilamuwa kuti asasochere." Ankalalikira zomwe anaphunzira

kuchokera m'mabuku a atsogoleri ake opatukawa omwe ndi Nezir Husayn, Rashid Ahmad Kankuhi ndi Khalil Ahmad Seharanpuri. Pofuna kupusitsa Asilamu, nthawi zonse amanena za kufunika kwa Swalah ndi jamaah. Koma palibe Swalah kapena zochita zawo zopembedza zomwe zimavomerezeka chifukwa iwo ndi gulu la ahl al-bida (ogalukira). Iwo anali kunja kwa chiphunzitso cholondola cha Ahl as-Sunna. Choyamba choti iwowa achite ndi kuwerenga mabuku olondola olembedwa ndi akatswiri a chipembedzo a za Ahl as-Sunna, kuti adzipulumutse ku zikhulupiriro zopatukazo ndi kukhala asilamu enieni. Anthu amene amatanthauzira ma ayah molakwika ndi matanthauzo obisika mu **Quran al-Karim** amatchedwa anthu a bidah, kapena opatuka. Adani a Chisilamu omwe amatanthauzira ma ayah molingana ndi maganizo awo ndi ma zindiq omwe akuyetsetsa kusintha **Quran al-Karim** komanso Chisilamu. Magulu amenewa amayambitsidwa, kuthandizidwa ndi kulandira ndalama kuchokera kwa ma British, mdani wamkulu wa Chisilamu kuti afalitse zabodzazi. Ma membala a Tabligh Jamaa, omwe ndi mbuli zomwe zagwera mu msampha wa ma British osakhulupirira, akuyesetsa kupusitsa Asilamu podzitchula kuti iwo ndi 'Ahl as-Sunna', kuswali ndi kunena mabodza. Ena mwa iwo, atavala nduwira za zikulu ngati zisa za adokowe[1], zomangidwa pa mwamba pa ma minaret, osunga ndevu ndi kuvala mikanjo yayitali, amasoma Quran ndi kutanthauzira molakwika ndi cholinga chonyenga Asilamu.Koma hadith sharif ikunena kuti "**Allahu Taala amakuweruzani osati kamba ka mavalidwe koma zomwe zili mmitima yanu ndi zolinga zanu**. "

Chifukwa choti iwowo amalephera kuyankhapo pa mabuku athu a Hakikat Publishing, amati "mabuku otsindikizidwa ndi Hakikati ndi mabuku a anthu opatuka komanso abodza. Musawawerenge". Chizindikiro chosonyeza kuti anthu awa ndi opatuka ndi okanira ndipo ndi adani a Chisilamu ndi zoyankhula zao zoti "zolemba za ophunzira a Ahl as-Sunna ndi zabodza" komanso mabukhu omwe amafalitsa ndi cholinga choti anthu asamawerenge zolembazi za akatswiri a a Ahl as-Sunna. Bukhu lathu la chi Turkish, **Faideli Bilgiler** likufotokoza za zoipa zomwe anthu awa achitira Chisilamu ndipo likupereka mayankho omwe akatswiri a Ahl as-Sunna apereka pa nkhaniyi.]

Muhammad "salallahu alaihi-wasalam" ndi wapamwamba mwa Aneneri onse ndipo ndi chifundo cha Allahu Taala ku zolengedwa zonse. Zolengedwa za mmaiko 18,000 zimalandira madalitso kuchokera ku nyanja ya madalitso ake. Iye ndi mtumiki wa anthu ndi ma jinni onse. Ma lipoti ambiri amanena kuti iye ndi mtumiki wa angelo, zomera , nyama ndi china chilichonse. Pomwe Atumiki

[1] Dokowe ndi mbalame yayikulu, yamiyendo yaitali, khosi lalitali yokhala ndi milomo yayitali yolimba.

ena anatumizidwa kwa mitundu ina yokha, Muhammad “salallahu alaihi-wasalam” anatumizidwa kwa mitundu yonse ya anthu ndi zolengedwa zonse za moyo ndi zopanda moyo. Allahu Taala ankawayitana atumiki ena ndi maina awo. Koma Muhammad alaihi-salam ankakonderedwa ndi kuitanidwa kuti ‘Oh Mtumiki wanga!’ Zozizwitsa zomwe zinaperekedwa kwa atumiki ena onse zinaperekedwanso kwa iye. Allahu Taala anampatsa Mtumikiyu mphatso zambiri ndipo analoledwa kuchita zozizwitsa zambiri kuposera aneneri onse. Anapangidwa kukhala wa pamwamba mwa Aneneri onse ndi ma ulemu osiyanasiyana: mwezi umagawikana pakati Iye akapanga chizindikiro ndi chala chake chodalitsika; miyala akayitenga mmanja mwake inkatchula dzina la Allah; mitengo inkamulonjera ponena kuti, “Oh Rasulullah”; Ndodo yotchedwa Hannana inalira Rasulullah alaihi-salam atayisiya; madzi oyera ankatuluka pakati pa zala zake zodalitsika. Ndipo zinthu za pa mwamba izi zikapatsidwa kwa iye mu dziko lomwe lili nkudza: al-Maqam al-Mahmud (kuyamikiridwa ndi Ulemerero), ashShafa’at al-kubra (kutha kupemphera ena chikhululuko) al-Hawd al-Kawthar (woyera ngati dziwe loyera ngati mkaka lodzadza ndi ubwino lomwe liri ku Mparadizo pomwe umma wa Rasulullah alaihis-salam ukasonkhane pa tsiku lachiweruzo; al-Wasila (njira yoyandikira kwa Allah) ndi al-Fadila (makhalidwe abwino)**.** Anapatsidwa ulemerero woona kukongola kwa Allahu Taala asanakalowe ku Mparadizo (pa ulendo wa Mi’raj]). Anali wa makhalidwe abwino kwambiri kuposa aliyense pa dziko: wachikhulupiriro chopanda vuto, nzeru, kudekha, kuleza, kuyamika, zuhd (wosalabadira za mdziko), wodzisunga, wachilungamo, ungwazi, wolimba mtima, wa ulemu, wodziwa zinthu, wodzichepetsa, wothandiza, wachisoni ndi zina zabwino zambiri. Allahu Taala yekha ndi amene akudziwa kuchuluka kwa zozizwitsa zomwe iye anapatsidwa. Chipembezo chake ndi cha pamwamba mwa zipembezo zonse. Umma wake ndi wopambana kuposa ma umma onse. Ma awliya a umma wake ndi apamwamba kuposa ma awliya ama umma onse.

Mwa ma awliya a umma wake, yemwe anayenera kukhala Khalifa (Mtsogoleri) pambuyo pake ndi Abu Bakr as-Siddiq “radiyallahu taala anh”. Iye ankakondedwa ndi ma awliya komanso ma imam ndipo anali oyenera pa utsogoleriwu kuposa wina aliyense. Pambuyo pa Aneneri, Abu Bakr as-Siddiq “radiyallahu taala anh” ndi munthu wa pamwamba yemwe anabwera ndipo sikudzabweranso wina wonga ngati iyeyu. Iye anali woyamba kupatsidwa ulemerero wa Khalifaate. Chifukwa cha kukonderedwa ndi kudalitsidwa

kuchokera kwa Allahu Taala, iyeyu sanapembezepo mafano ngakhale Chisilamu chisanafike. Anatetezedwa ku kuperewera kwa chikhulupiriro ndi mabodza.[1]

**Abu Bakr as-Siddiq** "radiyallahu taala anh" atamwalira, wa pamwamba wotsatira ndikukhala Khalifa wa chiwiri anali **Umar ibn al-Khattab** "radiyallahu taala anh", yemwe anasankhidwa ndi Allahu Taala kukhala mnzake wa mtumiki wokondeka Muhammad alaihi-salam.

Wachitatu wa pamwamba pakati pa anthu ndi **Dhun-Nurain Uthman ibn Affan** "radiyallahu taala anh", wolemera ndi kukonderedwa ndi kudalitsidwa, gwero la kudzichepetsa, chikhulupiriro komanso nzeru za uzimu.

Atamwalira Uthman ibn Affan "radiyallahu taala anh", wapamwamba kwambiri Khalifa wa chinayi **Ali ibn Abi Talib** "radiyallahu taala anh". Iye anali mwini wa zinthu zodabwitsa kwambiri komanso 'Mkango' wa Allahu Taala.

Pambuyo pa Ali ibn Abi Talib "radiyallahu taala anh", pali Hazrat **Hasan ibn Ali** "radiyallahu taala anh"um. Iye anakhala Khalifa koma adaphedwa ndi poizoni ku al-Madinat a-Munawwara mu chaka cha 669/49. Iye ndi Khalifaate wotsiria mu zaka 30 za u Khalifaate zomwe zatchulidwa mu Hadith Sharif. Pambuyo pa iye wa pamwamba wina ndi Hazrat **Husayn ibn Ali** "radiyallahu taala anh" um, nyali ya maso a Rasulullah alaihi-salam.

Kupambana kwao kumatengera kuchuluka kwa thawab zomwe amapeza; kusiya dziko lawo ndi ma banja awo chifukwa cha Chisilamu; kukhala oyamba kulowa Chisilamu ena asadalowe; kutsata kwambiri zochita za Rasulullah alaihi-salam; kutsatira sunna yake mosamalitsa; kuvutika pofalitsa Chisilamu ndi kupewa kusakhulupirira, zipolowe ndi kufuntha.

Hazrat Ali "radiyallahu anh "anali woyambirira kulowa Chisilamu mwa onse kupatula Hazrat Abu Bakr "radiyallahu anh "Koma anali mwana, wopanda chuma ndipo ankakhala m'nyumba ya Rasulullah alaihi-salam ngati wa ntchito wake. Choncho, kulowa kwake m'Chisilamu sikunasinthe anthu osakhulupirira kuti alowe Chisilamu. Koma kulowa Chisilamu kwa ma Khalifa ena atatu aja kunalimbikitsa Chisilamu. Chifukwa choti Hazrat Ali ndi ana ake radiyAllahu Taala anhum anali achibale a magazi a Rasulullah alaihi-salam zikanatha kutengedwa ngati iwo ndi opambana kuposa Hazrat Abu Bakr ndi Hazrat Umar, koma kupambana kwao sikunapose awiriwa mu njira iliyonse. Ziri ngati Khidir

[1] Zikuwonekera poyera ndi mawu awa okhudza Abu Bakr as-Siddiq "radiyallahu taala anh". Ndi zomvesa chisoni kuti pali mbuli za anthu zina zpmwe zimaganiza ndi kulemba kuti Mtumiki alaihi-salam ankapembedza mafano asanakhale Mtumiki.

alaihi-salam yemwe anaphunzitsako zina Musa alaihi-salam.[1] Hazrat **Fatima** anali wopambana kuposa **Hazrat Khadija** ndi **Hazrat Aisha** "radiyallahu taala anh"unna chifukwa chakuti anali wa chibale wake potengera magazi. Koma kupambana kwa mtundu umodzi sikusonyeza kupambana ku mbali zonse. Akatswiri ophunzira a Chisilamu anayankhulapo motsutsana pa kupambana kwa azimayi atatu awa. Potengera Hadith Sharif, azimayi atatu awa komanso Hazrat Mariam (Mayi a Isa) ndi Hazrat Asiya (mkazi wa Pharaoh) anali azimai asanu apamwamba kwambiri kwa akazi onse a dziko lapansi. Hadith sharif imati **"Fatima ndi mzimayi wapamwamba kwambiri pa akazi onse ku Mparadizo, ndipo Hasan ndi Husayn ndi apamwamba pa a chinyamata onse aku Mparadizo"** potengera kupambana kwa mbali imodzi.

Otsatira pa kupambana mwa ma Swahaba al-kiram (abwenzi a Mtumiki) anali **al-Asharat al-Mubashshara**, anthu khumi omwe anadalitsidwa ndi uthenga wabwino woti akalowa ku Mparadizo. Pambuyo pa amenewo pali Asilamu 313 omwe anamenya nawo nkhondo yoyera ya Bedir. Kenako Asilamu 700 opanda mantha omwe anamenya nawo nkhondo ya Uhud. Kutsatira apo pali Asilamu 1400 omwe analumbira kuti athandiza Rasulullah alaihi-salam (**Biat ar-Ridwan**) pansi pa mtengo wina.

As-Swahaba al-kiram "radiyallahu taala anh" um ajmain anapereka miyoyo yawo ndi chuma chawo chifukwa cha Rasulullah "sallallahu taala alaihi wa sallam" ndi kumuthandiza Iye. Kotero ndi wajib kwa ife kutchula mayina awo mwa ulemu ndi chikondi. Sikololedwa kunena mawu achipongwe kwa anthu amenewa. Ungakhale gulu la ampatuko kutchula mayina awo mosalemekeza.

Munthu yemwe amakonda Rasulullah alaihi-salam, ayenera kukondanso ma Swahaba ake. Hadith sharif ikuti: "**Yemwe amakonda ma Swahaba anga amatero chifukwa amakonda ine. Yemwe amawada iwo amandida ine. Ndipo yemwe amandida ine amamuda Allahu Taala Ndipo yemwe amamuda Allahu Taala akalangidwa ndithu**". Mu hadith sharif ina anati; "**Allahu Taala akafuna kudalitsa munthu wa mu umma wanga, amaika mu mtima mwake chikondi cha Swahaba wanga: ndipo amawakonda kwambiri."**

Choncho, nkhondo zapakati pa ma Swahaba al-Kiram zisatengedwe ngati zimachitika ndicholinga choti akhale ma Khalifa kapena pofuna kukwaniritsa maganizo awo oipa kapena zilakolako za thupi ayi. Ndi ukambelembele womwe umayambitsa munthu kuyankhula zoipa za ma Swahaba al-Kiram powaganizira

[1] Kukanakhala kuti kupambana kumatengera ubale wa magazi, Hazrat Abbas akanayenera kuonedwa ngati wapamwamba kuposa Hazrat Ali. Komanso,Abu Talib ndi Abu Lahab, omwe anali oyandikana kwambiri pa nkhani ya ubale wa magazi, analibe ulemu ngakhale kupambana komwe kuli mwa okhulupirira otsikitsitsa.

motero. M'mitima mwa ma Swahaba al-Kiram munali mutachoswedwa nsanje ndi chilakolako cha ma udindo a dziko la pansi pokhala pa maso pa Mtumiki "swallaallaahu 'alayhi wa aalihi wa sallam" ndi kumvera mawu ake odala. Iwo anatsukidwa ndipo anachotsedwa umbombo, chilakolako, mkwiyo ndi chikhalidwe choipa. Iwo anayeretsedwa kwathunthu. Munthu amene amakhala kwa masiku angapo ndi m'modzi mwa ma Wali a Umma wa Mtumiki wa pamwamba amapindula ndi makhalidwe abwino a Wali ndi kuchita bwino kwake ndipo amakhala oyeretsedwa ku zilakolako za pa dziko. Zingatheke bwanji kuganizira kuti ma Swahaba a Mtumiki amenewa amalimbilana ulemerero wa pa dziko la pansi? Iwowa ankakonda Mtumiki "sallallahu taala alaihi wa sallam" kuposa wina aliyense; anapereka nsembe, chuma chawo ndi kusiya dziko lawo chifukwa chaMtumiki; amakonda kukhala ndi Iye zomwe zimatsitsimutsa mizimu yao. Ndi ugogodi chabe kutsogolera kunena kuti anthu awa anali oyipa; kuti ma naf awo sanali oyera ndi kuti ankalimbikira kuti apeze ulemerero wa dziko la pansi. Anthu akulu amenewa ndithudi anali oyera kuposa wina aliyense.

Sichilungamo kufanizira kusagwirizana ndi kulimbana pakati pa iwo ndi kusemphana kwa ife, anthu osafunirana za bwino, kapena kunena kuti amalimbana ndi cholinga chokwaniritsa zilakolako zawo zoipa, za kuthupi ndi za pa dziko. Ndizosaloledwa kuganizira ma Sahabat al-Kiram zotere. Munthu amene amawada ma Sahabat al-Kiram adziwe kuti ndi chimodzimodzi kumuda Mtumiki "swallaallaahu 'alayhi wa aalihi wa sallam", ndipo kunena za chipongwe za iwo zikutanthauza kuyankhula chipongwe kwa Iye, yemwe anawaphunzitsa iwo. Pachifukwa ichi, akuluakulu a Chisilamu adanena kuti kusowa ulemu ndi kusalabadira za ma Sahabat al-Kiram kumatanthauza kusakhulupirira Mtumiki wa Allah. Nkhondo za "Jamal" (Ngamila) ndi "Siffin"[1] sizingakwanire kukhala zifukwa zokwanira zowanyozera iwo. Ma Sahabi omwe analimbana ndi Hazrat Ali pa nkhondo imeneyi anali ndi zifukwa za chipembedzo zomwe zinawatetedza kuti asakhala oyipa ndipo adzalipidwa pa tsiku la chiweruzo. Hadith sharif ikuti: "**Mphotho imodzi idzaperekedwa kwa**

[1] Imfa ya Uthman bin Affan, mtsogoleri wachitatu, inadzetsa zipolowe komanso mikangano pakati pa Asilamu. Mikangano iyi inawona mkazi wa Mtumiki, Aisha, ndi amzake apa mtima monga Talha ibn Ubaydallah ndi Zubayr ibn al-Awam akumenya nkhondo yolimbana ndi Ali ibn Abi Talib, Khalifa wosankhidwa kumene. Nkhondo iyi inadziwika kuti ndi Jamal (Ngamila). Asilamu anali pa chiphinjo chomwe sanakumanepo nacho kale lomwe; mbali imodzi Khalifa, msuweni wake, ndi mnzake wachinsinsi wa Mtumiki Swalla Allaahu 'alayhi wa sallam, ndipo mbali inayo mkazi ndi maswahaba apamtima a Mtumiki. Nkhondo iyi inaphetsa ma swahaba ambiri a Mtumiki zomwe zinachititsa kuti pakhale magulu pakati pa Asilamu.

**mujtahid amene walakwitsa, ndipo ziwiri kapena khumi kwa iye amene wapeza choonadi. Imodzi mwa mphoto ziwirizo ndi chifukwa chogwiritsa ntchito Ijtihad.**[1] **Inayo ndi chifukwa chopeza choonadi."** Mikangano ndi ndewu pakati akuluakulu a Chisilamuwa inali chifukwa chakusiyana kwa ijtihad ndi kufuna kuchita zomwe Chisilamu chalamula koma osati chifukwa cha ukali kapena chidani. Aliyense wa Sahabat al-kiram anali mujtahid.[2]

Ndi Fardh kwa mujtahid aliyense kutsatira zomwe wapeza potsata ijtihad yake ngakhale ijtihad yake itapanda kugwirizana ndi Mujtahid a pamwamba kwambiri kuposa iye. Sikunali kololedwa kwa iye kutsatira ijtihad ya wina. Awiri mwa ophunzira a Al-Imam al-azam Abu Hanifa Numan ibn Thabit yemwe anamwalira ku Baghdad m'chaka cha 767/150, Abu Yusuf ndi Muhammad ash-Shaibani, komanso ophunzira awiri a Imam Muhammad ibn Idris ash-Shafii yemwe anamwalira ku Egypt m'chaka cha 820/204), Abu Sawr ndi Ismail al-Muzani, sanagwirizane ndi aphunzitsi awo pa zinthu zambiri, komanso za zinthu zina zomwe Aphunzitsi awo amati ndi 'halal' (zaloledwa) iwo anati ndi 'haram' (zoletsedwa). Iwo sanganenedwe kukhala ochimwa kapena oipa pa chifukwa chimenecho. Palibe ananena choncho, pakuti iwo anali mujtahid ngati Aphunzitsi awo.

Ndizoona kuti Hazrat Ali "radiyallahu taala anh" anali wa pamwamba komanso wophunzira kwambiri kuposa Hazrat Muawiya ibn Abu Sufyan, yemwe anamwalira ku Damascus m'chaka cha 680/60 komanso Hadzrat Amr ibn al-As "radiyallahu taala anh"uma yemwe anamwalira ku Egypt m'chaka cha 663/43. Anali ndi makhalidwe ambiri apamwamba kuposa iwo, ndipo ijtihad yake idali ya mphamvu kwambiri komanso yolondola kuposa ma ijtihad iwo. Koma poti ma Sahabat al-Kiram onse anali mujtahid, sikunali kololedwa kwa awiriwa kutsata ijtihad ya mtsogoleri wamkulu wa chipembedzoyo. Zinali zoyenera kuti iwo atsatire ijtihadis zawo.

**Funso:** "Pa nkhondo za 'Jamal' ndi 'Siffin', ma Muhajirun ambiri ndi ma Ansari pakati pa Sahabat al-Kiram anatenga nawo mbali ndikumvera komanso kumutsata Hazrat Ali. Ngakhale kuti iwo anali Mujtahid, anaona kuti ndi wajib kumutsata. Izi zikusonyeza kuti kunalinso wajib kwa Mujtahid kumutsatira Hazrat Ali ngakhale kuti ma ijtihad awo sanagwirizane ndi iye, sichoncho?"

---

[1] Ijtihad: liwu la za malamulo achisilamu lomwe limatanthawuza kulingalira kodziyimira pa kokha kochitidwa ndi katswiri wa malamulo achisilamu, kapena kuyeserera mokwanira kwa akatswiri a zamalamulo kuti apeze yankho la funso la za malamulo (zomwe sizinafotokozedwe mwatchutchutchu ndi Qur'ān kapena m'ma Hadith).

[2] Mwachitsanzo, zanenedwa mu Hadith sharif pa tsamba 298 la al-Hadiqa kuti Amr ibn al-As **"radiyallahu taala anh"**) anali mujtahid.

**Yankho:** Asilamu omwe anatsatira Hazrat Ali “radiyallahu taala anh” ndikumenya nkhondo kumbali yake, sanatero potsatira ijtihad yake koma kuti ma ijtihad awo anali ogwirizana ndi ijtihad yake ndipo kuti kunali wajib kutsatira Imam Ali. Chomwechonso ma ijtihad a ma swahaaba ambiri otchuka a Mtumiki samagwirizana ndi a Hazrat Ali, ndipo zinali Wajib kwa iwo kumenyana naye. Ma ijtihad a ma Sahabat al-Kiram pa nthawiyo zinapezeka m’njira zitatu zosiyana: ena mwa iwo anamvetsa kuti Hazrat Ali amalondola, ndipo kunali koyenera kwa iwo kuti atsatire Hazrat Ali; Gulu linaona kuti ijtihad ya omwe amatsutsana ndi Hazrat Ali inali yolondola. Ndipo kunali koyenera kwa iwo kutsatira amenewa ndikulimbana ndi Hazrat Ali; gulu lachitatu linaona kuti sikunali kofunika kutsata mbali iliyonse kotero sikunali kofunika kumenya nawo nkhondo zimenezi. Magulu atatu onsewa anali olondola ndipo ayenera kulipidwa pa tsiku lomaliza.

**Funso:** “Yankho [liri pa mwambali] likusonyeza kuti amene anamenyana motsutsana ndi Hazrat Ali “radiyallahu taala anh” nawonso anali olondola. Koma akatswili a Ahl as-Sunna amanena kuti Hazrat Ali amalondola ndipo otsutsana nawo anali olakwa, koma anali okhululukidwa chifukwa anali ndi udhr (chifukwa chololedwa), ndipo anapeza thawab. Nanga tinganene chiyani pa nkhaniyi?”

**Yankho:** Al-Imam ash-Shafii ndi Umar ibn Abd al-Aziz, akuluakulu awiri achisilamu, ananena kuti nkosaloledwa kugwiritsa ntchito mawu oti 'zolakwika' ponena Sahabat al-Kiram aliyense. Pa chifukwa ichi, zinanenedwa kuti: “Ndi kulakwa kunena kuti ‘zolakwika’ ponena za akuluakulu.” Sizololedwa kwa anthu ammunsi kunena mawu monga, “Anachita bwino,” “Iye analakwa,” “Tikuvomereza,” kapena “Sitikuvomereza,” za akuluakulu awo. Monga momwe Allahu Taala watikaniza kukhetse mwazi wa anthu Akuluakulu awa, tiyeninso titeteze lirime lathu kuti tisalankhule mawu monga ‘wolungama’ kapena ‘osalungama.’ Akatswili ozama omwe anaphunzira ma umboni ndi zochitika ndi kunena kuti Imam Ali analondola ndipo otsutsana naye analakwitsa, amatanthauza kuti Hazrat Ali akanakhala ndi mwayi wolankhula ndi omwe anali mbali inayo, iye Akanawaongolera pogwiritsa ntchito Ijtihad molingana ndi yake. Kunena zoona, Hazrat Zubair ibn Awwam ankatsutsa Hazrat Ali mu Nkhondo ya 'Jamal' koma, ataphunzira zambiri mozama, anasintha ijtihad yake ndikusiya kumenyana. Mawu a Akatswiri a Ahl as-Sunna omwe amaona kuti kulakwa uku ndi kololeka, ayenera kutengedwa choncho. Ndi kosaloledwa kunena kuti Hazrat Ali ndi omwe anali naye anali m’njira yolungama ndipo ma Swahaaba a Mtumiki Swalla Allaahu ‘alayhi wa sallam omwe anali m’gulu lina limodzi ndi mayi athu Aishat as-Siddiqa, anali pa njira yolakwika.

Nkhondo za pa kati pa Sahabat al-Kiram izi **zimachitika** chifukwa cha kusiyana kwa ijtihad mu nthambi za **Ahkam ash-Shar'iyya** (malamulo a Chisilamu). Panalibe kusiyana kulikonse pa zofunika za Chisilamu. Masiku ano, anthu ena amalankhula zachipongwe komanso mopanda ulemu za akuluakulu anthu achisilamu monga Hazrat Muawiya ndi Amr ibn al-As "radiyallahu taala anh"uma; sazindikira kuti ponyoza Sahabat al-Kiram amaipitsa mbiri komanso kunyoza Mtumiki "swallaallaahu 'alayhi wa aalihi wa sallam". Zalembedwa mu Shifa ash-sharif kuti Imam Malik ibn Enes anati: "Munthu wotukwana ndi kunyoza Muawiya ndi Amr ibn al-As akuyenera nawo kutukwanidwa ndi kunyozedwa. Ndikofunika Kalanga anthu amene amalankhula ndi kulemba zonyozazi ndi zopanda ulemu. Allahu Taala atipatse chikondi chodzaza m'mitima mwathu chokonda ma Sahaba Ake okondedwa! Asilamu oopa Mulungu amakonda akuluakuluwa koma osati aziphamaso ndi anthu ochimwa.

[Anthu amene akuzindikira ubwino ndi ukulu wa Mtumiki Swalla Allaahu 'alayhi wa sallam, amene akukonda ma Swahaba ndi amene amakonda ndi kulemekeza onse mwa iwo ndi kuwatsatira, amatchedwa **Ahl as-Sunna**. Anthu amene amanena kuti amakonda ena iwo, ndi kusakonda ena, moti mpaka kuwawonongera mbiri zawo; Ndi zomwe satsata aliyense mwa iwo, amatchedwa ma **Rafidi** kapena **Shia**. Ma Rafidi ambiri ali ku Iran, India ndi Iraq. Ku Turkey kulibe. Pofuna kunyenga Asilamu, ena mwa iwo amadzitcha ma Alawi. Ma Alawi ndi 'Asilamu amene amakonda Hazrat Ali. Kukonda munthu kumafunika kutsatira m'mapazi ake ndi kukonda omwe iye amakonda; ngati amamukonda Hazrat Ali "radiyallahu taala anh" bwenzi akutsata m'mapazi ake. Iye ankakonda ma Sahaba a Mtumiki onse. Iye anali phungu wa Khalifa Hazrat Umar, yemwe anali Khalifa wa chiwiri, yemwe amamuuzana naye zachinsinsi. Anakwatitsa mwana wake wamkazi yemwe anabereka ndi Hazrat Fatima, Umm Ghulthum kwa Hazrat Umar. Mu khutba, iye ananena za Hazrat Muawiya motere: "Abale athu sagwirizana nafe. Koma sikuti ndi osakhulupirira kapena Ochimwa. Ijtihad yawo ndi yomwe imawachititsa kutero." Pamene Hazrat Talha "radiyallahu taala anh", yemwe amamenyana ndi Hazrat Muawiya, anaphedwa mnjira ya chikhulupiriro, Hazrat Mu'awiyah mwiniwake adasasa fumbi pa nkhope ya Hazrat Talha ndipo anaswalisa janaza yake. Allahu Taala akunena mu **Quran al-Karim**: "**Okhulupirira ndi pachibale."**

Mu ayat yomaliza ya Sura al-Fath, Allahu Taala akuti: **"Ma swahaba a Mtumiki Swalla Allaahu 'alayhi wa sallam amakondana wina ndi mnzake."** Kusakonda ngakhale m'modzi mwa ma swahaaba a Mtumiki Swalla Allaahu 'alayhi wa sallam ngakhale kumuda woipitsitsa, zimatanthauza kusakhulupirira mu **Quran al-Karim**. Akatswiri a Ahl as-Sunna amamvetsetsa kupambana kwa

Sahabat al-Kiram “radiyallahu taala anh” um ajmain molondola ndipo analamula Asilamu kuti azikonda onse potero anapulumutsa Asilamu ku tsoka.

Anthu otchedwa "Khariji" amawada ndi kuchitira chipongwe Ahl-i Bayt (abale a Mtumiki), omwe ndi olemekezeka Hazrat Ali “radiyallahu taala anh”) ndi ana ake ndi zizukulu mu mbado wake, Asilamu a Sunni okondedwa kwambiri. Tsopano ma Yazidi, mfundo zawo ndi za bodza kwambiri, zosakhuzana ndi Islam.

Ma **Wahhabi**, ngakhale amati amakonda ma Sahabat al-Kiram onse, iwa samatsatira anthu odalitsidwawo koma kutsata njira zawo zampatuko zomwe iwo amanamizira kuti ndi za ma Swahaba. Wahhabism inayamba pophatikiza maganizo a munthu wa mpatuko Ibn Taimiyya, yemwe amatsutsana ndi Sunni ndi mabodza a Hempher, kazitape wa ku Britain. Akuluakulu a tasawwuf ndi ma Shiites samawakonda akatswiri a Ahl as-Sunna ndipo amawanyoza. Iwo amaganiza choncho iwo okha ndi Asilamu. Amaganiza kuti iwo okha ndiye Asilamu. Amatenga anthu amene sali ngati iwo kuti ndi a ‘ampatuko’ ndipo kuti ndi halal kuwapha ndi kuwalanda katundu wawo. Choncho, ma Wahhabi amakhala anthu a **ibahi** kapena kuti ma **ibahati**, anthu, omwe amati ndi ‘halal’ kupha ndi kulanda katundu wa Asilamu mopanda chilungamo; zomwe ndi haram. Iwo amatanthauzira molakwika **Quran al-Karim** ndi Hadith Sharif ndipo amaganiza kuti Chisilamu chili ndi matanthauzo a iwo okhawo. Amatsutsa **Adilla Al-Shariyya** ndi ma Hadith ambiri. Akatswiri akulu a madhhab anayi, akupereka umboni kuchokera m’mabuku ambiri kuti amene anasiya Ahl as-Sunna analowera ku chipembedzo chonyenga ndipo amaononga kwambiri Chisilamu.[1]

[1] Kuti mumve zambiri, werengani mabuku athu achingerezi, Advice for the Muslim ndi Endless Bliss; Al-minhat al-wahbiyya firraddil-Wahhabiyya, At-tawassuli bin-Nabi wa bis-salihin ndi Sabil annajat omwe ali mu chiArabu komanso Sayf ul-abrar lomwe liri mu chi Persian. Mabuku awa ndi mabuku ena ofunika alembedwa potsutsa ahl al-bida asindikizidwa ndi Hakikat Publishing ku Istanbul. M’mutu wa "Baghi" mu bukhu la chitatu lochedwa Radd al-muhtar lolembedwa ndi Muhammad Amin Ibn Abidin yemwe anamwalira ku Damascus m’chaka cha 1836/1252 komanso m’mutu wa “Nikah” m’bukhu la chi Turk lotchuedwa Ni’met-i Islam, zalembedwa momveka bwino kuti ma Wahhabis ndi ma ibahi Eyyub Sabri Pasha Yemwe anamwalira m’chaka cha 1890/1308), komanda mu nthawi ya Sultan Abd al-Hamid Khan. II, m’mabuku ake a m’chi Turkey a Mir’at al-Haramain ndi Tarikh Wahhabiyyan, komanso Ahmed Cevdet Pasha, m’bukhu la chisanu ndi chiŵiri mu Turkey lotchedwa Osmanlı Tarihi, akukamba zambiri za ma Wahhabi. M’buku lake la chiarabu latchedwa Shawahid al-haqq losindikizidwa kachitatu ku Cairo 1965/1385, Yusuf an-Nabhani, anatsutsa ma Wahhabi ndi ma Ibn Taymiyya motambasula.

Eyyub Sabri Pasha “rahimahallahu taala” analemba kuti: “Chi Wahhabi chinayamba ndi mpatuko wozunzika wankhanza pa chilumba cha Arabia mu 1791/1205.” Muhammad Abduh waku Egypt anali m'modzi mwa anthu amene anayesa kufalitsa Chiwahabi ndi kutsutsa ma madhhab kudzera m'mabuku ake kulikonse pa dziko lapansi. Ngakhale kuti anali Freemason (Gulu la kumidima) yemwe ananena poyera kuti amasilira Jamal ad-din al-Afghani yemwe anamwalira m’chaka cha 1867/1314, ndipo anali mkulu wa Masonic Lodge ku Cairo, Abduh anawonetsedwa kwa achinyamata ngati “wophunzira wamkulu wa Chisilamu, wanzeru, wotchuka posintha zinthu” Adani a Chisilamu, omwe anabisalira kuti awononge Ahl as-Sunna ndi kufafaniza Chisilamu, adayambitsa chipongwechi (fitna) mwachinyengo ponamizira kuti ndi anthu opembedza. Abduh anayamikiridwa mwapamwamba. Akatswiri akuluakulu a Ahl As-Sunna, a **aimmat al-madhahib**, analengeza kuti anthu awa anali mbuli. Mayina awo samatchulidwanso. Koma mbadwa za chilungamo za makolo athu, ana olemekezeka ofera chikhulupiriro, omwe anapereka miyoyo yawo chifukwa cha Mtumiki “sallallahu taala alaihi wa sallam” ndi Chisilamu, sananyengedwe kapena kukopeka ndi izi ngakhalekuti ma miliyoni a ma paundi angwiritsidwa ntchito. Iwo sanamvere kapena kutchulapo za ‘ngwazi za Chisilamu’ za bodzazi. Iwo anatetezedwa ndi Allahu Taala ku ziwembu za zigawenga za chinyengozi. Masiku ano, kuli mabuku otanthauziridwa ndi anthu omwe satsatira madhhab aliwonse monga Mawdudi yemwe anayambitsa Al-jamaa al-Islamiyya ku India, (anamwalira m’chaka cha 1979/1399), Sayyid Qutb yemwe anaphedwa ku Egypt mu 1966/1386, Hamidullah ndi mamembala a Tabligh Jamaa omwe akuperekedwa kwa achinyamata. Mabuku otanthauzidwa amenewa, amayamikira kwambiri m’mauthenga omwe ali ndi malingaliro ampatuko ndi otsutsana ndi zonena za akatswiri a Ahl as-Sunna. Nthawi zonse tiyenera tikhale atcheru ndi osamala. Allahu Taala azindikiretse Asilamu chisomo cha Wokondedwa Wake Mtumiki Muhammad alaihi-salam! Atiteteze kuchokera ku chinyengo ndi mabodza a adani anthu! Amin. Tasazinamize pongopemphera pokha. Kupemphera popanda kutsatira Adat-ilahiyya (mwambo kapena chizolowezi, Cha umulungu), popanda kugwira ntchito kapena kugwira njira, kumakhala ngati kupempha zozizwitsa kwa Allahu Taala. Msilamu ayenera kugwira ntchito ndi kupemphera. Tiyenera kutsatira njira ndi kupemphera. Njira yoyamba yopewera kusakhulupirira ndi kuphunzira ndi kuphunzitsa Chisilamu. Ndipo ndi fardh (zokakamizika) komanso ntchito yayambirira ya aliyense, mwamuna kaya mkazi, kuphunzira ziphunzitso za Ahl as-Sunna, zolamulidwa ndi zoletsedwa. Makono ndi kwapafupi kuphunzira, chifukwa pali ufulu wolemba ndi kufalitsa mabuku a zoona a chisilamu. Msilamu aliyense ayenera kuthandiza Boma lomwe lapereka ufulu uwu kwa Asilamu.

Anthu omwe saphunzira ilm al-hal (zikhulupiriro ndi machitidwe) a Ahl as-Sunna ndi kuphunzitsa ana awo ali pa chiopsezo chotuluka m'Chisilamu ndi kugwera m'phompho la ukafiri. Ma pemphero a anthu otere sazalandiridwa. Ndiye, angaziteteze bwanji kwa ukafiri? Rasulullah "swallaallaahu ´alayhi wa sallam alaihi wa Sallam" adati: "**Pali Chisilamu pamene pali kudziwa. Palibe Chisilamu pamene palibe chidziwitso**." Munthu ayenera kudya ndi kumwa kuti asafe ndi njala. Chimodzimodzi ndikoyenera kuphunzira chipembedzo chathu kuti tisanyengedwe ndi osakhulupirira komanso kuti tisakhale osakhulupirira. Makolo athu nthawi zambiri ankasonkhana ndi kumawerenge mabuku a ilm al-hal, amaphunzira chipembedzo chawo ndipo potero amakhala Asilamu osangalala. Iwo anatipatsira kuwala kwa chisangalalo kumeneku molondola. Kuti tikhalebe Asilamu komanso kuti ana athu asanyengedwe ndi adani ochokera mkati kapena kunja, chofunika kwambiri choyamba ndi kuwerenga ndi kumvesetsa mabuku a ilm al-hal olembedwa ndi akatswiri a Ahl as-Sunna. Makolo omwe akufuna mwana wawo kuti akhale Msilamu ayenera kuti mwanayo aphunzire kuwerenga **Quran al-Karim**. Tiyeni tiwerenge, tiphunzire ndi kuphunzitsa ana athu, ndi iwo tikwayang'anira, pomwe tili ndi mwayi wotero. Ndi kovuta koma mwinanso ndi kosatheka kuti iwo amphunzire akupita ku sukulu. Zizakhala zopanda phindu kudandaula zinthu zitawonongeka. Tisakhulupirire mabuku onyenga, ma nyuzipepala, magazini, TV ndi ma pulogalamu a pawailesi, ma filimu ndi masamba a nchezero a ma zindiq ndi adani a Chisilamu. Ma **Zindiq**, monga momwe anafotokozera Ibn Abidin "rahimahallahu taala" m'buku la chitatu la **Radd al-muhtar**, kuti ndi anthu achinyengo osakhulupirira omwe, ngakhale kuti sakhulupirira m'chipembedzo chilichonse, amanamizira kukhala Asilamu ndi kumaphunzitsa zinthu zoyambitsa ukafiri ngati kuti ndi za Chisilamu, ndi kuyesetsa kuwatulutsa Asilamu m'Chisilamu."

**Funso:** "Munthu amene wawerenga mabuku otandauzidwa achinyengowa akuti: 'Tiyenera kuwerenga tafsir (mafotokozedwe) a **Quran al-Karim**. Kusiyira ntchito yophunzira chipembedzo chathu ndi **Quran al-Karim** kwa akatswiri achipembedzo okha ndi lingaliro lowopsa komanso lowopsa lochititsa mantha. **Quran al-Karim** siyikunena kuti, "Oh, akatswiri achipembedzo". Akuti, "Oh, Asilamu" kapena "Oh Anthu inu." Pachifukwa ichi, Msilamu aliyense ayenera kuyimvetsetsa **Quran al-Karim** pa yekha ndipo asalekere ntchito anthu ena."

"Munthu ameneyu akufuna kuti aliyense awerenge mabuku a tafsir ndi hadith. Sakulimbikitsa kuwerenga mabuku a kalam, fiqh ndi ilm alhal olembedwa ndi akatswili achisilamu ndi akuluakulu a Ahl as-Sunna. Mabukhu osindikizidwa ndi Rashid Rida's (wophunzira wa Muhammad Abduh, yemwe anamwalira m'chaka cha1935/1354) m'buku lotchedwa **Islamda Birlik Ve Fikh**

**Mezhebleri** lolembedwa ndi Ofesi yayikulu ya Chipembedzo (bukhu la no. 157; mu 1974/1394) linayambitsa .chisokonezo pakati pa awerengi. Pa masamba ambiri a bukhuli, makamaka mu "Dialogue Six," bukulo limati:

*'Iwo [ma muqallid, otsatira amodzi mwa madhhab anayi] anakweze ma imamu a mujtahid ngati a neneri. Moti amafika pokonda zoyankhula za ma mujtahid omwe amatsutsana ndi zoyankhula za Mtumiki m'ma Hadith. Amanena kuti ndikutheka kuti ma Hadith anathetsedwa (naskh) kapena pakanakhala Hadith ina m'mabuku a ma imam awo. Pogwiritsa ntchito zonena za anthu omwe angakhale olakwika malinga ndi mamvedwe awo ndipo omwe akhonza kukhala kuti samadziwa za nkhaniyo, komanso ponyalanyanza Hadith za Mtumiki yemwe samalakwitsa, ma muqallids awa amatsutsananso ndi mujtahid. Iwo amatsutsana ndi Quran potero. Amanena kuti ma imam a Mujtahid okha ndi omwe amayimvetsetsa Quran. Mawu otero a faqih ndi ena a muqallid amasonyeza kuti anawatenga kuchokera kwa Ayuda ndi Akhristu. Kuyimvetsa Qur'an ndi ma Hadith ndi kosavuta kusiyana ndi kumvetsetsa mabuku olembedwa ndi anthu a fiqh. Anthu omwe aphunzira bwino chiarabu ndi galamala yake sangavutike kumvetsetsa Quran ndi ma Hadith. Ndani angatsutse pa dziko lapansi kuti Allah ndi okhonza kufotokoza chipembedzo Chake mwachindunji? Ndani angatsutse zoti Rasulullah anali kumvesetsa zimene Allah akutanthauza kuposa wina aliyense? Kunena kuti mafotokozedwe a Mtumiki anali osakwanira kwa Asilamu zikutanthauza kuti iye analephera kukwaniritsa ntchito yake yoyankhulirana (tabligh) mwatchutchutchu, Zikanakhala kutu anthu ambiri sanamvetsetsa Quran ndi Sunna, Mulungu sakanaweluza anthu onse ndi malamulo a Bukhu ndi Sunna. Munthu aliyense ayenera kudziwa bwino chikhulupiriro chake ndi ma umboni ake. Allah samalola taqlid (kutsatira madhhab) pongotsatira njira za makolo awo ndi azigogo awo, koma chifukwa chomvetsetsa. Ma Ayah akuwonetsa kuti Allah savomereza taqlid. Ndi kosavuta kumvetsa gawo la chipembedzo lokhudza furu (zochita mu Chisilamu zomwe zalamulidwa) kuchokera ku umboni wake kusiyana ndi kumvetsetsa gawo la chikhulupiriro (usul, iman). Mmalo mufuna zovuta Allah sakanafuna zosavutazo? Zidzakhala zovuta kupanga malamulo pa zinthu zosowa, poti zidzakhala zosavuta kupezerapo zifukwa posaziziwa kapena kusazichita. Anthu a fiqh adayambitsa mavuto angapo iwo okha. ndikupanga malamulo ake. Iwo anayesetsa kuyambitsa zinthu monga raayi (chiweruzo chaumwini), qiyas jail (fanizo lodziwikiratu) ndi qiyas khafi (fanizo lobisika) ngati mabukhu awo.*

*Zinthu izi anazipangitsa kuti zifalikire mbali za Ibaadat, komwe kunali kovuta kupeza chidziwitso kudzera mu kulingalira. Potero anatambasula chipembezo kambirimbiri. Anayika Asilamu pa vuto. Sindikana qiyas (kuganizira) koma*

*ndikuti palibe qiyas mu ibadat. Iman ndi Ibadat zidamalizidwa mu nthawi ya Mtumiki. Palibe angaonjezerepo kanthu. Ma imamu a mujtahid analetsa anthu kutsanzira (taqlid) anapanga taqlid kukhala yoletsedwa."*

"Zoyankhula izi, zasankidwa kuchokera m'mabuku lotchedwa **Islamda Birlik Ve Fikh Mezhepleri**, lolembedwa ndi munthu wosatsata madhhab aliwonse, Rashid Rida. Monga anthu ena onse osasata madhhab aliwonse mabuku awo amaletsa kutsatira ma imamu a madhaba anayiwo. Amalamulira kuti aliyense aphunzire tafsir ndi Hadith. Munganene chiyani pa nkhaniyi?"

**Yankho:** Ngati ndime zolembedwa ndi anthu osatsatira madhhab ziwerengadwa ndi chidwi, munthu atha kuona mosavuta kuti iwo amayesa kunyenga Asilamu pokometsera malingaliro awo a mpatuko ndi osamveka bwino komanso mawu onama. Anthu osadziwa (mbuli mchipembezo),akhonza kutengeka ndi kugwa mu msampha wa abodzawo poganiza kuti zolembazo ziri ndi gwero la choonadi koma kwa anthu ophunzira omwe amayang'anitsitsa, sangagwere mu msampha wa onyengawa.

Pofuna kuchenjeza achinyamata za kuopsa kwa anthhu osatsata madhhab kapena kuti otsutsa chi Sunni, omwe chakhala akutengera Asilamu ku chionongeko chosatha, akatswiri a Chisilamu rahimahum-Allahu Taala analemba mabuku ofunika zikwi mu zaka zoposa mazana anayi. Zotsatirazi ndi kumasulira kwa ndime zina zochokera m'Buku **la Hujjat-Allahi ala-l-alamin** lolembedwa ndi Yusuf an-Nabhani [yemwe anamwalilira ku Beirut mchaka cha 1932/1350) ngati yankho ku funso lomwe lili pa mwambapa:

"Sikuti aliyense angathe kupanga ahkam (malamulo, kumanga mfundo) kuchokera mu **Quran al-Karim**. Poti ngakhale ma Imam a mujtahid sakanatha kumanga mfundo pa nkhani zonse za mu **Quran al-Karim**, ndi chifukwa chake Rasulullah "sallallahu taala alaihi wa sallam" anafotokoza malamulo a mu Quran al-Karim m'ma Hadith ake. Monga **Qur'an al-Karim** idalongosoledwa ndi iye yekha, ma Hadith imatha kumveka ndi kufotokozedwa ndi Sahabat al-Kiram ndi ma mujtahid okha. Kuti athe kuzimvetsa. Allahu Taala anapatsa ma imam mujtahid **aqli** (luntha, nzeru zomvetsa ndi za sayansi) komanso **naqli** (chidziwitso cha chipembedzo chofalitsika), kuzindikira kwa mphamvu, kupenyatsetsa, kulingalira kwakukulu ndi zina zambiri za pa mwamba. Choyambirira pa za bwino zonsezi panali taqwa (kudzitchinjiriza ku Haramu). Chotsatira chinali kuwala kopatulika m'mitima yawo. Ndi thandizo la makhalidwe abwino amenewa, ma Imam a mujtahid athu ankamvetsa zomwe Allahu Taala ndi Rasulullah alaihi-salam amatanthauza m'mawu awo. Koma pa

zomwe samamvetsa amapeza mayankho ake kudzera mu **qiyas**[1]. Aliyense mwa aimmat al-madhahib (ma Imam akuluakulu anayi omwe anayamba maddhab a Ahl as Sunna Islam) ananena kuti sanalankhule za m'maganizo awo ndipo anauza ophunzira awo kuti: 'Ngati pali Hadith ya sahih, siyani mawu anga ndipo tsatirani za hadith ya Mtumiki alaihi-salam!' Akatswiriwa anali anthu a tarjih (ofufuza, kufananiza, kukondetsa) omwe ankadziwa zolemba za atsogoleri a madhhab anayi kutengera pa ma ijtihad awo. Iwo anawerenga ndi kumva zolemba ndi ofalitsa ma Hadith omwe Mtsogoleriyo wa madhhab anakhazikitsa ijtihad yake ndi ma Hadith a sahih omwe anakumana nayo atsopano. Anaunika zomwe zinanenedwa kumapeto kwake ndi zina zambiri, potero anazindikira kuti ndi ziti zimene ziyenera kusankhidwa. Kapena imam wa mujtahid [imam al-madhhab] anaganiza za chochitika kapena momwe zinthu zinalili (masala) kupyolera mu qiyas chifukwa hadith yomwe ikanatambasula [kapena kufotokoza] inali isanamufike iye, ndipo ophunzira ake atapeza kuti hadith imeneyo ndi sharif, anakhala ndi maganizo osiyana. Koma pogwiritsa ntchito ijtihad motero, ophunzira sanatero mopysola malamulo okhazikitsidwa ndi imamu. Ma mufti a Mujtahid omwe anabwera pa mbuyo pa iwo anapereka fatwa mnjira imeneyinso. Monga zikumvekera kuchokera mu zonse zomwe zalembedwa apa, Asilamu omwe akhala akutsatira ma imam anayi a madhhab ndi ma Mujtahid omwe anaphunzitsidwa madhhab awo akhala akutsata malamulo a Allahu Taala ndi Mtumiki Wake. Ma Mujtahid amenewa amamvetsa malamulo a mu **Quran al-Karim** ndi Hadith Sharif, omwe aliyense samkawamvetsetsa, ndi kufotokoza zomwe anamva. Asilamu akhala akuchita taqlid pa zomwe mujtahid anamva ndi ndikuuza ena kuchokera m'Bukhu ndi Sunna; chifukwa Allahu Taala anayankhula mu ayah karima ya 43 ya surah an-Nakhl: **"Ngati simukudziwa, funsani amene akudziwa."**[2]

---

[1] Qiyas ndi njira yofanizira mwakuya ziphunzitso za hadith ndi zomwe zili mu Quran komanso pogwiritsa ntchito lamulo lodziwika pa zochitika zatsopano ndikupanga lamulo latsopano.

[2] Ayah iyi ikusonyeza kuti si aliyense angathe kumvetsa Bukhu ndi Sunnah molondola. Pakhonza kukhala anthu ena omwe sangathe kumvetsa. Ayah iyi ikulamula anthu amene sangathe kumvetsa kuti asayetsere kumva mwa iwo okha **Quran al-Karim** kapena Hadith Sharif koma kuti aphunzire pofunsa anthu omwe akumvetsetsa bwino. Zikanakhala kuti aliyense anamvetsetsa matanthauzo a Qur'an al-Karim ndi Hadith Sharif molondola, magulu 72 achinyengo aja sakanabadwa. Omwe anayambitsa maguluwa amenewa anali ophunzira mozama, koma onse sanatha kumvetsetsa matanthauzo a mu Nass (Qur'an al-Karim ndi Hadith Sharif) molondola. Chifukwa chosamvetsetsa, iwo adapatuka njira yolondola ndikusocheretsa Asilamu ma miliyoni ambiri. Ena mwa iwo akhala akuwonjeza popereka matanthauzo olakwika a ma Ayah ndi Hadith kotero kuti asanduka achinyengo omwe amawatchula Asilamu a njira yoyenera kuti ndi 'okanira' ndi 'ampatuko'. Mu

“Allahu Taala anapereka mwayi wapadera kwa Umma wa Mtumiki alaihi-salam wa ma imamu anayi a madhhab kuti azitha kuchita ijtihad. Ndipo kuti Asilamu onse azasonkhana m’madhhab amenewa. Allahu Taala, analenga ma imamu a itiqad (iman, zikhulupiriro) ndipo, anateteza chipembedzo Chake kuti chisasokonezedwe polenga ma imamu a madhhab. Dalitso limeneli kunalibe m’zipembedzo za Chikhristu ndi chi Yuda. Ndichifukwa chake zinapotozedwa ndipo zinasinthidwa kukhala masewera.

"Ndi mgwirizano wa akatswiri a Chisilamu kuti pambuyo pa zaka 400 zotsatira Imfa ya Mtumiki “swallaallaahu ‘alayhi wa aalihi wa sallam”, sikudzakhala katswiri wophunzira mwa kuya woti angagwiritse ntchito ijtihad. Aliyense amene amateteza ntchito ya ijtihad mu nthawi ino ndi wamisala kapena osaphunzira mokwanira Chisilamu. Pomwe Katswiri pa chipembedzo wamkulu Jalal ad-din as-

Suyuti Abd ar-Rahman “rahimahullahu taala” (Yemwe anamwalira ku Egypt, mu 505/911) ananena kuti wafika pa geredi ya ijtihad, akatswiri amakono anamufunsa za funso lomwe mayankho ake awiri anali osiyana. Anamfunsa kuti anene yankho lomwe linali lodalirika kwambiri koma sanathe kuwayankha. Anangonena kuti anali wotanganidwa kwambiri moti analibe nthawi yoyankhira. Komabe, anafunsidwa kuti agwiritse ntchito ijtihad pa fatwa, yomwe inali ya mlingo wotsika kwambiri wa ijtihad. Ngati katswiri wozama ngati- Suyuti anapewa kugwiritsa ntchito ijtihad pa fatwa, tingawaganizire bwanji anthu amene amakakamiza anthu kugwiritsa ntchito ijtihad ya mtheradi (mutlaq)? Tingalakwitse kuwanena kuti ndi a misala kapena mbuli zachipembedzo? Al-Imam al-Ghazali “rahimahallahu taala” (omwe anamwalira ku Tus, mchaka cha 1111/505) ananena m’buku lake lotchedwa **Ihya Ulum ad-Din** kuti mu nthawi yake kunalibe mujtahid.

“Ngati Msilamu wopanda mujtahid waphunzira hadith yosagwirizana ndi chigamulo cha imam wa madhhab ake ndipo akuona kuti ndi kovuta kwa iye kuchita potengera madhhab ake, iye ayenera kupeza mujtahid ina mwa madhhab anayi aja yomwe ijtihad yake ikuchokera pa hadith imeneyo. Ndipo achite chinthucho motsatira madhhab omwe mujtahidyo ikuchokera.[1] Chifukwa ndi kosaloledwa kwa anthu amene sanafike mulingo ya ijtihad kuti

---

bukhu lotchedwa **Kashf ash-shubuhat**, lomwe lamasuliridwa mu chi Turkey ndipo linalowetsedwa mwachinsinsi mdziko la Turkey, likuti ndi mubah (kololedwa) kupha ndi kulanda chuma cha Asilamu amene amakhulupirira Ahl as-Sunna.

[1] Katswiri wamkulu wa Cipembedzo al-Imam Yahya an-Nawawi “rahimahallahu taala” – yemwe anamwalira ku Damascus mchaka cha 1277/676) anafotokodza izi mozama m’bukhu lake lotchedwa **Rawdat attalibin.**

apange lamulo kuchokera mu Nass (**Quran al-Karim** ndi Hadith Sharif). Tsopano pali mbuli zina zimati zafika mulingo ya Ijtihad mokwanira, koti akhoza kupanga lamulo kuchokera mu Nass ndi kuti iwo safunikanso kutsatira madhhab aliwonse; amasiya kutsatira madhhab omwe akhala akutsata kwa zaka zambiri. Amayesa kutsutsa ma madhhab ndi mafunso ao osamveka, naneka kuti 'sitingatsatire malingaliro a anthu opembedza oti anali ngati ife.' Monyengeka ndi Satana ndi motsogozedwa ndi zilakolako zawo amadziwona kupambana. Sazindikira kuti potero amawonetsa kuchepekedwa ndi utsiru wawo momvetsa manyazi. Pakati pawo pali a mpatuko ena, mbuli zimene zimanena ndi kulemba kuti aliyense awerenge mabuku a tafsir ndi kupeza malamulo kuchokera m'mabuku a tafsir ndi [Sahih ya] **al-Bukhari**. O m'bale wanga Msilamu! Ndithudi pewani kuchita ubwenzi ndi zitsiru zotere, powaganizira kuti iwo ndi anthu opembedza. Musawerenge mabuku awo opeka! Gwirani molimba madhhab a imam wanu! Ndi inu omasuka kusankha amodzi mwa madhhab anayiwa, koma nkosaloledwa kutsakaniza ma rukhsas a madhhab zomwe zimatchedwa '**talfiq**'.[1]

"Asilamu omwe amatha kuwerenga ndi kumvetsetsa ma Hadith ayenera kuphunzira ma Hadith omwe anali zolemba za madhhab awo, ndichita zomwe zayamikiridwa ndi kupewa zomwe zili zoletsedwa ndi ma hadith amenewo. Kenako phunzirani izi: ukulu ndi kufunika kwa chipembedzo cha Chisilamu; ungwiro wa Mtumiki "swallaallaahu 'alayhi wa aalihi wa sallam" ndi mayina ndi zizindikiro za Allahu Taala; moyo wa Rasulullah, kukoma ndi zozizwitsa zake; dongosolo la dziko lino ndi ilo liri kudza; za kuuka kwa akufa, za Chiweruzo, M'Paradiso ndi Gahena; angelo, mizimu, Umma wakale, Atumiki ndi mabuku awo akumwamba; apamwamba odziwika kwa Mtumiki "swallaallaahu 'alayhi wa aalihi wa sallam" ndi ku **Quran al-Karim**; moyo wa ma Al ake (abale ake a kumagazi) ndi ma Sahaba wake; zizindikoro za tsiku lomaliza, ndi kudziwa zambiri za dziko ili ndi dziko liri mkudza. Zambiri zokhudza dziko lapansi ndi lotsatiralo zasonkhanitsidwa mu ma hadith a Mtumiki "swallaallaahu 'alayhi wa aalihi wa sallam"

"Monga zikumvekera zomwe zalembedwa pano, zikusonyezeratu kuti ndi umbuli kunena kuti zigamulo za chipembedzo za Mujtahid zomwe ndi zokhazikitsidwa pa ma hadith, ndizopanda ntchito. Mwa zinthu zochuluka

[1] 'Talfiq' ndi mchitidwe wosatsata madhhab aliwonse koma kusakaniza njira zosavuta za madhhab anayi aja. Munthu akachita chinthu chololedwa m'chisilamu molingana ndi imodzi mwa ma madhhab anayi aja, adzichitanso ntchito zina zambiri mogwirizana ndi momwe zikunenedwera m'madhhab ena atatuwo. Mchitidwe wowonesetsa kuti munthu ukutsata zokhazo zovomerezeka m'madhhab anayiwa matchedwa **'taqwa'**, ndipo umapereka thawab zambiri (malipiro a Tsiku Lomaliza).

zomwe zaperekedwa mu ma hadith, zophunzitsa ibadat ndi muamalat (ubale pakati pa anthu, monga malonda m'chisilamu) ndi zochepa. Malinga ndi kunena kwa akatswiri ena, akuti ziripo pafupifupi 500, koma mukaphatikiza zobwereza sizikupitirira 3000. Mwa ma hadith ochepawa, ndizachiziwikire kuti iliyonse mwa ma imam a madhhab anayiwo ndikutheka kuti mwina sanamve hadith imodzi ya sahih. Hadith iliyonse ya sahih inagwiritsidwa ntchito ngati chikalata ndi m'modzi mwa ma imamu anayi a madhhab. Msilamu yemwe akuona kuti ntchito inayake m'madhhab mwake ikutsutsana ndi Hadith ya sahih, achite ntchitoyo potsatira madhhab ena omwe adatengera ijtihad yake pa Hadith imeneyo. Mwina Imam wa madhhab a munthu ameneyo anamvanso za Hadithyo koma anatsatira Hadith ina yomwe amayimva kuti ndi sahih kwambiri, kapena inanenedwa mochedwa, kusiya yoyamba, kapena, pazifukwa zina zodziwika kwa Mujtahid, sanatenge Hadith yayambayo ngati zolembedwa. Ndibwino kwa Msilamu amene akumvetsa kuti Hadith ndi sahih kutsatira hadith posiya chigamulo cha madhhab awo chomwe sikugwirizana ndi Hadith imeneyo, koma potero ayenera kutsanzira madhhab ena omwe anagwiritsa ntchito hadith imeneyo mu ijtihad yake pa nkhani ikukambidwayo; chifukwa imam wa madhhab yachiwiri ija, podziwa zolembedwa za chigamulo chosadziwika kwa munthuyo, anapeza kuti palibe chomwe chingalepheretse kutsata Hadith imeneyo. Ngakhale zili choncho, nkololedwanso kwa munthu ameneyo kutsata nkhaniyo molingana ndi madhhab awo, chifukwa n'zosakayikitsa kuti imam wa madhhab awo ankadalira zolembedwa zomveka bwino mu chigamulo chake. Chisilamu chikuona kuti ndi zokhululukidwa kuti muqallid (wotsatira, madhhab) asadziwe zolembedwazo, pakuti palibe ndi m'modzi mwa ma imam a madhhab anayi anapatuka m'Buku ndi Sunna mu ijtihad. Madhhab awo ndi kufotokoza kwa Buku ndi Sunna. Anafotokoza matanthauzo ndi malamulo a m'Buku ndi Sunnah kwa Asilamu. Anawafotokoza m'njira yoti Asilamu amvetse, ndipo anazilemba m'mabuku. Ntchito imeneyi ya ma imam anayi madhhab rahimahum-Allahu Taala unali utumiki wopambana kwambiri m'Chisilamu moti siyikanatheka ndi phamvu za munthu kukanakhala kuti Allahu Taala sanawathandize. Ma Madhhab awa ndi umboni woyenera kwambiri wotsimikizira kuti Mtumiki "swallaallaahu 'alayhi wa aalihi wa sallam" ndi Mtumiki woona ndipo Chisilamu ndi Chipembedzo Choona.

"Kusiyana kwa ma ijtihad a aimmat al-madhahib athu kunali pa nkhani zokhudzana ndi machitidwe (furu ad-din, pankhani za fiqh, malamulo achisilamu okhazikidwa pa ziphunzitso za **Quran al-Karim** ndi Hadith). Ndipo samasiyana wina ndi mzake pa ziphunzitso za machitidwe zomwe ndi zodziwika kuti ndi ofunika mu chipembedzo ndipo zomwe zinatengedwa m'ma hadith omwe zolemba zawo zinaperekedwa m'njira ya tawatur (zotsatizana,

zobwerezabwereza, zamitundu yambiri, zoona zosakayika, zofalitsa zambiri za chidziwitso cha chisilamu). Amasiyana mu zinthu zina za chidziwitso zokhudza machitidwe. Izi zinayamba chifukwa cha kusiyana kwa kamvedwe kawo ka zolembedwa za nkhani zimenezi. Kusiyana pang'onoku pakati pawo ndi chifundo cha Allahu Taala pa Umma; Asilamu amaloledwa kutsata madhhab aliwonse omwe angafune ndi omwe ali osavuta kwa iwo. Mtumiki "swallaallaahu 'alayhi wa aalihi wa sallam" ananeneratu za kusiyana uku kuti ndi madalitso ndipo zinachitika monga momwe kunanenedweratu.

"Ndi kosaloledwa kugwiritsa ntchito ijtihad m'chidziwitso cha itiqad, ndiko kuti, mu mfundo zoti zikhulupiridwe. Zimapereka mpata wopatuka ndi za m'maluwa. Ndi tchimo lalikulu. Pali njira imodzi yokha yolondola pa nkhani zokhudzana ndi chikhulupiriro yomwe ndi **Ahl as-Sunna wa'l Jamaa**. Kusiyana komwe kunanenedwa kuti ndi chifundo cha Allahu Taala mu Hadith ya Sharif kunali kusiyana kwa machitidwe.

"Pa nkhani yomwe zigamulo za madhhab onse anayi zikusiyana, chigamulo chimodzi chokha ndiye cholondola. Iwo amene amatsata njira yolondolayo adzapatsidwa thawab ziwiri, koma iwo omwe atsata njira imodzi mwa zigamulo zolakwikazo adzapatsidwa thawab imodzi Madhhab. Ichi ndi chifundo Allah. Ndi kololedwa kusiya madhhab imodzi ndi kutsatira chigamulo cha kachitidwe m'madhab ena. Koma, kupatula madhhab anayi odziwikawa, ndi kosaloledwa kutsatira madhhab aliwonse omwe adali a Ahl as-Sunna, ngakhale Sahabat al-Kiram, popeza madhhab amenewo sanalembedwe ndipo anayiwalika Tsopano ndi kosatheka kotsatira madhhab aliwonse kupatula anayi odziwikawa. Imam Abu Bakr Ahmad ar-Razi "rahimahallahu taala" (omwe anamwalira mchaka cha 980/370), nawo ananenanso kuti kunalengezedwa ndi akatswiri a Chisilamu mogwirizana kuti sikunali kololedwa kutsatira [mwachindunji] Sahabat al-Kiram. Ndikumema onse omwe akufuna kumvetsetsa bwino kupambana kwa madhhab, a mujtahid, makamaka a aimmat al-madhahib anayi kuti awerenge mabuku a **Al-mizan al-kubra** and **Al-mizan al-Khidriyya** olembedwa ndi Imam Abd al-Wahhab ash-Sharani "rahimahallahu taala".[1] Mmenemo azamva zoti madhhab awo sanachokere kwina kuli konse ndipo kuti malamulo omwe iwo

[1] Yusuf an-Nabhani**, Hujjat-Allahi alal-alamin**, p. 771. Mndandanda wa mau alembedwa apawu ndi otanthauzidwa kuchokera ku chi Arabu, omwe ali ndi zowonjezera kuchokera zochokera m'mabuku ena omwe anaikidwa m'mabulaketi monga momwe timachitira m'mabuku athu onse. Potero timakhala tikulekanitsa zobwerekera kuchokera ku mabuku ena ndi za ndi zomwe tikumasulira. Chiarabu choyambirira chinasindikizidwa pa makina a offset ku Istanbul m'chaka cha 1974/1394.

amkapereka kudzera mu ijma ndi qiyas sanali maganizo awo koma anali ochokera m'Buku ndi Sunna.

Ndi zolakwika kunena kuti, "Quran al-Karim sinena kuti 'za akatswiri a Chipembezo." Pali ma ayat angapo omwe amayamika akatswiri a chipembezo (Ulama) ndi maphunziro(ilm). Hazrat Abd al-Ghani an-Nablusi (yemwe anamwalira mchaka cha 1731/1143) analemba m'buku lake la kuti **Al-hadiqa**:

"Ayat ya chisanu ndi chiwiri ya Surah al-Anbiya yalamula kuti: '**Afunseni anthu a dhikr zimene simukuzidziwa**.' 'Dhikr' (kukumbukira Allahu Taala) ikutanthauza 'kudziwa'. Ayat al-karima iyi ikulamula omwe saphunzire kupeza akatswiri ndi kuphunzira kuchokera kwa iwo. Izi zikufotokozedwanso mu Ayat karima ya chisanu ndi chiwiri mu Surah Al Imran: **'Ndi odziwa okha omwe amamvetsetsa matanthauzo a ma ayat okuluwika'**; mu ayat karima 18 ya sura yomweyi: **'Zoti Allahu Taala alipo ndipo ngwamphamvu zoposa, ngwanzeru zakuya'**; mu ayat karima 82 mu Surah ya al-Qasas: "Anzeru anati kwa iwo; "**Manyazi akugwireni! Mphotho zomwe Allahu Taala adzawapatsa okhulupirira ndi ochita zabwino, ndi zabwino kuposa zabwino za padziko lino**"; mu ayat karima 56 ya Surah Rum: 'Ndipo amene apatsidwa nzeru ndi chikhulupiriro adzanena: "**Ndithu inu munakhala mchilamulo cha Allah kufikira tsiku louka ku imfa; Tsono ili ndi tsiku louka ku imfa koma inu simunali kudziwa**". Mu ayat karima 108 mu Surah ya Isra: **'ndithu anapatsidwa nzeru kale ikalakatulidwa kwa iwo Qur'an al-Karim, amagwa ndi zibwano zawo molambira. Ndipo amanena:**

**"Mbuye wathu Ngoyera! Ndithu, lonjezo la Mbuye wathu ndi lokwaniritsidwa!"**; m'ndime 54 ya Surah Haji: '…… **amene apatsidwa kuzindikira akumvetsa kuti Quran al-Karim ndi choonadi chochokera kwa Allahu Taala** mu ayat karima 49 mu Surah Ankabut: **'Quran al-Karim yakhazikika m'mitima ya amene apatsidwa nzeru'**; m'ndime ya chisanu ndi chimodzi (6) mu Surah Saba:**'Amene apatsidwa (dalitso la) Kudziwa akuzindikira kuti Quran al-Karim ndi yovumbulutsidwa kuchokera kwa Mbuye wako. Ndipo imawongolera ku njira ya Mwini Mphamvu zoposa; wotamandika.'**

Ayat karima ya khumi ndi imodzi (11) mu Surah al-Mujadala: **'Allah adzawakweza (ulemerero) mwa amene akhulupirira ndi amene apatsidwa nzeru m'Paradaiso'**; mu ayat karima 27 mu Surah al-Fatir: **'Ndi odziwa okha omwe amamuopa Allahu Taala'**; ndi mu Ayat karima ya 14 ya Sura al-Hujurat: **"Wopambana kwambiri mwa inu ndi amene amaopa kwambiri Allahu Taala."**

Zafotokozedwa mu Hadith yomwe yatchulidwa pa tsamba 365 m'buku lomweli la **Al-hadika** kuti: **" 'Allahu Taala, angelo ndi zolengedwa zonse**

**zimapempherera omwe amaphunzitsa anthu zabwino'; 'Patsiku lachiweruzo,kuoyamba aneneri, kenako akatswiri amaphunziro, kenako ofera chikhulupiriro adzapembedwera'; 'Oh anthu inu! Dziwani kuti maphunziro ata kupezeka pomvera kwa ophunzira';** ndipo **'Phunzirani maphunziro! Kuphunzira kudziwa ndi ibada. Mphunzitsi ndi wophunzira nzeru adzapatsidwa mphotho zofanana ndi mphoto ya jihad. Kuphunzitsa nzeru kuli ngati kupereka za chifundo. Kuphunzira Kudziwa kuchokera kwa katswiri kuli ngati kuchita tahajjud**, (Salah yomwe imaswalidwa pa mbuyo pa Isha. Salah ya usiku m'chigawo cha chitatu chomaliza cha usiku isanakwane fajr [pemphero la m'mawa]).' Tahir Bukhari, "rahimahullahu taala" yemwe anamwalira mchaka cha 1147/542) mlembi wa bukhu la fatwa lotchedwa **Khulasa**, analemba kuti: 'Kuwerenga mabuku a fiqh kumabweretsa thawab zambiri kuposa kuchita Swalah zoonjezera usiku. Ndi fardh kuphunzira ma fardh ndi haramu kuchokera kwa akatswiri kapena m'mabuku awo. Kuwerenga mabuku a fiqh ndicholenga chochita zomwe waphunzira kapena kuphunzitsa ena ndi bwino kuposa kuchita salat at-tasbih, yomwe ndi nafila (yowonjezera), pemphero lamwambo. Zanenedwa mu Hadith sharif: **'Kuphunzira kudziwa Ndikoyenera kuposa ntchito zonse zopembedza zowonjezera, chifukwa ndi kothandiza onse awiri, kwa wophunzitsa ndi kwa iwo amene adzawaphunzitsa'; 'Munthu amene amaphunzira kuti aphunzitse ena adzalipidwa ngati siddiqs (wa bwino; wonena zoona).'** Maphunziro a Chisilamu angaphunziridwe kuchokera ku a Mbuye ndi mabuku. Anthu amene amanena kuti mabuku achisilamu ndi ndondomeko zake ndi zosafunika ndi abodza kapena ndi ma zindiq, amene amanyenga Asilamu ndi kuwatsogolera ku chiwonongeko. Chidziwitso m'mabuku achipembedzo chimachokera mu **Quran al-Karim** ndi Hadith Sharif."

Allahu Taala anatumiza Mtumiki alaihi-salam kuti adzaphunzitse **Quran al-Karim**. Sahabah al-Kiram anaphunzira chidziwitso cha mu **Quran al-Karim** kuchokera kwa Rasulullah. Akatswiri a Chisilamu anaphunzira kuchokera kwa ma Sahabah al-Kiram, ndipo Asilamu onse anaphunzira kuchokera kwa akatswiri Achisilamu ndi mabuku awo. Zalengezedwa m'ma Hadith akuti: "**Kudziwa ndi a chuma. Kiyi wake ndi kufunsa ndi kuphunzira"; "Phunzirani ndipo phunzitsani kudziwa!"** "**Chilichonse chili ndi gwero lake. Gwero la taqwa ndi mitima ya ma 'arif**,' ndiponso **"Kuphunzitsa kudziwa ndi chiombolo ku machimo."**

Al-Imam ar-Rabbani (rahmat-Allahi Taala alaih) adalemba Kalata ya 193 ya voliyumu yoyamba ya **Maktubat** yake:

"Munthu wa **mukallaf,** (wa nzeru ndi wa chinyamata, wodalirika achipembedzo) choyamba ayenera kukonza iman ndi itiqad yake. Kutanthauza

kuti aphunzire maphunziro a chikhulupiriro zolembedwa ndi akatswiri a Ahl as-Sunna wa'l Jamaa ndi kukhulupirira moyenera. Tipemphe Allahu Taala kuti alipire malipiro ochuluka akatswiri akuluwa chifukwa cha ntchito zawo. Amin! Chipulumutso ku mazunzo a dziko lili mkudza chitengera zomwe akunena. - [Anthu amene akutsatira njira ya akatswiriwa amatchedwa **Sunni.]** Ndi okhawo amene akutsatira mapazi a Mtumiki "swallaallaahu 'alayhi wa aalihi wa sallam" ndi ma Sahaba ake "ridwanullahi alaihim ajmain".

Ziphunzitsa zolondola ndi za mtengo wapatali mwa zidziwitso zochokera m'Buku la **Quran al-Karim** ndi Sunna (Hadith Sharif), ndi ziphunzitso zomveka ndi zosimbidwa ndi akatswiri akuluakulu kuchokera m'Buku ndi Sunna. Popeza munthu aliyense wa bid'ah, (omwe akuti akukonzanso, aliyense wa mpatuko ndi wosatsata madhhabi) pofuna kuyipitsa ndi kunyoza akatswiri a Ahl as-Sunna, chifukwa cha umbuli wawo amati maganizo awo oipawo anatenga kuchokera m'Buku ndi Sunna. Monga tikuwonera, si mawu onse kapena zolembedwa zonse zomwe amati zachokera m'Buku ndi Sunna ziyenera kuvomerezedwa kuti ndi zolondola, komanso tisanyengedwe ndi mabodza awo odzikongoletsa.

"Pofotokoza chikhulupiriro cha akatswiri a Ahl as-Sunna wa'l Jamaa, buku la **al-Mutamad** ndi lofunika komanso ndi la mtengo wapatali. Bukhuli linalembedwa m'chinenero cha Chipezya ndi katswiri wa mkulu wa chisilamu wa fiqh mu madhhab a Hanafi, Hazrat Fadlullah bin Hasan Tur Pushti, yemwe anamwalira mu 1263/661. Bukhuli likufotokoza za chikhulupiriro chowona chiphunzitsidwa ndi akatswiri a Ahl as- Sunna. Ndi lolembedwa momveka bwino, choncho ndi zosavuta kumva. Bukulo linasindikizidwa ndi Hakikat Publishing mu 1989/1410.

"Titakhonza ziphunzitso zokhudzana ndi chikhulupiriro, tiyenera kuphunzira **halal** (zololedwa, zovomerezeka mu Chisilamu), **haram** (zoletsedwa mu Islam), **fardh** (malamulo mu Chisilamu), **wajib** (yofunikira, zokakamiza mu Chisilamu), **sunna** (zochita, zinthu zomwe sanalmulire Allahu Taala koma zomwe zinachitidwa ndi kukondedwa ndi Mtumiki wa Allah 'alaihi-salam ngati ibadah), **mandub** (zochita zolangizidwa, zopereka malipiro) ndi **makruh** (zinthu zosakondedwa, zonyansa) zochokera m'mabuku a fiqh olembedwa ndi akatswiri a Ahl as-Sunna ndi kuzichita mogwirizana ndi iwo (akatswiriwo). Tisawerenge mabuku ampatuko ofalitsidwa ndi mbuli zomwe sizimvetsa ukulu wa akatswiriwa. Asilamu omwe ali ndi chikhulupiriro chogwirizana ndi chikhulupiriro cha Ahl as-Sunna sazathawi moto wa Jahannama pa tsiku lomaliza - Allahu Taala titetezeni ife! Msilamu yemwe ali ndi chikhulupiriro cholondola, koma wofowoka pa ku pembedza, atha kudzakhululukidwa ngakhale atapanda kulape. Ngakhale atapanda khululukidwa, iwo

adzapulumutsidwa ku Jahannama pambuyo pa mazunzo. Cholinga chachikulu ndi kukonza chikhulupiriro chako. Khwaja Ubaidallah al-Ahrar qaddas-Allahu Taala sirrahul-aziz (yemwe anamwalira ku Samarkand m'chaka cha 1490/895) anati: 'Ndikadapatsidwa ma kashf onse (kuvumbulutsidwa zinsinsi za Umulungu) ndi ma karamah onse (za chilengedwe zodabwitsa za ma wali) koma ndi kumanidwa chikhulupiriro cha Ahl as-Sunnat wa'l Jamaa, ndikanazitenga ine kuti ndi wowonongeka. Ndikanakhala wopanda kashf kapena karama ndikukhala ndi zolakwa zambiri, koma ndikadapatsidwa chikhulupiliro cha Ahl as- Sunnat wa'lJamaa, sindikanamva chisoni.' "Makono Asilamu ku India ndi bwinja. Adani a Chisilamu akuwawukira paliponse. Lero ndalama yochepa yoperekedwa potumikira Chisilamu ikupereka thawab zambiri (mphoto zoperekedwa ndi umulungu pa tsiku la chiweruzo chifukwa cha ntchito zabwino) kuposa zikwi za ndalama zoperekedwa nthawi ina. Ntchito yaikulu yoti ichitike m'Chisilamu ndi kupeza mabuku a Ahl as-Sunna omwe akuphunzitsa chikhulupiriro ndi miyambo, komanso kuwagawa kwa anthu aku midzi ndi achinyamata. Anthu opindula kwambiri komanso amwayi ndi iwo omwe apatsidwa kugwira ntchito iyi. Ayenera kukondwera nayo ndipo kuthokoza kwambiri Allahu Taala chifukwa cha mwayi uwu. Nthawi zonse ndi bwino kutumikira Chisilamu. Koma pa nthawi ngati izi, pomwe Chisilamu chikufooketsedwa, pomwe kuwononga Chisilam kukulimbikitsidwa kudzera m'mabodza ndi ugogodi, ndikwabwino kwambiri kuyesetsa kufalitsa chikhulupiriro cha Ahl as-Sunna. Mtumiki "swallaallaahu 'alayhi wa aalihi wa sallam" anati kwa ma Sahaba ake: '**Mukukhala mu nthawi yakuti ngati mutamvera magawo asanu ndi anayi a magawo khumi a Malamulo a Allahu Taala ndi zoletsedwa zake koma ndi kunyozera chimodzi, inu mudzawononongeka. Mudzazunzidwa! Ndithu padzabwera nthawi yoti anthu okhulupirira gawo limodzi mwa magawo khumi a malamulo ndi zoletsedwa zake, adzakhululukidwa**.'[1]

Hadith sharifyi inkanena za nthawi ino. Ndi kofunika kulimbana[2] ndi anthu osakhulupirira. Kuwadziwa kuti iwowo ndi ndani ndi kuwapewa. Chifukwa kugawa mabuku ndi kufalitsa uthenga wa ophunzira akuluakulu a Ahl as-Sunna sikufunika kukhala munthu woziwa kapena wophunzira kwambiri ayi. Msilamu aliyense ayenera kuyetsetsa kuchita izi. Mwayi umenewu usaphonyedwe. Pa

[1] Mishkat-ul mesabih, vol. 1, p. 179; pa-Tirmizi, Kitab-al Fitan, chikalata cha 79.

[2] Jihad pigwiritsa ntchito mphamvu (jihad qatli) yomwe imapangidwa ndi Boma, pogwiritsa ntchito asilikali ake. Asilamu amene akuchita jihad imeneyi amagwira ntchito yomwe apatsidwa ndi boma. Koma monga zalembedwa mu kalata ya 65 ya **Maktubat**, pali jihad qawli, yomwe imapangidwa polankhula ndi kulemba. Ndi njira yabwino ndipo ili ndi thawab kuposa jihad qatli.

tsiku lachiweruzo, Msilamu aliyense adzafunsidwa pa izi ndipo adzafunsidwa chifukwa chomwe sanagwirire ntchito ya Chisilamu. Anthu omwe sathandiza kugawa mabuku ophunzitsa za Chisilamu ndi omwe sathandiza mabungwe omwe akugawa uthenga wa Chisilamu akazunzidwa momvetsa chisoni. Palibe zifukwa zikaloledwa posachita izi. Ngakhale aneneri alaihimus-salam anali apamwamba komanso anthu adziwika, iwo samasamalire za kumasuka kwa thupi lawo ndi zopinga zina. Pofalitsa chipembezo cha Allahu Taala, yomwe ndi njira ya kumtendere wosatha, anagwira ntchitoyi masana ndi usiku. Kwa omwe ankafunsa za zozizwitsa ankawayankha, '**Zozizwitsa zimalengedwa ndi Allahu Taala; ntchito yanga ndi kukuuzani za chipembezo chake.**' Pamene amagwira ntchito ndi cholinga chimenechi, Allahu Taala amawathandiza ndi kuwapatsa zozizwitsa. Ifenso tikuyenera kugawa mabukuwa ndi ziphunzitso za ophunzira akuluakulu a Ahl as-Sunna rahimahum-Allahu Taala ndi kuuza achinyamata ndi anzathu ochita zoipa ndi za chinyengo, osakhulupirira, adani ndi omwe amanyoza ndi kuzunza Asilamu.[1]

Anthu omwe sakugwira ntchitoyi kudzera mu chuma chawo, mphamvu kapena ma udindo awo sadzazemba mazunzo. Pogwira ntchitoyi, kuvutika ndi kuzunzidwa zitengedwa ngati chisangalalo komanso phindu lathu lalikulu. Pamene Atumiki Rasulullah "sallallahu taala alaihi wa sallam" ankauza anthu za malamulo a Allahu Taala, ankakumana ndi ziwopsyezo zochokera kwa mbuli ndi anthu ofooka mmaganizo. Anavutika kwambiri. Muhammad Rasulullah "sallallahu taala alaihi wa sallam" wokondedwa wa Allahu Taala yemwe anasankhidwa kukhala wapamwamba mwa anthu opambanawa adati: '**Palibe mneneri yemwe anazunzidwa ngati ine.**'"

Ophunzira akuluakulu a Ahl as-Sunna omwe a naonetsa njira yolondola kwa Asilamu pa dziko pano ndi kutitsogolera kuphunzira chipembezo cha Muhammad alaihi wa sallam popanda chosintha kapena kuononga, ndi ophunzira omwe anafika pa muyeso wa ijtihad wa ma madhhab anayi aja. Mwa akatswiri amenewa, anayi anali wotchuka kwambiri. Woyamba anali **al-Imam al-Azam Abu Hanifa Numan ibn Thabit** "rahimahallahu taala" Iye anali mmodzi mwa akukuakulu a Chisilamu. Anadzakhala mtsogoleri wa ahl as-Sunna.

[1] Kuwauza si miseche koma amr bil ma'ruf (ntchito yophunzitsa malamulo a Allahu Taala). Msilamu aliyense ayenera kuphunzira chikhulupiriro cha Ahl as-Sunna ndi kuphunzitsa kwa anthu omwe angawafikire. Mabuku, magazini ndi mapepala ofotokoza za chiphunzitso chaakatswiri a Ahl as-Sunna ziyenera kugulidwa ndi kutumizidwa kwa achinyamata ndi kwa owadziwa. Tiyesetse kuti awerenge zimenezo. Komanso mabuku ofotokoza zolinga zenizeni za adani a Chisilamu ayenera kugawidwa.

Anabadwira ku Kufa m'chaka cha 699/80 ndipo adaphedwa ku Baghdad m'chaka cha 767/150.[1]

Wachiwiri anali **Imam Malik ibn Anas** "rahimahallahu taala" yemwe anali wophunzira wamkulu kwambiri. M'bukhu la **Radd al-muhtar**, Ibn Abidin analemba kuti anakhala zaka 89 ku Medina kuchokera mchaka cha 708/90 mpaka 795/ 179. Agogo ake anali Malik bin Abi Amir.

Wachitatu anali **Imam Muhammad ibn Idrisash-Shafii** "rahimahallahu taala" amene ankalemekezedwa kwambiri ndi akatswiri a Chisilamu onse. Anabadwira ku Ghazza, dziko la Palestine, mu 767/150 ndipo anamwalirira ku Egypt mu 820/204.

Wachinayi ndi **Imam Ahmad ibn Hanbal** "rahimahallahu taala" Iye anabadwira ku Baghdad mu 780/164 ndipo anamwalirira komweko mchaka cha 855/241. Iyeyu ndi imodzi mwa 'msichi zikuluzikulu za chisilamu.'

Lero, munthu amene wosatsata m'modzi mwa ma imam anayi amenewa ali pa chiopsezo. Munthu wotero ali wopatuka. Kupatula ma imam anayiwa, palinso ophunzira ena a Ahl as-Sunna omwe anali ndi madhhab achilungamo. Koma ndi kupita kwa nthawi madhhab awo anaiwalika ndipo sakanaikidwa m'mabuku. Mwachitsanzo ophunzira akulu akulu aku Medinan omwe ankatchedwa **al-Fuqaha as-sab'a** ndi **Umar ibn Abd al-Aziz**, **Sufyan ibn Uyayna** (yemwe anamwalira ku Mecca mu 813/198), **Is'haq ibn Rahawayh**, **Dawud at-Tai, Amir ibn Sharahil ash-Shabi**, **Layth ibn Sad**, **Amash**, **Muhammad ibn Jarir at-Tabari**, **Sufyan ath-Thawri** (yemwe anamwalira ku Basra mchaka cha 778/161) ndi **Abd ar-Rahman Awzai** rahimahum-Allahu Taala ndi ena mwa iwo.

Ma Swahaba al-Kiram "radiyallahu taala anh" um ajmain onse anali "nyenyezi" potsogolera molondola. Aliyense mwa iwo pa yekha anali wokwanira kutsogolera dziko lonse ku njira yachiongoko. Anali ma mujtahid, aliyense akutsatira madhhab ake. Za mbiri m'Madhhab awo zinali zofanana. Koma poti ma **madhhab** awo sanalembedwe m'mabuku, ndi kovuta kwa ife kuwatsatira. Ma madhhab a ma imam anayi aja, zomwe anaphunzitsa pa zinthu zoyenera kukhulupirira ndi zomwe ziyenera kuchitidwa, zinasonkhanitsidwa ndi kufotokozeredwa ndi iwo eni komanso ndi ophunzira awo. Zinalembedwa m'mabuku. Lero msilamu aliyense ayenera kutsatira amodzi mwa ma madhhab

[1] Mbiri yake yafotokozedwa mwatsatanetsatane mu The Sunni Path komanso mu fascicle yoyamba ya Endless Bliss.

anayi atchulidwa pamwambawo. Adzikhala ndi kumapanga ibadat (miyambo yopembedzera) motengera madhhab omwe akutsatirawo[1].

Mwa ophunzira ama Imam anayi amenewa, omwe anadzakhala ophunzira akuluakulu nawo, awiri anafika pa muyeso wa pa mwamba kwambiri pofalitsa ziphunzitso za Iman, (zikhulupiriro za chisilamu. Choncho, pakhala ma madhhab awiri mu itiqad kapena **madhhab mu iman.** Chikulupiriro chotengera pa **Quran al-Karim** ndi Hadith Sharif ndi chokhacho choonetsedwa ndi ma imam awiriwa, omwe anafalitsa pa dziko lonse chikhulupiriro cha Ahl as-Sunna, lomwe ndi gulu la chipulumutso (al-Firqat an-Najiyya). Mmodzi wa iwo anali **Abu 'l-Hasan Ali al-Ash'ari** "rahimahallahu taala" ndipo anabadwira ku Basra m'chaka cha 879/226 ndikumwalirira ku Baghdad mu 941/330. Wina anali **Abu Mansur al-Maturidi** "rahimahallahu taala" Uyu anamwalirira ku Samarkand, mchaka cha 944/333. Polemekeza chikhulupiriro, msilamu aliyense ayenera kutsatira mmodzi mwa ma Imam opambana amenewa.

Turuq[2] (njira) za awliya[3] ndi zolondola. Ndi pang'ono pomwe sanasochere mu njira ya Chisilamu.[4] Awliya amapatsidwa karamat (zodabwitsa, ukatswiri wapadela wochokera kwa Allahu Taala). Karamat awo onse ndi omveka komanso owona. Al-Imam Abdullah al-Yafi'i (yemwe anamwalira ku Mecca mchaka cha 1367/76) Anati: "Zozizwa za Ghawth ath-Thaqalain Maulana Abd al-Qadir al-Jilani qaddas-Allahu Taala (yemwe anamwalirira ku Baghdad mu 1161/561, zakhala zoziwika moti palibe angazikaikire kapena kuzikana poti tawatur (mosatizana, kubwerezabwereza, zosakaikitsa,zowanda) ndi umboni wolemba wokhudza Zowona."

---

[1] Aliyense yemwe sakufuna kutsatira aliwonswe mwa madhhab anayiwa' iye alibe ubale ndi Ahl as-Sunna.

[2] Turuq ndi mchuluko wa mawu oti tariq/tariqa omwe akutanthauza kuti njira kapena malamulo a tasawwuf.

[3] awliya ndi mchuluko wa mawu oti wali ndipo akuthanthauza munthu wokondedwa komanso kutetezedwa ndi Allahu Taala

[4] Mu m'bado uliwonse pakhala pali abodza ndi opatuka omwe amagwiritsa ntchito Chipembedzo ngati njira yopezera zofuna zao za pa dziko lapansi. Iwo amobisalira ngati ndi awliya, murshid (alangizi okhwima mu uzimu) kapena ngati anthu okhala ndi udindo m'chipembedzo. Makono mu ntchito iliyonse muli anthu oipa. M'nthambi iliyonse ya za umisiri ngakhale pa udindo uliwonse pali anthu oyipa. Timaona anthu akupindula ndi kusangalala popondereza ena. Ndi kulakwa kapena ndi umbuli kunena kuti ntchito zonsezi ndi zoipa chifukwa muli anthu ena omwe ali oipa ogwira ntchitozi. Chimogzimodzi tisayankhule zoyipa za akatswiri a Chisilamu chifukwa choti pali ena omwe amazionetsera ngati ndi akatswiri koma ali opatuka ndi mbuli.

Ndi kulakwa kunena anthu oti akuswali "makafiri" pokhapokha iwo eni atanena popanda darura (kukakamizidwa) chinthu choonetsa kuti ndi osakhulupirira. Sitingawatemberere pokhapokha tili ndi umboni woti anamwalira ali wosakhulupirira. Sizololedwanso kutemberera munthu wosakhulupirira. Pa chifukwa ichi ndi bwino osatemberera Yazid (mwana wa mwamuna wa Hazrat Muawiye '"radiyallahu taala anh", yemwe anapha Hazrat Huseyin '"radiyallahu taala anh".)

5 - Msichi ya chisanu ndi chimodzi ya Iman ndi **"kukhulupirira tsiku Lomaliza (al-Yawm al-Akhir).**" Limayamba pa tsiku lomwe munthu wamwalira mpaka pakutha pa tsiku la chiweruzo. Limatchedwa "tsiku lomaliza" chifukwa sikudzakhalanso usiku pakatha pa tsiku ili komanso lidzabwera pakutha pa dzikoli. "Tsiku" ili, lomwe latchulidwa mu hadith sharif silidzakhala ngati tsiku kapena usiku womwe tikulidziwa. Limatanthauza kanthawi. Sizikudziwika kuti tsiku la chiweruzo lidzafika liti. Palibe amene angayerekeza za nthawi ya tsikuli. Koma Mtumiki "sallallahu taala alaihi wa sallam" anatchulapo zizindikiro ndi zisonyezo zambiri za tsikuli monga: kubwera kwa Hazrat al-Mahdi[1]; kutsikira kwa Isa alaihis-salam ku Damascus kuchokera kumwamba; Kuoneka kwa ad-Dajjal[2]; anthu otchedwa Yajuj ndi Majuj[3] adzabweretsa chisokoneza padziko lonse; dzuwa lidzatulukira ku madzulo ndi kulowera ku mmawa; zivomelezi za

[1] Hazrat al-Mahdi adzakhala wobadwa kuchokera ku mtundu wa Mtumiki wathu wodalitsika Muhammad alaihi-salam Dzina lake lidzakhala Muhammad ndipo dzina la bambo ake lidzakhala Abdullah. Adzatsogolera Asilamu, limbikitsa Chisilamu ndi kuchifalitsa paliponse. Adzakumana ndi Isa alaihi salam, Ndipo limodzi adzamenyana ndi kumupha Ad-Dajjal. Pa nthawi yake, Asilamu adzakhala paliponse ndi kukhala mu mtendere ndi momasuka.

[2] Ad-Dajjal (yemwe a Kristu amamutcha kuti Antikhrastu, amenenso adzatchedwa Mesiya chifukwa kutchuka kwake kudzafalikira pa dziko lonse lapansi) kudzakhala mwana wa Myuda waku Khurasan, kumpoto kwa Iran, koma mdani wa Chisilamu. Adzalamulira asilikali osawerengeka. Adzapha Asilamu, kusowetsa mtendere ndi bweretsa chisokonezo ku Middle East. Pambuyo pokhetsa mwazi wambiri, adzaphedwa ndi Hazrat Mahdi. Zinalembedwa ndi ma umboni m'buku la Mukhtasaru Tadhkirat al-Qurtubi lolembedwa ndi Abd al-Wahhab ash-Sha'rani ndipo lotulutsidwa ndi Hakikat Publishing mu 2000/1421) kuti dzina ad-Dajjal lidzakhala Ibn as-Sayyad.

[3] Kwalembedwa mu Quran al-Karim kuti Yajuj ndi Majuj (Gog ndi Magogi) ndi mitundu iwiri yoyipa, yomwe kalekalelo idatsekeredwa ndi chipupa. Iwo adzafalikira pa dziko poyandikira kutha kwa dziko. Poganizira kuti kafukufuku wa mabwinja wakhala akupeza mizinda yokwiririka pansi ndi yokwiriridwa pansi pa Nyanja, pa mwamba pa mapiri; chipopa chimenecho mwina chinapezaka ndipo anthu amenewo mwina anatuluka. Sayenera kukhala ochuluka kwambiri kuti tithe kuwawona kapena kuwadziwa lero; zikhoza kukhala kuti ena mwa anthu mabiliyoni alipo pano anachokera mwa makolo awiriwo ndipo akufalikira pa dziko lapansi ku malo awo sangadziwike lero.

mphamvu zidzachitika; nzeru za chipembezo zidzaiwalika; kuchimwa (fisq) komanso zinthu zoipa zidzachuluka; anthu osapemphera, amakhalidwe onyansa ndi osaona mtima adzakhala atsogoleri; Malamulo a Allahu Taala adzaletsedwa; zinthu za Haram zidzachitidwa pali ponse; moto udzachokera ku Yemen; nyanja zikuluzikulu ndi mapiri zidzagawika m'zidutswa; dzuwa ndi mwezi zidzada; nyanja zazikulu zidzasakanikirana kuwira ndi kudzauma.

Msilamu yemwe akuchita machimo amatchedwa **fasiq** (munthu yemwe amaphwanya malamulo a Chisilamu, wochimwa). Ma Fasiq ndi anthu osakhulupirira onse adzazunzidwa (azab) m'manda mwawo. Zinthu izi zikuyenera kukhulupiridwa ndithu. Akakwiliridwa m'manda, wakufa amakhala moyo wina wosadziwika womwe amasangalala kapena kuzunzika. Monga momwe zinanenedwera momveka bwino m'ma Hadith kuti Angelo awiri, **munkar** ndi **nakir**, omwe amabwera ngati anthu awiri oopsa, adzabwera m'manda kudzafunsa amafunso. Malinga ndi ophunzira ena, mafunso a m'manda adzakhala okhudza zina mwa za chikhulupiriro, koma ophunzira ena amanena kuti mafunsowa adzakhala pa zikhulupiriro zonse. Pa chifukwa ichi tiyenera kuphunzitsa ana athu mayankho a mafunso awa: Kodi Rabbi (Mlengi) wako ndani? Chipembezo chako ndi chiti? Kodi umma wako ndi uti? Buku lako Loyera ndi liti? Kodi qibla yako inali kuti? Kodi ma madhhhab ako mu itiqad (Iman) ndi amal(ntchito)anali ati? Zalembedwa mu **Tadhkirat al-Qurtubi** (bukhu lolembedwa ndi Muhammad Qurtubi Maliki, yemwe namwalira mu 1272/671) kuti omwe si a Sunni sadzatha kuyankha mafunsowa molondola. Manda a anthu omwe amayankha mafunsowa molondola amakula ndipo zenera lopita ku Mparadizo limatsekuka. Mmawa komanso madzulo aliwonse amaona malo awo amtsogolo aku Mparadizo ndipo Angelo amachitira zabwino ndi kuwawuza nkhani zabwino. Omwe amakanika kuyankha molondola, amakwapulidwa kwambiri ndi nyundo za chitsulo. Zolengedwa zonse kupatula munthu ndi ziwanda zimamva kulira kwawo. Manda awo amachepa mpaka amamva nthiti zawo zikugundana. Mabowo a ku Gahena amatsekulidwa. Mmawa ndi madzulo alionse amaona malo omwe akakhale ku Gahena. Amazunzidwa kwambiri m'manda mwawo mpaka Tsiku la kuuka kwa akufa.

Ndi zofunika kukhulupirira za kuuka kwa akufa [kuuka kwa akufa ndi kukhalaso ndi moyo pa Tsiku Lomaliza]. Thupi ndi mafupa zikadzavunda ndi kusanduka dothi ndi mpweya, zidzasonkhanitsidwanso; mizimu idzalowa m'mathupi momwe inkakhala ndipo anthu onse adzauka kuchokera m'manda awo[1]. Choncho nthawi iyi imatchedwa **Tsiku la Qiyama** (kuyima).

[1] Zomera zimayamwa mpweya wa Kaboni Diyiokosidi kuchokera mu mlengalenga ndi madzi ndi michere (mineral zinthu) kuchokera m'nthaka ndi kuzigwirizanitsa ndi kupanga

Zolengedwa za moyo zonse zidzasonkhana pa **Mahshar** (malo osonkhanilana) patsiku lomaliza. Aliyense adzapatsidwa mabuku a ntchito zake. Allahu Taala Wamphamvu zonse, Mlengi wa dziko la pansi, ku mwamba, nyenyezi ndi zonse adzapangitsa kuti izi zitheke. Mtumiki wake “sallallahu taala alaihi wa sallam” ananena kuti izi zidzachitika. Ndizachidziwikire kuti zomwe ananena ndi zoona. Zonse zidzachitika ndithu.

Mabuku a ntchito za ma Salih (anthu oopa Mulungu, anthu abwino) adzapatsidwa ma buku awo kuchokera ku dzanja la manja, ndipo ma fasiq (ochimwa, anthu oipa) adzapatsidwa mabuku awo kuchokera kumbuyo kapena kuti dzanja la manzere. Ntchito iliyonse, yabwino kapena yoipa, yaikulu kapena yaying’ono, yochitika mwachinsinsi kapena mowonekera, zidzakhala zitalembedwa m’buku limenelo. Ngakhale ntchito zomwe angelo otchedwa kiraman katibin sadazidziwe, zidzaululika ndi ziwalo zomwe zinali mboni po ngwira ntchitozo komanso Allahu Taala yemwe amadziwa chilichonse. Kudzakhala kufunsidwa komanso kuweruza pa ntchito iliyonse. Pa Tsiku la Chiweruzo, ntchito iliyonse yachinsisi idzaululika ngati Allahu Taala adzafune kuti zitero. Angelo adzafunsidwa pa zomwe anachita pa dziko komanso ku mwamba. Atumiki alaihimus-salam adzafunsidwa momwe anaperekera uthenga wa Allahu Taala kwa anthu ndipo anthu adzafunsidwa momwe adawalandirira atumiki, momwe adakwanilitsira udindo wawo pa zomwe zinavumbulutsidwa kwa iwo komanso mmene adalemekezera ufulu wa wina ndi mnzake. Pa Tsiku la Chiweruzo, anthu omwe ali ndi Iman ndipo ntchito ndi makhalidwe awo abwino, adzapatsidwa mphoto ndi madalitso, ndipo anthu amakhalidwe oyipa ndi ochimwa adzalangidwa kwambiri.

Allahu Taala, wopereka zochuluka ndi wa chifundo, adzakhululuka machimo a Asilamu omwe adzafune kuwakhululukira. Adzakhululuka tchimo lililonse akadzafuna kupatula ukafr (kukanila) ndi shirk (kupembedza kapena kupembedzera wina aliyense kapena china kusiya Allahu Taala), ndipo adzalanga tchimo angakhale laling'ono akadzafuna. Allahu Taala wanena kuti oyense wakufa ali kafr kapena wa shirk sadzakhululukiridwa. Anthu osakhulupirira omwe ali ndi omwe alibe buku lovumbulutsidwa, omwe sakhulupirira kuti Muhammad “sallallahu taala alaihi wa sallam” ndi Mtumiki

---

zinthu (organic) za moyo za ziwalo zathu. Zikudziwika tsopano kuti zotsatira za kusakaniza kwa mankhwala zomwe zimatenga zaka kuti ziziwike, zitha kuchitika mma sekondi ochepa pogwiritsa ntchito catalyst. Chimodzimodzi Allahu Taala adzagwirizanitsa madzi, mphweya wa carbon dioxide ndi michere m'manda ndi kulenga ziduswa zomwe zizapanga ziwalo za mathupi m'kasekandi. Mukhbir as-sadiq (Mtolankhani wowona, Mtumiki ) ananena kuti ife tidzabwera m’moyo winawo mmene tikuonekeramu. Mmene ziliri, sayansi imatsimikizira kuti izi zikuchitika kale m'dziko lino.

wa anthu onse ndi omwe savomereza angakhale lamulo lake ndi limodzi lomwe anapereka, akaikidwa ku Gahena ndi kuzunzidwa kwamuyaya.

Pa Tsiku La Chiweruzo kudzakhala **Mizan** (sikelo), zosiyana ndi zomwe timazidziwazi, zoyezera ntchito ndi makhalidwe athu. Zidzakhala zazikulu kwambiri kuti koti sikelo imodzi itha kunyamula dziko lonse ndi kumitambo komwe. Sikelo ya ntchito zabwino idzakhala yowala ndipo idzakhala ku manja kwa Arsh komwe kuli Mparadizo. Sikelo ya machimo idzakhala yakuda ndipo idzakala ku manzere kwa Arsh komwe Gahena ili. Ntchito, mawu, maganizo ndi maonekedwe ochitika pa dziko lino zidzaoneka ndi maso pa pamenepo, ntchito zabwino zikuwala pomwe ntchito zoipa zikuoneka zakuda ndi zonyasa. Zidzayezedwa pa sikelo zomwe zidzakhale zosafanana ndi za m'dzikoli. Zidanenedwa kuti sikelo yonyamula zolemera idzakwera ndipo yonyamula zopewuka idzatsika. Malinga ndi ophunzira kwambiri za chisilamu ena, akuti padzakhala miyezo yosiyanasiyana. Ena ambiri anati : "M'Chisilamu sizinaonetsedwe mwatchutchutchu za kuchuluka kwa ma sikelo komanso mmene masikelowo adzagwirire ntchito, ndipo ndi kwabwino osaziganizira kwambiri."

Kudzakhala mulatho wotchedwa **Sirat** (njira) womwe udzamangidwe pa mwamba pa Gahena ndi lamulo la Allahu Taala. Aliyense adzalamulidwa kudutse pa mulathowo. Pa tsikulo, Atumiki onse adzachonderera: "Oh Allah! Titetezeni!" Anthu oyenera kukalowa ku Mparadizo adzadutsa pa mulathowo mosavuta ndi kukalowa ku Mparadizo. Ena mwa iwo adzadutsa ndi liwiro ngati chiphaliwali, ena ngati mphepo ndipo ena ngati kavalo wothamanga. Mulatho wa Sirat udzakhala woning'a kwambiri ngati tsitsi ndi wakuthwa koposa lupanga. Kukhala makhalidwe a Chisilamu pa dziko pano kuli ndi mbali yofanana; Kutsatira Chisilamu kuli ngati kuwoloka pa Sirat. Omwe amapirira ndi zovuta a zilakolako (zomwe zimadza ndi zikhumbo za mtima) pa dziko pano, adzadutsa pa mulathowo mosavuta. Omwe satsatira Chisilamu chifukwa cha zilakolako za thupi adzavutika kuwoloka mulatho wa Sirat. Pa chifukwa ichi, njira yosonyezedwa ndi chisilamu imatchulidwa "**Sirat al-Mustaqim"** (Njira yowona) ya Allahu Taala. Kufanana kwa m'mainauku kuonetsa kuti kukhala m'njira ya chisilamu kuli ngati kuoloka pa Sirat. Onse oyenera kukalowa ku Gahena adzagwera mu Gahena podutsa pa Sirat.

Kudzakhala thawale lotchedwa **Hawd al-Kawthar** (Mtsinje wa madzi okoma kwambiri ku Mparadaizo) lomwe linasungidwa kusungira bwana wathu Muhammad Mustafa "sallallahu taala alaihi wa sallam" Lidzakhala lalikulu ngati ulendo wa mwezi umodzi. Madzi ake adzakhala oyera kuposa mkaka, ndipo fungo lake labwino kuposa musk (zonunkhiritsa). M'bali mwake

mudzazunguliridwa ndi matambula ochuluka kuposa nyenyezi. Yemwe angamwe madzi ake sangakhalenso ndi luzu ngakhale atakhala ku Gahena.

Tiyenera kukhulupirira kuti kudzakhala **shafaa** (kupempha m'malo mwa..). Atumiki, awliya, Asilamu oyera, Angelo ndi ena omwe adzaloledwe ndi Allahu Taala adzapempha chikhululuko pa machimo akulu kapena ang'ono a Asilamu omwe anamwalira osalapa ndipo, mapemphero awo adzavomeredwa. [Mtumiki wathu "sallallahu taala alaihi wa sallam" ananena kuti **"Ndidzawapemphera chikhululuko kwa anthu a umma wanga omwe akuchita machimo akulu.**"] Mu dziko lomwe lili nkudza, kupemphaku kudzakhala kwa mitundu isanu:

Koyamba, kutopa ndi kudikirira kwa nthawi yayitali kwa ochimwa pa malo a Chiweruzo; adzalira ndi kupempha kuti kuweruza kuyambike. Padzakhala kuwapemphera pa izi.

Kwa chiwiri, kudzakhala kupempha kuti kufunsa mafunso kuchitike mwachangu ndi mosavuta.

Kwa chitatu, kudzakhala kupempha, kupemphera Asilamu kuti asagwe pa Sirat kugwra m'moto kotero kuti adzapulumutsidwe ku mazunzo a ku Gahena.

Kwa chinayi, kudzakhala kupempha kuti Asilamu amachimo aakulu kuti achotsedwe ku moto wa Gahena.

Kwa chisanu**,** Kudzakhala kupempha kuti Asilamu aikidwe ku mzinda wa pamwamba wa ku Mparadizo. Ngakhale kuti ku Mparadizo kudzakhala zabwino zosawerengeka ndi zosatha, koma kudzakhala mizinda (ma giredi) asanu ndi atatu. Giredi ya munthu aliyense idzakhala malinga ndi mmene chikhulupiriro chake chinalili, komanso ntchito zake.

Mparadizo ndi Gahena zilipo panopo. Mparadizo uli pa mwamba pa mitambo isanu ndi iwiri. Gahena ili pansi pa chilichonse. Pali ma Mparadizo asanu ndi anayi (8) ndi ma Gahena asanu ndi awiri (7). Mparadizo ndi waukulu kuposa dziko la pansi, dzuwa ndi mitambo, ndipo Gahena ndi yokulirapo kuposa dzuwa.

6 - Msichi yomaliza ya imman ndi "**kukhulupirira mu qadar, kuti zabwino (khair) ndi zoipa (sharr) zimachokera kwa Allahu Taala**." Zabwino ndi zoipa, mwayi ndi tsoka, kuluza ndi kupambana zomwe zimampeza anthu zimatheka ndi chifuniro Chake. M'buku lotanthauzira mawu, **'qadar'** imatanthauza 'kuyesa kuchuluka; chiganizo, lamulo; kuchuluka ndi kukula.' Chifuniro cha Allahu Taala chamuyaya choti chinthu chikhale chimatchedwa **qada** (kukonzeredweratu). [Mwachitsanzo] kupezeka kwa qadar, kapena kuti chinthu chinafunacho, kumatchedwa **qada**. Mau oti qada ndi qadar amagwiritsidwanso ntchito ngati

mawu amodzi. Choncho, qada ikutanthauza kukonzeratu kwa Allahu Taala mu umuyaya wa zinthu zomwe zalengedwa ndi zomwe zidzalengedwa kuchokera mu umuyaya wakale mpaka kutsogolo kosatha ndipo qadar ikuthanthauza [mwachitsanzo] kulengedwa kwa chirichonse mogwirizana ndi qada, osachotsera kapena kuonjezera. Kale lamuyaya, Allahu anadziwiratu chilichonse chomwe chidzachitike. Kudziwa kwa Allahu Taala uku kumatchedwa qada ndi qadar. Katswiri wanzeru zakuya pa maphunziro wakale wa ku Greece anakutcha kudziwa uku kuti al-inayat al-azaliyya (chisomo cha muyaya). Zolengedwa zonse zidachokera mu **qada.** Komanso kulengedwa kwa zinthu mu kudziwa kwake kwa kale kamuyaya kumatchedwa **qada** ndi **qadar**. Pokhulupirira mu qadar tiyenera kudziwa ndi kukhulupirira kuti akanafuna muyaya kuti alenge chinthu, chikuyenera kukhala mofanana ndi momwe Iye anafunira kuti chikhalire, mosachotsera kapena kuonjezera. Ndi kosatheka kuti kusapezeke zinthu zomwe Wafuna kulenga kapena kupezeka kwa zinthu zomwe sanafune kulenga.

Nyama zonse, zomera, zinthu zopanda moyo [zolimba, zamadzi, mphweya, nyenyezi,kuyenda kwa cholengedwa chirichonse] zopezeka kapena zosapezeka pa chilichonse, ntchito zabwino ndi zoipa za anthu, chilango chawo pa dziko pano ndi ku dziko lomwe lili nkudza, ndi china chilichonse chinalipo kale la muyaya mukuzindikira kwa Allahu Taala. Ankazidziwa zonse kwa muyaya. Zinthu zomwe zinachitika mu kale la muyaya komanso zomwe zingadzachitike m'tsogolo la muyaya, momwe zinthuzo zinachitikira ndi momwe zidzachitikire zalengedwa ndi Iye molingana ndi kufuna kwake. Ntchito zonse za bwino ndi zoipa za anthu, chikhulupiriro chawo kapena kusakhulupirira kwao m'Chisilamu, zochita zao zonse, zochita mofuna kapena mosafuna, zonse zimalengedwa ndi Allahu Taala. Iye yekha ndi amene amalenga ndi kupanga chilichonse, Iye amalenga zinthu zomwe zimachitika kudzera munjira Yake. **Allahu Taala amalenga chirichonse kudzera mu kudziwa kwake.**

Mwa chitsanzo, moto umayaka. Koma ndi Allahu Taala yemwe amalenga kuyaka. Moto si ukukhudzana kuyaka. Koma chikhalidwe Chake ndi choti ngati moto sukhudza kanthu, Iye salenga kuyaka[1]. Allahu Taala Yekha ndi amene

[1] Wophunzira ku yunivesite amaganizira mphamvu komanso chirichonse chingatenge malo. Zikuoneka kuti pomwe munthu akudziwa zambiri, ndi pamene akuyandikira ndi kuzindikira kuti pali zambiri zomwe zoyambitsa kuti chinthu chichitike. Atumiki alaihimusalam, omwe anali pa mlingo wa pamwamba kwambiri pa kuzindikira ndi sayansi ndi kumatha kuona zenizeni za chilichonse ndi akatswiri a Chisilamu omwe ankatsatira m'mapazi a anthu otchukawo, omwe anapeza ma dontho kuchokera m'nyanja za kudziwa anawonetsa kuti chilichonse mwa zinthu zomwe zikuyenera kuyaka kapena kumangidwa

amalenga kuyaka. Atha kuyatsa chinthu popanda moto koma Chikhalidwe chake koyatsa ndi moto. Ngati wafuna kuti asayatse, amaletsa kupsa ngakhale moto ulipo. Sanawotche Ibrahim (Abraham) alaihi-salam m'moto; chifukwa chomukonda kwambiri, adaimitsa Chikhalidwe chake chootcha.[1]

Allahu Taala akanafuna akanatha kulenga popanda njira, kuyatsa popanda moto, kutikhutitsa ndikutipatsa mphamvu popanda chakudya, kutipanga kuti tiziuluka popanda ndege ndi kumva zinthu za kutali popanda wailesi. Koma anachitira anthu chisomo polenga chilichonse kudzera mu china chake. Anafuna kulenga zinthu zina podzera ku zinthu zina. Ntchito zake zimadzera mu zina. Mpamvu zake zabisika mu zodutsiramo. Yemwe angafune kuti Allahu Taala alenge china chake amagwiritsa ntchito chodutsiracho ndipo amapeza chomwe akufunacho[2].

Ntchito za Allahu Taala zikanakhala kuti zinalengedwa popanda modzera, palibe munthu akanafuna mnzake, aliyense bwenzi akupempha chilichonse mwachindunji kwa Iye ndipo sibwenzi akufuna chinthu kwa aliyense. Kukanakhala kopanda ubale pakati pa anthu monga bwana ndi wa ntchito wake, folomani ndi omuthandizira, mphunzitsi ndi ophunzira ndi zina zotero. Kukanakhala chisokonezo pa dzikoli ndi dziko lomwe lili nkudza, ndipo sipakanakhala kusiyana pakati pa zokongola ndi zonyansa, chabwino ndi choipa, aulemu ndi amwano.

Akanafuna Allahu Taala akanafuna akanatha kulenga Chikhalidwe chakechi mu njira ina. Ndipo akadalenga chilichonse potengera njira imeneyo. Mwachitsanzo, akanafuna, akanatha kuyika onse osakhulupirira, okonda

---

tsopano ndi zosatheka komanso njira zoyipa zoyambitsa ndi zolengedwa.Ndipo kuti mwini kupanga, mwini kulenga si mkhalapakati koma Allahu Taala.

[1] Kunena zoona, Allahu Taala amalenganso zinthu zomwe zimalepheretsa moto kuyaka. Akatswiri a Kemestile akhala akupeza zinthu zimenezi.

[2] Amene akufuna kuyatsa nyali amagwiritsa ntchito machesi; amene akufuna kuyenga mafuta azitona amagwiritsa ntchito zida zophwanyira; omwe akumva mutu amamwa asupurin; amene akufuna kupita ku Paradiso kuti akapeze zabwino zosatha amatsatira Chisilamu; amene adziwombere yekha ndi mufti kapena kumwa poizoni adzafa; amene amamwa madzi ali ndi thukuta amaononga thanzi lawo; amene akuchita machimo ndi kutaya umunthu wawo adzapita ku Gahena. Chilichonse chomwe munthu angagwiritse ntchito, adzalandira chinthu chimene mkhalapakati wake anapangidwira kukhala njira yake. Amene amawerengani mabuku a Chisilamu amaphunzira Chisilamu, amachiyamikira, ndipo amakhala a Silamu. Amene akukhala pakati pa anthu osapembedza kapena amene satsata madhhab, ndikumamvera zomwe akunena, amakhala mbuli za Chisilamu. Ambiri omwe sadziwa Chisilamu amakhala Osakhulupirira. Munthu akakwera basi amapita kumwe basiyo ikupita.

zisangalalo za pa dziko, ozunza anzao ndi achinyengo ku Mparadizo, ndi kuyika onse olungama, opemphera ndi achifundo ku Gahena. Koma ma ayah ndi ma hadith akuonetsa kuti Allahu Taala sanafune choncho.

Allahu Taala ndi amene amalenga mwa munthu machitidwe a zinthu mwakufuna kapena mwaufulu ndi zomwe amachita mosafuna. Analenga **ikhtiyar** (chisankho) ndi **irada** (kufuna) mwa anthu polenga zochita zao mofuna, zochita mwakufuna kwao, ndikupanga chisankho ndi kufuna kukhala njira yolengera zochita zao. Munthu akafuna kuchita chinthu, Allahu Taala amalenga chofuna kuchitacho ngati wafuna.Ngati munthu safuna kuchita ndipo Allahu sanafune, Iye salenga chinthuncho. Salenga chifukwa choti munthu wafuna ayi, koma ngati Iyenso wafuna. Kulenga kwake kwa zofuna za munthu kukufanana ngati momwe moto ungagundire chinthu pomwe Allahu Taala amalenga kuyaka kwa chinthucho. Ndipo ngati moto siugunda chinthucho, Iye salenga kuyaka. Pamene mpeni wagunda chinthu, iye amalenga kudula. Si mpeniwo womwe umadula ayi koma Allahu Taala ndi amene amalenga kudula. Wapanga mpeniwo kukhala njira yodulira. Mwa njira ina, Iye amalenga zochitika za munthu mwa chisankho pa chifukwa (sabab) chomwe munthuyo ali nacho, amakonda, ndipo amazifuna zochita zimenezi. Koma zoyenda za chilengedwe sizidalira kufuna kapena kusafuna kwa munthu, koma zimalengedwa kudzera mu zoyambitsa zina pamene Allahu Taala yekha wafuna kuzilenga. Palibe olenga wina kupatula Allahu Taala, ndipo Yekhayo ndi amene amalenga kuyenda kwa chiri chonse: dzuwa, madontho a madzi, ma gelemusi ndi zina zosiyanasiyana. Komabe pali kusiyana pakati pa kayendedwe ka zinthu zopanda moyo ndi zochita mwakufuna mwa munthu ndi nyama: Munthu kapena nyama zikafuna kuchita chinthu ndipo Allahu Taala wafuna, Allahu Taala amalenga chinthucho. Zochita za munthu sizili mu mphamvu yake. Ndipo sadziwanso kuti chinthucho amachipanga motani[1]. Zinthu zosayenda zilibe chisankho choti ziyende kapena ayi. Allahu Taala amalenga kuyaka pamene moto wagunda pa chinthu, si motowo omwe umasankha kuyatsa kapena kuwotcha ayi.[2]

---

[1] Chochita munthu chirichonse ndi zotsatira za zochitika zambiri za kuthupi ndi mankhwala.

[2] Nayenso Allahu Taala amafuna ndi kulenga zabwino, zofuna zothandiza za anthu Ake olengedwa amene Iye amawakonda ndi kuwamvera chisoni. Iye safuna kapena kulenga kukwaniritsidwa kwa zokhumba zawo zoipa ndi zowononga. Nthawi zonse ntchito zabwino, zochitika zofunika zimachitidwa ndi anthu okondedwawa. Pali zambiri zomwe amadandaula kuti analephera kuchita koma akanaganiza ndi kuziwa kuti ntchitozo sizinalengedwe pachifukwa choti mwina zikanakhala zowononga, sabwenzi atadandaula mpang'ono pomwe. M'malo mwake, akanasangalala ndi kuthokoza Allahu Taala, Yemwe mu umuyaya Mwake anafuna kuti alenge zochita za anthu mwachisankho pamwe mitima

Zochita zosankha za munthu zimachitika pambuyo pa zinthu ziwiri. Choyamba, chisankho cha mtima wake, kufuna ndi mpamvu zake zimafunika. Pachifukwa ichi, zochita za munthu zimatchedwa **kasb** (kupeza), chomwe ndi chizindikiro cha munthu. Chachiwiri, kulenga kwa Allahu Taala kumachitika. Malamulo ake, zoletsa, malipiro ndi mazunzo zimachitika chifukwa choti kasb yaperekedwa kwa munthu. Mu ayah 96 Sura as-Saffat, Allahu Taala akuti: **"Wakulengani inu ndi zochita zanu."** Ayah iyi ikuonetsa kupezeka kwa kasb komanso chisankho cha mtima ndi **iradat juziyya** (ufulu wakudzisankhira) muzochita za munthu ndi umboni wa kusapezeka kwa kukakamizidwa. Pachifukwa ichi, [zochita zimatengera munthu] ndipo zitha kunenedwa kuti "zochita za munthu" monga timanenera kuti "Ali anagunda ndi kuthyola" Komanso Ayah iyi ikuonetsa kuti chilichonse chimalengedwa ndi qada ndi qadar.

Zanenedwa kuti kasb imayambitsa ndipo imakhala ndi gawo pa kulenga kwa zochita. Koma sikungakhale kulakwa kunena kuti kasb ilibe gawo pa kulenga zochita zomwe munthu angathe kusankha poti chotita chimafunidwa ndi munthu ndipo zomwe zimalengedwa si zosiyana ndi china ndi chinzake. Kotero munthu sangachite chilichonse akufuna; zinthu zomwe iye safuna zitha kuchitikanso. Zikanakhala kuti munthu atha kuchita chirichonse chomwe akufuna ndipo chirichonse chomwe samafuna chisachitike, iye sakanakhala munthu. Akanadzipatsa umulungu. Pomvera chisoni ndi kuwakondera anthu, Allahu Taala anawapatsa mphamvu zokwanira pa zofuna zao komanso zoti zigwirizane ndi kuchita malamulo Ake ndi zoletsedwa. Mwachitsanzo, munthu yemwe ali ndi thanzi komanso ndi chuma atha kupanga hajj kamodzi pa moyo wake; atha kusala mu mwezi wa Ramadhan; atha kuswali kasanu patsiku; yemwe ali ndi chuma chokwanira atha kulipira Zakah ngati chuma chake chafika pa mulingo wa nisab. [Nisab ndi chuma chochepa chimene Msilamu ayenera kukhala nacho,atawerengera ndalama zimene akufunakugwiritsa ntchito pa chaka, kuti akhale woyenerera kupereka zakat.] Choncho, munthu amachita zinthu zomwe wafuna ngati wafuna kutero ndipo ngati safuna kuchita izi, sachita. Ukulu wa Allahu Taala umaonekera apa. Chifukwa choti mbuli ndi zitsiru sizingamvetse nzeru za qada ndi qadar, sizimakhulupirira zomwe ophunzira akuluakulu a Ahl as-Sunna ananena ndipo zimakaika za mphamvu ndi kusankha komwe kuli mwa munthu. Amaganiza kuti munthu ndi wosatha ndipo

yawo inasankha ndi kuzifuna; Anafuna kutero. Akanakhala kuti sanafune kutero muyaya, nthawi zonse bwenzi akulenga ngakhale zochita zathu mwachichisankho mokakamiza, popanda ife kuzifuna. Kulenga kwake zochita zathu ife titazifuna ndi chifukwa chakuti anafuna kutero kale lamuyaya. Kenako, Chinthu chomwe chili cholamula ndi kufuna kwa Allahu Taala.

amakakamizikadwa mu kasankhidwe kake ka zochita. Poona kuti nthawi zina munthu sangasakhe kuchita zofuna zake, iwowa amanyoza za Ahl as-Sunna. Mawu olakwika ngati amenewo amaonetsa kuti ali ndi kusankha komanso kufuna.

Kukwanitsa kupanga kapena kukanika kupanga chinthu ndi nkhani ya **qudra** (mphamvu). Kusankha kuchita kapena kusachita chinthu kumatchedwa **ikhtiyar** (chisankho). Kufuna kupanga chomwe wasankha kuchita kumatchedwa **irada** (funo). Kuvomereza chinthu kapena kuchikana kumatchedwa **rida** (chilolezo). Mphamvu ndi kufuna zikakumana pa chifukwa choti ndi zabwino kuti china chichitike, **Khalq** (kulenga) kumachitika. Koma zikakumana pa modzi pomwe palibe chabwino choti chichitike, zimatchedwa **kasb** (kupeza). Aliyense yemwe amasankha kanthu si mlengi. Chimodzimodzi chilichonse chofunidwa sichili choyenera chilolezo kwenikweni. Allahu Taala amatchedwa **Khaliq** (Mlengi) ndi **Mukhtar** (yemwe ali ndi kusankha), ndipo munthu ndi **kasib** (wokhala ndi kasb) ndi mukhtar (wokhala ndi kusankha).

Allahu Taala amafuna ndi kulenga ma taat (zinthu zomwe Allahu Taala Wakonda) ndi machimo a anthu. Koma amapereka chilolezo ku ma taat ndi kusakonda matchimo. Chilichonse chimapezeka muchifuniro cha Allahu Taala ndi kulenga Kwake. Mu ayah 102 ya Sura al-Anam, Wanane kuti: "**Palibe mulungu koma Allah, Mlengi yekhayo wa chilichonse**."

Anthu achinyengo a gulu la **Mutazila**, polephera kusiyanitsa pakati pa kufuna ndi chilolezo, anabalalika ndikunena: "Munthu amalenga zochita zake yekha." Anakana qada ndi qadar. Gulu lina [lopatuka] lotchedwa **Jabriyya** ndiye linabalalika kotheratu; sanamvetse kuti patha kukhala kusankha koma popanda kulenga. Poganiza kuti munthu alibe kusankha mwa iye, anafanizira munthu ku mwala ndi nkhuni. Tipemphe Allahu Taala kuti atiteteze kwa opatuka omwe amati: "Anthu si ochimwa. Allah ndi Yemwe amapangitsa kuti zoipa zichitidwe." Kukanakhala kuti panalibe kufuna ndi kusankha mwa munthu ndipo ngati Allahu Taala ndi yemwe amayambitsa zoipa ndi machimo mokakamiza ngati momwe anaanenera mamembala a Jabriyya. Sipakanakhala kusiyana pakati pa mayenda a muthu yemwe wa ponyedwa kuchokera pa phiri atamangidwa manja ndi miyendo yake ndi yemwe akutsika Phiri payekha. Zoona ndi zoti womangidwayo akakamizika kugubuduzika popita pansi ndipo wosamangidwayo adzitsetsereka mwachifunira chake ndi kusankha modutsa. Anthu omwe sangaone kusiyana kwa anthu awiriwa ndi operewera nzeru komanso omwe akukana ma ayah. Amatenga malamulo a Allahu Taala ndi zinthu zomwe Waletsa ngati zinthu zosayenerera Poganiza kuti munthu amalenga zomwe wafuna, monga gulu la Mutazila (lotchedwanso Qadariyya) limakhulupirira, ndikukanila ayah al-Karima yomwe ikuti "**Allah yekha ndi**

**Mlengi wa zonse**." Uku ndi chimodzimodzi kuphatikiza munthu kukhala mtandizi wa Allahu Taala polenga.

Ma Shiya nawo monga Mutazila, amanena kuti munthu amalenga zomwe akufuna. Ngati umboni, iwo amati bulu sangaoloke mtsinje ngakhale atakwapulidwa chotani. Iwo saganizira komwe zoti munthu atafuna kuchita chinthu ndipo kuti Allahu Taala sakufuna kuti chinthucho chichitike, chifuniro cha Allahu Taala chimachitika. Mfundo ya ma Mutazila ndi yolakwika; munthu sangalenge kapena kuchita chilichonse chomwe akufuna. Zikadakakhala kuti zilizonse zomwe munthu wafuna zimatheka ngati mmene akunenera iwowo ndiye kuti Allahu Taala anakakhala wosatha. Allahu Taala sangakhale wosatha. Zokhazo zomwe wafuna Allahu Taala ndi zomwe zimatheka. Iye Yekha ndi yemwe amalenga chilichonse, ameneyo ndiye Allahu Taala. Ndi zonyansa kwambiri kunena ndi kulemba mawu oti, "Munthu analenga ichi," "Ife tinalenga icho," kapena "Awo analenga icho[1]." Uwu ndi mwano kwa Allahu Taala. Izi zimayambitsa kutaya chikhulupiriro.

## -5-

# KUFUNIKA KOGWIRITSA NTCHITO NJIRA

### MAKALATA AWIRI A

### SHARAF AD DIN MUNIRI "rahimahallahu taala"

Sharaf ad-din Ahmad ibn Yahya Muniri "rahmatallahi alaih" (omwe anamwalira mu 1380/782), mmodzi mwa Asilamu ophunzira akuluakulu

[1] Monga tafotokozera pamwambapa, zochita za munthu zosankha zimachitika kudzera mu zambiri zochitika za kuthupi, za mankhwala ndi za mmaganizo, zomwe sizidalira chifuniro chake ndipo nthawi zina sazindikira nkomwe. Wa sayansi wololera amene wazindikira mochenjera izi angachite manyazi kunena kuti, "Ndachita," osati "Ndalenga," ponena za zochita zake zimene sangasankhe. Iye akanamva modzichepetsa kwa Allahu Taala. Munthu wochepekera mu kudziwa, kumvetsetsa ndi kudzichepetsa, sachita manyazi kunena chilichonse pa malo aliwonse. Allahu Taala ali ndi chifundo pa anthu onse pa dziko lapansi. Amalenga chilichonse chimene akuchifuna ndi kuchitumiza kwa aliyense. Iye amadziwitsa anthu momveka bwino zomwe ayenera kuchita kuti athe kukhala m'dzikoli mwa mtendere ndi mosangalala, ndi kupeza chisangalalo chosatha m'dziko ilo liri mkudza. Amamuongolera kunjira yoongoka amene wamfuna mwa iwo amene asiya njira yowona ndi kutsata njira ya ukafiri (Kusakhulupirira) ndi kupatuka chifukwa chonyengedwa ndi ma nafs (zilakolako) zawo, abwenzi oipa, mabuku oipa, ndi zofalitsidwa. Allahu Taala amawakokera ku njira yolondola. Sapereka madalitso awa kwa anthu ankhanza ndi opyola malire. Amawasiya kuti akhala m'dambo la ukafiri momwe analowa atalakalaka ndi kumukonda.

yemwe anaphunzira ku India analemba motere m'kalata yake ya 18 mu **Maktubat**[1] a chi Persia:

"Anthu ambiri amalakwa pogwiritsa ntchito zokaikitsa ndi zopeka. Ena mwa anthu oganiza molakwikawa amati: 'Allahu Taala safuna ibadah (ntchito za kupembeza) zathu. Ibadah zathu sizipindulira Iye. Ukulu wake siusintha kaya anthu timupembeza kapena sitikumumvera. Anthu omwe amapanga ibadah amangodzivuta chabe popanda phindu.' Kuganiza uka ndi kolakwika; anthu omwe sadziwa Chisilamu amanena izi poganiza kuti ibadah inalamulidwa chifukwa ndi yofunika kwa Allahu Taala. Uku ndi kaganiza kolakwika ndipo kumapangitsa wina kusokoneza zotheka ndi zosatheka. Ibadah iliyonse yopanga munthu imamupindulira yekha. Allahu Taala wanena momveka bwino mu ayah 18 mu Surah Fatir kuti izi zili motero. Munthu yemwe angaganize motero ali ngati munthu yemwe akudwala ndipo dokotala wamuuza kuti asamale pa zakudya zina zomwe amadya koma iyeyo sakusamala pa kadyedwe kake ndikumati:, 'Sazimuwononga dokotala nditapanda kusamala madyedwe anga.' Akunena zoona kuti dokotalayo sangavutike , koma iye mwini ndi amene akhale mavuto. Dokotala wamuuza za madyedwe abwino ndi cholinga choti moyo wa odwalayo usamalike osati kuti apindula dokotalayo. Ngati atatsatira malangizowo achira koma ngati satsatira. Ngati sasamala atha kumwalira ndipo dokotayo sapeza vuto lililonse.

"Anthu ena oganiza molakwika sachita ibadah ndipo sasiya kuchita zomwe zaletsedwa (Haram); Iwo samvera Chisilamu. Iwo amati, 'Allah ndi Wachifundo Chambiri (Karim) ndi Wachisoni (Rahim): amamvera chisoni anthu ndi kuwakhululukira mopanda malire ndipo Allah sazunza aliyense. Inde, akulondola m'chiganizo chawo choyambacho koma akulakwa m'chiganizo chomalizacho. Pa nkhaniyi, Satana amanyenga ndi kuwasocheretsa kukhala osamvera. Munthu woganiza bwino sanganyengedwe ndi Satana. Allahu Taala sikuti ndi Wachifundo Chambiri ndi Wachisoni chokha, komanso amalanga mowawitsa kwambiri. Timachitira umboni kuti Allahu Taala ampanga anthu ambiri kukhala mu umphawi ndi movutika pa dziko pano. Amapanga, mopanda

[1] Maktubat ndi makalata 100 omwe anasonkhanitsidwa ndipo analembedwa mu 1339/741 ndikusindikizidwa ku India mu 1911/1329. Ku Library ya Suleymaniyye ku Istanbul kuli bukhuli lolembedwa pa manja. Irshad assalikin ndi Madin al-maani ndi Sharaf ad-din Ahmad ibn Yahya Muniri's "rahimahallahu taala" ndi mabuku ena awiri ofunikanso. Yahya Muniri ankakhala ku Bihar, India, kumene kuli manda ake. Munir ndi mudzi ku Bihar. Mbiri yake idalembedwa mwatsatanetsatane mu Shah Abd al-Haqq ad- Zolemba za Dahlawi "rahimahallahu taala" Ntchito yina ya Persian Akhbar al-akhyar, lomwe linasindikizidwa ku Deoband, India, mu chaka cha 1914/1332 ndipo pa mbuyo pake idapangidwanso ku Lahore, Pakistan.

kukaika zolengedwa zambiri kukhala m‘mazunzo. Ngakhale Iye ali ndi Chifundo chambiri ndi Wosamalira (Razzaq), sangapereke ngakhale mtanda wa nsima pokhapokha anthu atagwira ntchito yaulimi. Ngakhale kuti amasunga aliyense ndi moyo, sangalole munthu kukhalabe ndi moyo popanda kudya kapena kumwa. Ngakhale kuchiza munthu wodwala popanda kumwa mankhwala. Adalenga njira zopezera madalitso onse a dziko lapansi monga kukhala ndi moyo, Kusadwala ndi kukhala ndi chuma, ndipo saonetsa chisoni powalanda iwo amene satsatira njira za madalitso a dziko lapansi. Pali mitundu iwiri ya mankhwala. Mankhwala akuthupi ndi a ku uzimu. Mankhwala ochiza kudwala kulikonse kwa ku uzimu ndi kupereka chopereka, ndi kupemphera. Hadith imati, “ **Chizani odwala omwe ali pakati panu polipira chopereka**!" ndipo" **kunena Astaghfar (Astagfurullah) kawiri kawiri ndi mankhwala a chilichonse.**" Pali mankhwala ambiri akuthupi. Amaphunziridwa kudzera mu kuyesa (ma experiment). Kugwiritsa ntchito mankhwala a ku uzimu kumathandizanso kupeza mankhwala a kuthupi. Chimodzimodzi ndi kupeza madalitso a dziko ilo liri mkudza. Allahu Taala Anapanga kusakhulupilira ndi umbuli kukhala mankhwala okupha mtima ndi moyo, ndipo ulesi umapangitsa moyo kudwala. Ngati mankhwala sagwiritsidwa ntchito, mzimu udzadwala ndi kufa. Mankhwala okhawo omwe angachidze kusakhulupirira ndi umbuli ndi marifa (kudziwa chachinsinsi cha Mulungu). Mankhwala a ulesi ndi kuswali ndi kuchita ibadah ya mtundu uliwonse. Pa dziko pano munthu atamwa poizoni ndikuti: 'Allah ndi Wachifundo ndipo amateteza kuwononga kwa poizoni,‘ atha kudwala ndi kumwalira. Munthu yemwe akutsekula mmimba atamwa mafuta a nsatsi [kapena munthu wodwala shuga akudya zinthu za shuga] matenda ake amakula. Izi zimachitika chifukwa thupi la munthu ndi lofewa, limafuna zinthu zosiyanasiyana zofunikira zambiri monga chakudya, zovala ndi pokhala. Ndi kovuta kupeza zinthu zofunikirazi ndi kuzikhonza kuti zigwiritsidwe ntchito moigwirizana ndi malamulo a chisilamu. Kuti ntchitozi ziwongoleledwe mosavuta, mphamvu yapadera yotchedwa **nafs** inalengedwa mwa munthu**.** Mphamvu iyi siinalengedwe mu nyama. Nafs imafuna zinthu zomwe zili zofunikira ku thupi. Imasangalala kuchita zinthuzi mopyola muyeso. Zokhumba za nafs zimatchedwa **shahwa** (chilakolako). Kugwiritsa ntchito shahwa mopyola muyezo koma mopanda kuganizira kumaononga mtima ndi thupi la munthu ndi anthu ena zomwe zimazetsa uchimo. (Chonde onani gawo lomaliza la mutu wa 13 wa bukhu loyamba la fascicle of **Endless Bliss.**

“Gulu lina la anthu oganiza molakwika amapanga riyada (kudzimana) pokhala ndi njala kuti achotse shahwa (chilakolako), ghadab (mkwiyo) ndi kusamalira zilakolako zawo zomwe zimakanidwa mu chisilamu. Amaganiza ngati kuti Chisilamu chimalamula kuti zilakolakozo zithetsedwe. Koma

akazunzika ndi njala kwa nthawi yaitali amaona kuti zelakolakozi sizichoke ndipo amayamba kunena kuti Chisilamu chalamula zinthu zosatheka. Iwo amati: 'Lamulo la Chisilamu ili silingakwaniritsidwe. Munthu sangathe kuchotsa zinthu zomwe zili mbali ya chilengedwe chake. Kuyesera kuchotsa nafs kuli ngati munthu kuyesa kusintha mtundu wa khungu lake. Kuyesera kupanga chinthu chosatheka ndi kutaya nthawi.' Amaganiza ndi kuchita zinthu molakwika. Ndipo zonena zao zoti Chisilamu chalamula izi ndi umbili ndi uchitsiru wachiziwikire poti Chisilamu sichimalamula kuchotsa kwa makhalidwe aumunthu monga mkwiyo ndi chilakolako. Kunena kotero ndi kuyankhula kwa mnyozo motsutsana ndi Chisilamu. Zikanakhala kuti Chisilamu chinalamula izi, Muhammad salallah alaihi wasallam, mkulu wa Chisilamu, sakanakhala ndi makhalidwe awiriwa (mkwiyo ndi chilakolako). Ndipo Iye anati: '**Ndine munthu. Ngati munthu wina aliyense nanenso ndimakwiya.'** Nthawi zina ankaoneka okwiya. Mkwiyo wake umakhala chifukwa Cha Allahu Taala Mu ayah 134 ya Sura Al Imran mu **Quran al-Karim,** Allahu Taala amayamikira anthu '**amene amatha kugonjetsa mkwiyo wawo.**' Sayamikira omwe sakwiya. Zonena za anthu oganiza molakwika ndikumata azichotsa zilakolako ndi zopanda umboni. Mfundo yoti Rasulullah "sallallahu alaihi wa sallam" anakwatira akazi asanu ndi anayi "radiyallahu taala anh"unna ndi chitsimikizo kuti zoyankhu za anthu awa ndi zalakwika. Zilakolako za munthu zikatha, ayenera kubwezeretsa pakumwa mankhwala. Chimodzi modzi mkwiyo; munthu amateteza mkazi ndi ana ake kamba kokhala ndi mkwiyo. Amamenya nkhondo (jihad) ndi adani a Chisilamu mothandizidwa ndi mkwiyo. Chifukwa Cha chilakolako munthu amakhala ndi ana zomwe zimamupatsitsa ulemu ndi kutchuka iye atamwalira. Izi ndi zomwe chisilamu chimakonda ndi kuyamikira.

"Chisilamu sichikulamula kuthetsa mkwiyo ndi chilakolako ayi, koma kutha kusamala pozigwiritsa ntchito ziwirizi, potsatira malamulo a Chisilamu. Ndi chimodzimodzi momwe zikufunikira kwa munthu wa pa hatchi kapena mlenje kuti asasiya hatchi kapena galu wake chifukwa cha kuvuta kwawo, koma kuti aphunzitse zifuyozi m'njira yoti athe kuzigwiritsa ntchito bwino. M'njira yina, chilakolako ndi mkwiyo zili ngati galu wa mlenje kapena hatchi kwa munthu wa hatch. Popanda ziwirizi madalitso a dziko lomwe lili nkudza sangasakidwe Koma pafunika kudziphunzitsa ndi kugwiritsa bwino ntchito mu njira ya Chisilamu. Ngati mmalo mophunzira kugwiritsa bwino ntchito, izo zikuchuluka ndi kupyola muyeso wa Chisilamu, ndi pamene zimamtengera munthu ku chiononge ko. Cholinga chodzimana sikuchotseratu zinthu ziwiri izi, koma kudziphunzitsa ndi kuzipanga kuti zigonjere ku malamulo a Chisilamu. Izi ndi zotheka kwa wina aliyense. Kugwiritsa ntchito mphamvu ya atomiki kapena kupeza kwa zinthu monga ndege za jet sikutanthauza chitukuko koma kuzigwiritsa bwino ntchito

potumikira anthu ndiye chitukuko. Ndipo zimenezi ndi zotheka potsatira Chisilamu.

"Gulu la chinayi la anthu oganiza molakwika amazinamiza ponena kuti, 'Chilichonse chinakhonzedweratu kale la muyaya. Mwana asanabadwe, zatsimikiziridwiratu ngati angadzakhale **sa'id** (wopembeza, woyenera kukalowa ku Mparadizo) kapena **shaqi** (wochimwa, woyipa, woyenera kukalowa ku Gahenal). izi sizimasintha. Choncho, ndi zopanda ntchito kumapembeza.' Ma Swahaba al-Kiram anayankhulanso motero pamene Rasulullah "sallallahu taala alaihi wa sallam" ananena kuti qada ndi qadar sizingasinthe ndipo zonse zinali zitakhonzedweratu kale la muyaya. 'Tiyeni tidalire zokhonzedweratu kale la muyaya ndikusiya kuchita zopembedza (ibadah).' Rasulullah anayankha: **'Muzipanga ibadah! Ndi zosavuta kuti aliyense achite zomwe analemberadwa kale la muyaya kuti azachita!** Kutanthauza kuti yemwe analembedwera kuti adzakhala wopembedza kale la muyayalo adzakhaladi wolungama. Chimodzimodzi kuchita ntchito zopembedza ndi anthu omwe analemberedwa kale kuti adzakala oyera, ndi kusamvera Allah kwa iwo amene analembedwera kale kutiadzakhala oyipa zimafanana mmakhalidwe mwa anthu omwe anakonzedweratu kukhala ndi moyo wathanzi, kudya chakudya ndi kumwa mankhwala ndi awo omwe anakonzedweratu kudzadwala ndi kumwalira osadya chakudya kapena osamwa mankhwala. Anthu omwe adalemberedwa kuti adzamwalira ndi njala kapena matenda sapindula ndi chakudya kapena mankhwala. Njira zopezera ndalama zimatsegulidwa kwa omwe adalemberedwa kuti adzakhala olemera. Njira zopitira ku madzulo zimatsekedwa ngati munthu analemberedwa kuti adzafera ku mmawa. Ngati momwe zimanenedwera kuti Mngelo wamkulu, Izrail alaihi-salam, tsiku lina atakamuona Mtumiki Sulaiman (Solomon) alaihi-salam, anayang'na kwambiri mmodzi mwa anthu omwe anakhala pomenepo. Munthuyo anachita mantha ndi momwe Mngeloyo anamuyang'anira. Izrail alaihi-salam atapita, iye anapempha Sulaiman alaihi-salam kuti alamule mphepo kuti imutengere ku dziko lina ku madzulo kuti athawe mngelo Izrail alaihi-salam. Izrail alaihi-salam atabwereranso Sulaiman alaihi-salam anamufunsa chifukwa chomwe anamuyang'anira kwambiri munthu uja. Izrail alaihi-salam anati, 'Ndatumidwa kudzatenga mzimu wake koma kuti ndikatengere ku mzinda wina waku madzulo pasanathe ola. Koma nditamuona ali ndi iwe, sindinachitire mwina koma kumuyang'ana modabwa. Kenako ndinapita ku dera la kumadzulolo ndipo ndinakamupeza kumeneko moti ndachotsa mzimu wake[1]. Mmene

[1] Nkhaniyi yafotokozedwa mwatsatanetsatane m'bukhu la **Mathnawi** lolembedwa ndi Jalal ad-din Rumi, yemwe anamwalira ku Konya m'chaka cha 1273/672.

zaonedwera apa, kukonzedweratu kwamuyaya sikunali lamulo koma kudziwa. Pofuna kuti kukonzedweratu kwamuyaya kuti zichitike, munthuyo anaopa Izrail alaihi-salam,ndipo Sulaiman alaihi-salam anapanga zomwe iye anafuna; ndipo zomwe zidakonzedwa kale zinathekadi podzera mu zinthu zochitika zosiyanasiyana. Choncho munthu amene anatsimikiza kukhala wopembedza m'kale lamuyaya, adzapeza iman kwambiri ndi kukhonza makhalidwe ake woipa pochita riyada. Sura al-Anam ayah 125 ikuti: **'Choncho, amene Allahu Taala akufuna kumuongola, amamtsekula chifuwa chake kuti Chisilamu chilowemo.'** Munthu yemwe anadziwika mu kale lamuyaya kuti adzakhala woipa, amene anakonzedweratu kukalowa ku Gahena, amapatsidwa maganizo oti, 'Palibe chifukwa chomapangira ibadah. Zinakonzedweratu kale kuti anthu ena ndi oipa ena ndi abwino.' Iye sapanga ibadah chifukwa cha maganizo otero. Kusapanga kwake kwa ibadah kamba ka maganizo amanewo kukuonetsa kuti analemberedwa kale kudzakhala woipa. Nayenso yemwe umbuli wake adalembedwa kale amapatsidwa maganizo amenewo oti, 'Chilichonse chinalembedwa kale. Kuwerenga kapena kuphunzira sikungapindulire munthu ngati analemberedwa kudzakhala mbuli.' Iye sawerenga kapena kuphunzira kalikonse. Amakhalabe mbuli. Ndipo ngati kwalembedwa kuti munthu adzalima ndi kukolola zochuluka, amapatsidwa mpamvu zolimira ndi mbewu zobvala. Chimodzimodzinso ndi awo omwe kunalembedwa kuti adzakhala anthu abwino, amakhulupirira ndi kuchita zopembedza ndipo omwe kunalembedwa kuti adzakhala oipa amakanira ndi kusamvera. Mbuli zina zomwe sizitha kumvetsa izi, zimati, 'Kodi chikhulupiriro ndi miyambo zimagwirizana bwanji ndi kukhala wopembedza kwa muyaya, kapena kusakhulupirira ndi kusamvera ndi kukhala oipa?' Ndi kuganiza kwao koperewera, amayesa kumvetsetsa ubalewu ndi kupeza mayankho a zonse ndi nzeru zawo. Koma kuganiza kwa munthu kuli ndi malire, ndipo ndi kupusa kapena uchitsiru kuyesera kumvetsetsa zinthu zomwe ziri zapyola maganizo a munthu. Ndi kusaganiza kwao bwino, amayesera kumvetsetsa izi ndi maganizo awo. Anthu omwe amaganiza choncho ayenera kutengedwa ngati zitsiru. Isa alaihi-salam adati: 'zinali zosavuta kwa ine kuwapanga akhungu kuona, ngakhale kudzutsa anthu akufa. Koma sindinathe kufotokoza chowonadi ngakhale kwa chitsiru chimodzi.' Allahu Taala, Wodziwa kwamuyaya ndi Wanzero (hikma) zobisika amakweza zolengedwa zina zaumunthu kukhala paudindo wa angelo, ndipo ngakhale ku giredi la pamwamba kwambiri. Zina amazitsitsa mpaka pa mlingo wa galu kapena nkhumba.

Hazrat Sharaf ad-din Ahmad ibn Yahya Muniri walemba mu kalata yake ya76: " **'Saada'** ndi chiyero chobweretsa chimwemwe cha muyaya, khalidwe loyenera kukalowa ku mparadizo,' ndipo '**shaqawa**' ndi 'kuchimwa, koyenera

kukalowa ku Gahena.' Saada ndi shaqawa zili ngati chuma chiwiri kwa Allahu. Kiyi wokapezera chuma choyambacho ndi kuchita ntchito zabwino (taat, ibadah). Kiyi wa chuma chachiwiricho ndi kuchimwa. Allahu Taala anadziwa kale ngati munthu adzakhale sa'id (wa saada, woyera) kapena shaqi (wa shaqawa, woyipa). Kudziwa kwa Allahu uku kumatchedwa **'qadar'** (chikonzero). Munthu yemwe chikonzero chake chiri chokhala woyera, amamvera Allahu Taala. Yemwe chikonzero chake chiri chokhala woipa nthawi zonse amangochita machimo. Pa dziko pano aliyense atha kudziwa ngati ali oyera kapena oipa poona ntchito zake. Mnjira iyi ophunzira akulu akulu achipembezo omwe amakhala akulingalira za dziko lomwe lili nkudza, amatha kudziwa ngati munthu ali woyera kapena woipa. Koma munthu yemwe ali ndi udindo wa chipembezo koma amakomedwa ndi za mdziko lino sangadziwe izi. Ulemerero ndi madalitso aliwonse zimabwera kuchokera mukumvera ndi kupembedza Allahu Taala ndi **ikhlas** (moona mtima, mchitidwe wopanga zinthu chifukwa cha Allahu Taala yekha). Choipa chirichonse kapena mavuto zimayamba kuchokera pa kuchimwa. Mavuto ndi tsoka zimabwera kwa aliyense kudzera mu kuchimwa. Mtendere ndi kumasuka kumabwera kamba ka kumvera[1]. Panali munthu yemwe anakhala moyo wake kupemphera ndi chita ibadah pa mzikiti wa Aqsa ku Jerusalem. Koma chifukwa sanaphunzira zoyenera pa kupemphera ndi ikhlas, ankanyalanyaza kupanga sajda imodzi (kuika chipumi pansi poswali); iyeyu analuza zambiri mpaka adaonongedwa kotheratu. Koma chifukwa cha kuti galu wa As'hab al-kahf anayenda ma sitepe angapo kumbuyo kwa ma siddiq (abwino, achilungamo), ngakhale anali waumve, anakwezedwa kwambiri moti sananyozedwenso. Nkhaniyi ndi yodabwitsa kwa munthu; akatswiri ophunzira sanathe kupeza yankho pa nkhaniyi kwa zaka mazana. Nzeru za munthu sizingamvetse nzeru ya Umulungu zobisika mu nkhaniyi. Allahu Taala anamuuza Adam alaihi-salam kuti asadye tirigu koma anamulola kudya chifukwa ankadziwa kale lamuyaya kuti iye adzadya. Allahu Taala analamula Satana kuti awerame posonyeza ulemu kwa Adam alaihi-salam koma sanamulole kuti aweramire Adam. Allahu Taala anati tidzimufuna Iye, koma sanalole kuti anthu opanda ikhlas amupeze. [Pa nkhani izi] anthu oyenda m'njira yopatulika sakanatha kunenepo kalikonse kupatula kuti samkamvetsetsa. Ndiye ife tingayankhulepo kanthu? Allahu Taala safuna chikhulupiriro kapena kupemphera kwa anthu ndipo kusakhulupirira kapena

[1] Ichi ndi chizindikiro cha kupatulika kwa Allahu Taala Palibe angasinthe izi. Tisamaganizire chinthu chowoneka chophweka ndi chokoma ku nafs zathu ngati saada (umulungu wobweretsa chisangalalo cha muyaya). Komanso tisaganize kuti zinthu zooneka zovuta ndi zowawa ku ma nafs anthu ngati shaqawa (uchimo, mchitidwe woyenerera Gahena) kapena chiwonongeko.

kuchimwa kwa anthu sikumamupatsa vuto lililonse**.** Allahu Taala safuna zolengedwa. Wapanga maphunziro kukhala njira yothanira ndi kusakhulupirira ndipo analenga umbuli ngati njira yochimwira. Kukhulupirira ndi kupemphera kumachokera mu kudziwa zinthu, pomwe kusakhulupirira ndi tchimo zimachokera ku umbuli. Ntchito zabwino (taat) zisasiyidwe ngakhale ziri zochepa chotani! Kuchimwa kuyenera kupewedwa ngakhale tchimolo liri lochepa. Akatswiri ophunzira a Chisilamu anati zinthu zitatu zingayambitse zinthu zina zitatu: ntchito yabwino imapangitsa Rida (chilolezo) cha Allahu Taala; kuchimwa kumayambitsa mkwiyo wake(Ghadab); iman imapangitsa munthu kulandira ulemu ndi ulemerero. Pa chifukwa ichi, tipewe kuchimwa tchimo lomwe limatengedwa kuti silingakuchotsere chisomo cha umulungu m'moyo wako. Mkwiyo wa Allahu Taala utha kukhala mu tchimo limenelo. Tiyenera kumutenga wokhulupirira aliyense wa Ahl as Sunna Islam ngati wopambana kuposa ife. Akhonza kukhala yemwe Allahu Taala amamkonda kwambiri. Tsogolo la aliyense lomwe linalembedweratu kale, silingasinthidwe.

Allahu Taala, ngati angadzafune, adzakhululukira Msilamu yemwe amangochimwa ndipo sachita ntchito iriyonse yabwino. Monga zalembedwera mu ayah ya 30 mu Sura al-Bakara, pamene angelo anafunsa, **'Oh Allah! Kodi muika m'menemo amene adzidzawonongamo ndi kukhetsa mwazi**?' Allahu Taala sananene kuti zizabweretsa chisokonezo koma anati**:** '**Ndithudi, Ine ndikudziwa Zimene simukudziwa.'** Ankatanthauza kuti: 'Ndimapanga chopanda phindu kukhala chaphindu. Ndimapanga yemwe ali kutali kubwera pafupi. Ndimapanga onyozedwa kukhala wolemekezedwa. Mumawaweruza potengera ntchito zawo, koma Ine ndiyang'ana chikhulupiriro m'mitima yawo. Inu mukutenga kupanda tchimo kwanu, iwo adzadalira chifundo changa. Monga Ndikamakonda kusalakwa kwanu, Ndimakonda kukhululuka machimo a Asilamu. Simungadziwe zomwe Ndikudziwa. Ndimapanga anthu okhulupirira kupeza madalitso anga a muyaya ndi kuwakondweretsa onse ndi chisomo change chosatha.' "

Al-Imam ar-Rabbani "rahmatullahi alaih" analemba m'makalata osiyanasiya:

"Zinthu zomwe zalamulidwa ndi Allahu Talaa zimatchedwa **fardh**, ndipo zomwe zoletsedwa ndi **haram**. Zochita, zoyankhula, makhalidwe zomwe siziri fard kapena haram ndipo zanenedwa kuti ndi zololedwa zimatchedwa **mubah. Ibadah** (kulambira) ndi kuchita zinthu za fard, kupewa za haram, ndi kuchita mubah kuti upeze chilolezo cha Allahu Taala. Kuti ibadah ikhale sahih (yolondola, yangwiro) ndi maqbul (yolandiridwa, yokondedwa ndi Allahu Taala), ndi zofunika (a) kuphunzira **ilm,** (b) kuchita ntchito **amal** mogwirizana ndi zofunikira (msichi), ndi (c) kuchita izi ndi **ikhlas.**

"Msilamu yemwe amakhulupirira fardh ndi haram, koma sapanga ibada chifukwa cha ulesi kapena chifukwa cha amzake, akamwalira osalapa machimo ake, adzakalangidwa ku Gahena mpaka chilango cha machimo ake chitatha.

Munthu yemwe sakuphunzira kuti fardh ndi chan; munthu yemwe akuzidziwa faradh koma samadzilabadira ndipo sazichita mosadzimvera chisoni kapena kuopa Allahu Taala, anthu awa adzatuluka chisilamu ndi kukhala osakhulupirira. Azaponyedwa ku moto wa Gahena kwamuyaya. Izi chimodzimodzi ndi ochita haram.

"Ngati munthu saphunzira kapena kudziwa zofunika pochita ibada, kachitidwe kawo ka ibadayo sikakhala ka sahih ngakhale atapanga ibadah yo ndi ikhlas. Iwowa akaotchedwa ku moto wa Gahena ngati sanapange ibadahyo. Ibadah yopangidwa ndi munthu wodziwa ndi kuchita motsatira zofunika zonse sazazunzidwa ndi madzunzo a ku Gahena. Koma ngati akuchita ndi ikhlas, mwambo akupangawo ndi zabwino zawo zilizonse sizili maqbul (kolandiridwa). Sangapeze nazo thawab iliyonse. Allahu amasonyeza kusakodwa ndi ibadat kapena ntchito za chifundo zotero. Ibadah yopangidwa yopanda ilm ndi ikhlas ndi yopanda phindu. Siyingateteze ku kusakhulupirira, machimo ndi chilango. Anthu achinyengo ambiri amene ankachita ibada motero moyo wawo wonse achitiridwa umboni akufa ngati osakhulupirira. Ibadat yopangidwa ndi ilm ndi ikhlas imateteza munthu ku kusakhulupirira ndi ku uchimo ndipo izi zimapanga munthuyo kukhala aziz (wolemekezeka kwambiri) padziko. Kukamba za moyo wawo ku dziko ilo lili nkudza, Allahu Taala walonjeza anthuwa mu ayah al-Karima ya 9 ya Sura al-Maida komanso mu Sura al-Asr kuti iwowa adzapulumitsidwa ku mazunzo aku moto wa Gahena. Allahu Taala ngoona pa malonjezo Ake. Iye amasunga chipangano"]

**-6-**

## ALLAHU TAALA ALIKO NDIPO NDI MMODZI

ZOLENGEDWA ZONSE KUNALIBE
NDIPO ZONSE ZIDZATHA

Timazindikira zinthu zomwe zatizungulira kudzera mu zidziwitso za ziwalo zathu . Zinthu zomwe zimakhudza zidziwitso za ziwalozi zimatchedwa **nthu** (zolengedwa, kukhalapo). Zotsatira za anthu pa zidziwitso zisanu zathu zimatchedwa makhalidwe omwe amagwiritsidwa ntchito pozisiyanitsa chimodzi ku chinzake. Kuwala, mau, madzi, mpweya ndi galasi zonse ndi -nthu (zinthu); zonse zilipo. Zinthu zomwe zili ndi Sayansi, kulemera ndi kuchuluka,

tingoti zomwe zimatenga malo zimatchedwa **sabusitansi** kapena **mata**[1]. Ma **sabusitansi** amasiyana potengera makhalidwe ndi zizindikiro zawo. Mphweya, madzi, mwala ndi galasi zonse ndi ma sabusitansi. Kuwala ndi mau si ma sabusitansi chifukwa satenga malo omwe zili komanso zilibe kulemera. Nthu chiliyonse ili ndi mphamvu, kunena kuti zitha kugwira ntchito. Sabusitansi iliyonse ikhonza kukhala mmakhalidwe atatu: yolimba, yamadzimadzi komanso yampweya. Ma Sabusitansi olimba amakhala ndi shepi (mwachitsanzo kuzungulira ngati bokosi) Ma Sabusitansi amadzimadzi ndi a mpweya amatsatira shepi ya (kontena) yomwe zaikidwamo, ndipo zilibe shepi yeni yeni. Sabusitansi yomakhala ndi shepi imatchedwa obujekiti. Ma Sabusitansi ambiri ndi ma obujekiti. Mwachitsanzo, kiyi, pini, mbale, fosholo ndi m'somali ndi ma objeketi osiyana okhala ndi ma shepi osiyana. Koma zomwe zitha kukhala kuti zinapangidwa ndi mata imodzi yomwe ndi nyuroni. Pali mitundu iwiri ya sabusitansi ma Elementi ndi ma kompaundi.

Kusintha kumachitika mu obujekiti iliyonse. Mwachitsanzo, itha kusuntha malo omwe ili; kukula kapena kuchepa. Mtundu wake utha kusintha. Itha kudwala kapena kufa ngati ili ya moyo. Kusintha uku kumatchedwa **Events** (zochitika). Mata siyingasinthe pokhapokha pali mphamvu yochokera kunja kwake. Event (chochitika) yomwe siyisintha mchenicheni cha mata chimatchedwa **physical event** (chochitika chooneka). Kung'amba pepala si chochitika chooneka. Mphamvu Ina iyenera kukhudza sabusitansi kuti kuchitika kooneka (physical event) kuchitike pa sabusitansi. Chochitika chomwe chimasintha kapangidwe kapena zenizeni za sabusitansi chimatchedwa **chemical events** (zochitika za kemiko). Pamene pepala likuyaka ndi kusanduka phulusa, kuchitika kwa kemiko kwachitika. Sabusitansi iyenera kukhudzidwa ndi sabusitansi kuti chochitika cha kemiko chitheke mu sabusitansiyo. Ngati ma sabusitansi awiri kapena angapo alumikizana ndipo chochitika cha kemiko kwachitika mu sabusitansi ilichonse, pamakhala **chemical reaction** (kusintha kwa kemiko).

**Chemical reaction** (kusintha kwa kemiko) pakati pa ma sabusitansi, akakuzana, kumachitika mkati mwa tinthu tating'ono kwambiri totchedwa **atoms.** Obujekiti iliyonse imapangidwa ndi ma atomu.

Ngakhale kuti kapangidwe ka ma atomu ndi kofanana, kukula ndi kulemera kwao ndi kosiyana. Pano tikudziwa mitundu 118 ya ma atomu. Ngakhale atomu yaikulu pa onse siingaoneke pa makina a mayikolosikopu ya mphamvu. Ma atomu ofanana akabwera pamodzi, amapanga **elementi**. poti pali mitundu ya

[1] Chilichonse chomwe chimatenga malo komanso cholemera ndi **sabusitansi** koma chinthu chomwe chili ndi mawonekedwe ake ndi mankhwala ndi **mata**.

ma atomu 118 palinso ma Elementi 118. Zitsanzo za ma Elementi ndi monga, Iron, sulfur, mercury, oxygen ndi carbon. Ma atomu osiyana akabwera pamodzi amapanga **Kompaundi**. Ma kompaundi alipo a mitundu yambirimbiri. Madzi, mowa, mchere ndi laimu ndi zitsanzo za ma kompaundi. Ma kompaundi amapangidwa pokumanitsa ma elementi kapena ma atom awiri kapena angapo.

Zinthu zonse, ngati mapiri, nyanja, zomera za mitindu yonse ndi nyama zimapangidwa ndi ma Elementi 118. Miyala yomangira ma sabusitansi a moyo ndi opanda moyo onse ndi ma Elementi 118 awa. ali ngati miyala yomangira zinthu zonse zamoyo komanso zopanda moyo. Ma sabusatansi onse amapangidwa pophatikiza ma atomu a imodzi kapena angapo a ma Elementi 118 amenewa. Mpweya, dothi, madzi, kutentha, Kuwala, magetsi ndi ma gelemu zimalekanitsa ma kompaundi kapena kuyambitsa ma sabusitansi kuphatikizana ina ndi inzake. Kusintha sikuchitika popanda choyambitsa. gwiranapangitsa ma sabusitansi kugawikana kapena kubwera pamodzi. Mukusintha kumeneku, ma atomu, magawo a elementi, amayenda kuchoka sabusitansi ina kupita ku ina. Nthawi zina amangochoka mu subsitanti ndi kuyima paokha. Timaona ma obujekiti akuzimirira, chifukwa timawaonara kunja kwawo. Timalakwitsa, pakuti “kuzimira” kapena “kuoneka” sikanthu koma kusintha kuchokera ku sabusitansi ya mtundu wina kupita ku mtundu wina. Kuzimira kwa obujekiti, ngati mtembo m'manda ndi kusintha kupita ku sabusitance ina ngati madzi ndi mpweya ndi dothi. Ngati ma sabusitansi atsopano omwe apangika podzera mu kusintha sasintha ziwalo zomvera, sitingazindikire kuti zakhalapo. Pa chifukwa ichi timati obujekiti yoyambayo inazimira, pomwe inangosintha kutenga mtundu wina. Tikuwonanso kuti chikhalidwe chilichonse chama elementi 118 wa chimasintha ndipo zochitika za kuthupi ndi ku mankhwala zimachitika mu element iliyonse. Pamene element yaphatikizana ndi ina (kapena ndi ena) mu kompaundi, ma atomu ake amataya kapena kupeza electron ndipo zikatero zakuthupi ndi mankhwala osiyanasiyana a element amasintha. Atomu ya element iliyonse imakhala ndi nyukiliasi ndi mitundu yosiyanasiyana ya tinthu tating'onoting'ono totchedwa ma **elekitironi.** Nyukiliasi imakhala pakatikati pa atomu. Nyukiliasi ya atomu ya ma elementi onse kupatula hayidurojini ndi opangidwa ndi tinthu totchedwa **protoni** ndipo amakala ndi nyesi ya imuna. Amakhalanso ndi ma **Nyuturoni** omwe sakhala ndi nyesi. Elekiteroni ndi kanthu kakang’ono komwe kamatenga nyesi yachikazi ndipo inazungulira nukiliasi. Ma elekitironi amazungulira m'mayendedwe awo mphindi iliyonse ndi kusintha moyenda mwawomo.

Ndi zotsimikizirika kuti m‘ma elementi a **radioactive** muli kusintha kotchedwa ma fission ndi ma fusion, omwe amachitika mu nyukiliya ya m‘ma

atomu. Komanso m'ma nyukiliya fission elementi imodzi imasintha nkukhala ina ndipo kuchuluka kwina kwa mata kumatha ndi kusanduka mphamvu. Kusintha kumeneku kuli ndi njira yowerengetsera yomwe anayipeza wa Sayansi wachiyuda, Einstein (anamwalira mchaka cha 1955/1375). Ngati ma kompaundi, nawo ma elementi amasintha ndi kukhala ena. Sabusitansi iliyonse, ya moyo kapena yopanda moyo, imasintha. Yakale imasowa nkubwera yatsopano. Chamoyo chilichonse, chomera kapena nyama chomwe chilipo lero kunalibe kale, ndipo kunalinso zamoyo zina. Ndipo m'tsogolo muno, zomwe zili ndi moyo panozi sizidzakhalako ndipo za moyo zina zidzabwera kudzakhala. Chimodzimodzi zinthu zopanda moyo. Zonse za moyo ndi zopanda moyo zimasintha, za kale zimazimira ndipo zina zatsopano zimabwera. Poti ma sabusitansi ena akabwera mmalo mwa ena omwe analipo ndi ofanana, munthu chifukwa chosazindikira kusintha uku, iye amangoganiza kuti sabusitansi ndi yomweyobe. Chitsanzo ndi cha mu kanema, momwe chithunzi china chimabwera pa kanthawi kochepa mmalo mwa china ndipo munthu amaona ngati ndi choyambacho. Pomwe pepala lapysa ndi kusanduka phulusa, timati pepala lazimira ndipo phulusa lapezeka chifukwa kusintha uku timakuona. Madzi ouma (ayisi) asukunuka, timati choumacho chasowa ndipo madzi apezeka.

Kumayambiriro kwa bukhu la **Sharh al-Aqaid** zalembedwa motere: "Chifukwa chokuti zolengedwa zonse zikusonyeza kukhalapo kwa Allahu Taala zolengedwa zonse zimaztchedwa '**alam**' (chilichonse kupatula Allahu Taala). Gulu lililonse la zolengedwa za mtundu womwewo zimatchedwans alam. Mwachitsanzo alam (dziko) la anthu, alam ya angelo, alam ya nyama, alam ya zopanda moyo. Chinthu chilichonse chimatchedwa alam."

Zalembedwa pa tsamba 441 mu buku la **Sharh al-Mawaqif** lolembedwa ndi Sayyid Sharif Ali Jurjani (yemwe anamwalira ku Shiraz, mchaka cha 1413/816): "Alam, omwe ndi anthu onse, ndi zolengedwa (**hâdith)**[1]. Kutanthauza kuti kunalibe, iwo anakhalapo pambuyo pake. [Tinalongosolanso pamwapapo kuti zolengedwa nthawi zonse zimabwera kuchokera ku zina] Mata ndi zizindikiro za obujekiti zalengedwa pambuyo.

Pa nkhaniyi, pali zikhulupiriro zinayi zosiyana:

[1] Chizindikiro ichi ^ pa mwamba pa ma vawelo chimapangitsa katchulidwe ka mau kukhala kokoka. Mawu oti hâdith ndi chizindikiro ichi pamwamba pa vawelo "a"amatanthauza "kulengedwa pambuyo pake, komwe kuli kupezeka mochedwa" mosiyana ndi 'Hadîth' yokhala ndi chizindikirochi pamwamba pa vawelo 'i' amatanthauza 'mawu' a Mtumiki Muhammad alaihis salam.

Malingana ndi Asilamu, Ayuda, Akhirisitu ndi anthu opembedza moto, mata ndi zizindikiro za sabusitance zidalengedwa pa mbuyo.

Malingana ndi Aristotle ndi ma filosofa omutsatira, zonse mata ndi zizindikiro za sabusitance zinalipo kuyambira muyaya. Iwo amati sizinapezeka kuchokera popanda kanthu koma kuti zinalipo nthawi zonse. Sayansi ya khemisitire imatsusa izi. Munthu yemwe angakhulupirire kapena kunena choncho amakhala kuti watuluka Chisilamu ndipo ndi wosakhulupirira. Nayenso Avicenna (Ibn Sina Husain) yemwe anamwalira mu 1037/428 ndi Muhammad Farabi yemwe anamwalira ku Damascus mchaka cha 950/339) anati ma sabusitansi analipo kuyambira muyaya.

Malinga ndi Mafilosofa omwe analiko Aristotle asanabwere anati mata ndi yamuyaya koma zizindikiro za sabusitansi zinalengedwa pambuyo. Makono a Sayansi ambiri amakhulupirira zolakwika izi.

Palibe mwa iwo anati mata inalengedwa pambuyo ndipo kuti zizindikira ndi za muyaya. Filosofa wa Chigiriki, Galen (Galenus), sanathe kusankha yankho la nkhaniyi pa mayankho anayiwa."

Asilamu amaperekera umboni m'njira zingapo zoti zonse zinalengedwa pambuyo pa nthawi. Njira yoyamba ndi yoti mata ndi zopezeka mkati mwake zimakhala zikusintha nthawi zonse. Chinthu chomwe chimasintha sichingakhale cha muyaya. Chiyenera kulengedwa pa nthawi ina, popeza ndondomeko yoti sabusitance iliyonse ikhalepo kuchokera mu ina yoyamba siyingakhale yamuyaya. Kusintha kochokera ku chinthu china sikungapyole kale la muyaya. Kusintha kumeneku kuyenera kukhala ndi poyambira, kutanthauza kuti sabusitance yoyambirira inachita kulengedwa kuchokera popanda kanthu. Panakakhala kuti panalibe chinthu choyambirira chopangidwa popanda kanthu, kune kuti, ngati ndondomeko ya kutsatizana yomwe chinthu chimachokera ku chinthu china chapambuyo pake zikanakhala zikubwerera mpaka m'buyo mwa kale losatha, bwenzi palibe chiyambi cha zinthu zomwe zimachokera ku zimzake, ndipo palibe chinthu chomwe chikanakhalapo lero. Kupezeka kwa zinthu panopa ndi chiyambi chawo chochokera ku zinthu zina kumasonyeza mfundo yoti zachuluka kuchokera ku zinthu zoyamba zomwe zinalengedwa kuchokera popanda kanthu.

Kuonjezera apo, mwala womwe wagwa kuchokera kumwamba sunganenedwe kuti wachokera ku malo opanda malire kapena ku nthawi yamuyaya; popeza mau amenewa amaimira 'kupanda poyambira kapena malire.' Kuchokera kopanda malire ndiye kutanthauza kuti kuchokera popanda kanthu, ndipo chomwe chanenedwa kuti chachokera kopanda malire sichikanayenera kufika. Kungakhale kusaganiza bwino, zosamveka mu Sayansi

ndipo za umbuli kunena kuti, “chachokera kopanda malire.” Chimodzimodzinso kuchulukana kwa anthu atachokera kwa munthu mmodzi sizingakhale kuti zinachokera kopanda malire. Anayamba kuchulukana kuchokera kwa munthu woyamba yemwe adalengedwa kuchokera popanda kanthu. Ngati zinganenedwe kuti kudalibe munthu woyamba yemwe analengedwa kuchokera popanda kanthu, palibe munthu amene akanakhalapo. Izi ndi zofanana ndi zolengedwa zonse. Zikanakhala zopanda nzeru, zosagwirizana ndi sayansi ndi umbuli kunena kuti, “poti zinabwera choncho zidzapita. Panalibe ma sabusitance oyambirira omwe analengedwa popanda kanthu,” pokamba za zinthu zopezeka kuchokera mu zinthu zina. Kusintha sikuwonetsa umuyaya, ngakhale zikuoneka kuti kunalengedwa popanda kanthu; sizikuonetsa kukhala **Wajib al-wujud** koma kukhala **mumkin al-wujud** (chomwe chalengedwa popanda kanthu ndipo chikhonza kukhala chosapezeka pomwe chiripoidzakhala osapezeka).

**Funso**: “Mlengi ndi zizindikiro za kulenga kwake kwa zolengedwa ndi kwamuyaya, kodi zolengedwazi sizingakhalenso zamuyaya?

**Yankho**: Nthawi zonse timachitira umboni kuti Mlengi yemwe ndi wamuyaya, amasintha sabusitansi ndi tizinthu kudzera m’njira zosiyanasiyana. Amawawononga ndi kulenga ena m'malo mwake. Mlengi wa muyaya, akafuna, amalenga chinthu kuchokera mu china. Monga kulenga magulu a zolengedwa (alam) sabusitansi iliyonse ndi chilichonse kudzera mu njira ina. Allahu Taala atha kulenga izi posagwiritsa china chilichonse atafuna kutero.

Yemwe akukhulupirira kuti anthu anachita kulengedwa amakhulupiriranso kuti adzazimirira tsiku lina. Ndi zachidziwikire kuti anthu olengedwa pomwe panalibe akhonza kusakhalanso. Tiona tsopano kuti zinthu zambiri zikusowa.

Msilamu ayenera kukhulupirira mfundo yoti ma sabusitansi ndi ma obujekiti ndi anthu onse zinalengedwa kuchokera popanda kanthu, ndipo kuti zidzapezekanso kuti kulibe. Timaona ma obujekiti akukhalapo pomwe panalibe kenako ndikuzimira. Ma obujekiti akazimira ma sabusitansi awo amakhalira, koma momga tafotokozera pamwambapo ma sabusitansi amenewa si amuyaya koma analengedwa kale la muyaya ndi Allahu Taala, yemwe adzaononge zinthuzi pa tsiku la Chiweruzo.

Zoziwika mu Sayansi masiku ano sizimatilepheretsa ife kukhulupirira mfundo imeneyi. Kusakhulupirira izi kusonyeza kusakhulupirira Sayansi ndipo zikutanthauza kudana ndi Chisilamu. Chisilamu sichikana nzeru za Sayansi. Chimakana kusiyiratu kuphunzira chidziwitso chachipembedzo ndi ntchito yopembeza. Nzeru za Sayansi sizikana Chisilamu. M'malo mwake, zimatsimikizira.

Chifukwa choti dziko linabwera pambuyo, pakuyenera kukhala Mlengi yemwe analilenga kuchokera popanda kanthu. Tanena kale kuti palibe chomwe chimachitika pachokha. Masiku ano, mankhwala a nkhaninkhani, katundu wam'nyumba, katundu wa m'ma kampani ndi wamalonda zida zamagetsi ndi zida za nkhondo zikupangidwa m'mafakitole. Zambiri mwa izo zimapangidwa kudzera mu masamu ovuta komanso kuyesera kambirimbiri. Kodi anthu anganena kuti pali ngakhale chimodzi mwa izo chomwe chinakhalapo chokha? Ayi, amanena kuti zinapangidwa ndi wina akudziwa chomwe akupanga ndipo zonse zimayenera kukhala ndi wozipanga. Koma amanena kuti mamiliyoni a zinthu ndi zochitika zooneka, za moyo ndi zopanda moyo ndi zomwe zikutulukiridwa mwatsopano komanso zomwe zakhala zikutulukiridwa mzaka mazana zapitazi zinangopezeka mwangozi.

Ndi chinyengo chanji ichi ngati sichovuta kapena kupusa ndi kusowa nzeru? Ndi zachiziwikire kuti pali Mlengi mmodzi yekha yemwe amapangitsa chilichonse kupezeka komanso kuyenda. Mlengi ameneyu ndi **Wajib al-wujud**, kutanthauza kuti alibe chiyambi, sanachokere ku chilichonse. Mlengi ayeneradi kukhalapo nthawi zonse, ndipo safuna kalikonse kuti akhalepo. Akanakhala kuti panalibe anachita kupezeka ndiye kuti akanakhala **mumkin al-wujud** kapena hadith, cholengedwa monga zolengedwa za m'dziko. Akanalengedwa kuchokera popanda kanthu kapena kudzera mu kusintha kuchokera ku cholengedwa china, chomweso chikanalengedwa ndi mlengi wina. Izi zikanapangitsa kuti pakhale olenga osawerengeka. Wina pambuyo pa wina. Ngati titaganiza ngati momwe tafotokozera pa mwambapa, zoti kusintha kwa zolengedwa sikungakhale kwa muyaya, zizakhala zomveka kuti sipangakhale olenga osawerengeka ndipo kuti chilengedwe chinayambika ndi Mlengi woyamba. Chifukwa ngati alengi akulenga wina, winayo ndi kulenga wina, ndipo titabwerera m'buyo kale la muyaya, kukanapezeka kuti kunalibe mlengi woyamba kulenga ndiye kuti sikukanakhala Mlengi. Choncho mlengi woyambayo yemwe sanalengedwe ndi Mlengi Wapadera wa zolengedwa zonse. Palibe mlengi Iye asanabwere ndi pambuyo pa Iye. Mlengi woti sanalengedwe amakhalapo nthawi zonse. Ngati Mlengi atangosiya kukhalapo kwa kanthawi, Zolengedwa zonse zitha kuzimira. Wajib al-wujud safuna chilichonse pa chifukwa chiliyonse. Yemwe analenga dziko lapansi, mlengalenga, ma atomu ndi zamoyo mwadongosolo lokhazikika komanso losavuta zonse akuyenera kukhala Wamphamvu zonse,wodziwa zonse, wakutha kulenga chomwe wafuna, akuyenera kukhala wapaderadera komanso wopanda kusintha mwa Iye. Adakakhala kuti Mlengiyo sanali wamphamvu zonse ndipo ndi wosadziwa zonse, sakadatha kulenga chilichonse. Pakadakhala alengi angapo zolenga zawo zikadatha kukhala zosemphana aliyense atafuna

kulenga momwe wafunira. Yemwe walenga dziko lapansi, mlengalenga, atoms ndi zamoyo mwadongosolo lokhazikika komanso losavuta, ayenera kukhala wamphamvu zonse, wodziwa zonse, wokhoza kulenga nthawi imodzi chirichonse chimene Iye wafuna, ndipo zikalengedwa ziyenera kukhala zapadera, koma pasakhale chosintha chilichonse pa Iye. Ngati Mlengi alibe mphamvu zonse ndipo mphamvu Zake siziri zopanda malire, ndipo akanakhala wosadziwa zonse, Iye sakanatha kulenga zolengedwa mwa dongosolo komanso mosavuta. Pakanakhala alengi ambiri ndipo zofuna kulenga zao zinali zosiyana, omwe zifuna zawo zikanasiyidwa osachitika sakanakhala alengi ndipo zinthu zolengedwazo zikanakhala zopanda dongosolo.

Mwa Mlengi palibe chomwe chimasintha. Mmene analili asanalenge dzikoli ndi mmene alili pano. Monga analengera chilichonse kuchokera popanda kanthu, nthawi zonse ndipo adakalenga chilichonse; Mwina mwake, kusintha kulikonse kukanasonyeza kukhala cholengedwa ndi kulengedwa kuchokera popanda kanthu. Tafotokoza kale mmwambamo kuti Wakhalapo nthawi zonse ndipo sazazimira Choncho palibe kusintha komwe kumachitika mwa Iye. Ngati momwe zolengedwa zinamufunira pozilenga, choncho zimafuna Allahu nthawi zonse. Iye yekha ndiye amalenga chilichonse, kusintha zinthu. Kuti zonse zikhale zogwirizana komanso kuti anthu athe kukhala ndi moyo ndi kukhala wotukuka, Iye analenga chirichonse kudzera m'njira. Akamalenga zoyambitsa, amalenganso zothandizira ndi kuthekera kwao pa kuchita. Ntchito ya munthu ndi kukhala chodutsira pakuyambitsa zokhudza zinthu.

Zitsanzo za kuchita pogwiritsa ntchito zomwe zimayambitsanjira zolenga za Allahu Taala za tsopano ndi monga kudya ukamva njala, kumwa mankhwala ukadwala, kukhecha machesi poyatsa kandulo, kuika acid pa zinc kupanga hydrogen, kusakaniza ndi kutenthetsa laimu ndi dongo popanga simenti, kudyetsa ng'ombe kuti mkaka upezeke, kumanga makina opukusa madzi kuti mupange magesi ndi kumanga ma fakitole amtundu uliwonse. Zolinga ndi mphamvu za munthu nazo ndi njira zolengera za Allahu Taala Anthu ndi njira yolengera ya Allahu Taala. Allahu Taala akufuna kulenga m'njira iyi. Monga tawonera, lingakhale liwu la umbuli, zosemphana ndi kuganiza, Sayansi ndi Chipembezo kunena kuti, "Munthu analenga chinthu chakuti chakuti.

Anthu ayenera kukonda Mlengi wapadera, Yemwe amalenga iwo, Yemwe amasunga ndi kupanga zinthu ndi kuwatumizira zomwe akufuna. Akuyenera kukhala antchito ndi akapolo Ake. Anthu ayenera kupembeza ndi kulemekeza Allahu Taala. Izi zalembedwa ku chiyambi Cha bukuli. Dzina la kukhalapo kofunika kwambiri uku, wa Umulungu Wapadera uwu, ndi wadziwika kuti ndi **Allah.** Anthu alibe ufulu wositha dzina lomwe Allahu Taala anayika kuti

azidziwika nalo. Ntchito iliyonse yochitika popanda kukhala ndi ulamuliro wotero idzakhala yolakwika kwambiri ndi yonyansa.

Akhirisitu ndi azibusa awo amakhulupirira kuti pali olenga atatu. Zokambirana zomwe tafotokozazi zikutsimikizira kuti pali mlengi mmodzi yekha ndi kuti mfundo zomwe zimaperekedwa ndi a Chikhristu ndi ansembe awo ndi abodza komanso ampatuko.

**-7-**

## "SALAFIYYA"

Ndiyambe ndi kunena kuti ophunzira a Ahl asSunna "rahmatallahi taala alaihim ajmain" sananenepo chirichonse mu dzina la "Salafiyya" kapena "madhhab a Salafiyya" m'mabuku awo. Maina awa omwe anapangidwa ndi anthu osatsatira madhhab (ostsatira mahhab a Ahl as-Sunna). Ndipo awanda kudzera m'mabuku awo otanthauziridwa kuchokera ku Chiarabu ndi anthu omwe ndi mbuli zachipembezo.

Malingana ndi Iwo:

*"Salafiyya ndi dzina la madhhab omwe ankatsatiridwa ndi ma Sunni onse poyamba madhhab a Ashariyya ndi Maturidiyya asanakhazikitsidwe. Amatsatira mmapazi a Swahaba ndi maTabiun*[1]*. Madhhab a Salafiyya ndi madhhab a maSwahaba, maTabiun ndi ma Taba at-Tabiin. Ma imam anayi akuluakulu aja anali m'madhhab amenewa. Buku loyamba kukamba za madhhab a Salafiyya ndi* ***Al-Fiqh al-akbar*** *lolembedwa ndi al-Imam al-azam. Mu buku lake,* ***Iljam al-awam anil-kalam****, al-Imam al-Ghazali analemba zafunika za madhhab a Salafiyya zisanu ndi ziwiri (7). Ilm al-kalam (maphunziro kapena zikhulupirira za iman), za ma mutaakhkhirin (Omwe anabwera pambuyo pawo) pambuyo pa kutuluka kwa Imam al-Imam. Ataphunzira ma madhhab a akatswiri a maphunziro a kalam ndi maganizo a anamatetule a Chisilamu bwino, al-Imam al-Ghazali anasintha zinthu zina mmachitidwe a ilm al-kalam. Iye anaikamo maganizo akuya mu ilm al-kalam ndicholinga chotsutsa. Ar-Radi ndi al-Amidi adaphatikiza kalam ndi nzeru zakuya ndi kuzipanga kukhala nthambi imodzi ya chiziwitso. Ndipo al Baydawi anapanga kalam ndi nzeru zakuya kukhala chimodzi. Ilm al-kalam ya ma mutaakhkhirin ndiye inalepheretsa kufalitsa kwa madhhab a Salafiyya. Ibn Taimiyya ndi otsatira wake Ibn al-Qayyim al-Jawziyya anayetsetsa kubwezeretsa madhhab a*

[1] ***Swahaba al-Kiram****: ndi Asilamu omwe adamuwona Mtumiki alahi-salam kosachepera kamodzi; omutsatira.* ***Tabi'un*** *(****al-izam****): ndi Asilamu a m'bado wa chiwiri omwe anawona (m'modzi mwa) Swahaba al-Kiram ndi analandira ma Hadith kuchokera kwa iwo.* ***Taba al-Tabi'un****: Akatswiri achisilamu omwe anawona (m'modzi mwa) Tabi'un.*

*Salafiyya omwe pambuyo pake anagawikana pa wiri: ma salafi oyambirira samafotokoza mwatsatanetsatane za zizindikiro za Allahu Taala ndi ma ayah ndi ma hadith a matanthauzo obisika (mutashabih nasses). Ma salafi otsatira amatsindika za kufunika kwa tsatanetsatane wa iwo. Nkhaniyi ikuwoneka bwino ndi ma Salafi otsatira monga Ibn Taymiyya ndi Ibn al-Qayyim al-Jawziyya. Salafi yoyambilira ndi ya pambuyo, onse awiri, amatchedwa* ***Ahl as-Sunna al-khassa*** *(njira ya Ahl as Sunna). Anthu okhala ndi kalam omwe anali a Ahl as-Sunna anawafotokoza zina mwa ma ayah komanso ndi Hadith sharif, koma ma Salafiyya ankatsutsa izi. Ponena kuti 'nkhope' ya Allah ndi 'kudza' Kwake n'zosiyana ndi nkhope munthu ndi kubwera. Ma Salafiyya amasiyana ndi ma Mushabbiha( anthu omwe amati Allahu Taala ndi chinthu chogwirika)."*

Ndikulakwa kunena kuti ma madhhab a **al-Ash'ari ndi al-Maturidi** akhazikitsidwa mochedwerako. Ma imam awiri akuluakulu amenewa adafotokoza ndi kugawa bwino uthenga wa itiqad (dongosolo la zikhulupiriro) zomwe zinaperekedwa ndi Salaf as-salihin (mibado itatu yoyamba ya Asilamuyomwe ndi ma Swahaba al-Kiram, ma Tabi'un ndi Tabi' al-Tabi'un). Iwo anagawa bwino izi kwa achinyamata. Al-Imam al-Ashari anali mu mndandanda wotsatira omwe amatsatira a Al-Imam ash-Shafii . Ndipo Al-Imam al-Maturidi anali mlumikizi wamkulu wa otsatira a al-Imam al-azam Abu Hanifa's. Al-Ashari ndi al-Maturidi sanasiye njira ya aphunzitsi awo mu madhhab pa itiqad. Sadayambitse ma madhhab ena. Awiri awa, aphunzitsi awo ndi ma imam anayi ama madhhab aja anali ndi itiqad imodzi yomwe ndi madhhab amu itiqad yotchedwa **Ahl as-Sunna wa'l Jamaa**. Itiqad kapena zikhulupiriro za anthu awa ndi zofanana ndi zomwe zinali ndi ma Swahaba al-Kiram, ma Tabi'un ndi Tabi al-Tabi'un. Buku la **Al-Fiqh al-akbar** lolembedwa ndi al-Imam al-azam Abu Hanifa, likuikira kumbuyo Madhhab a Ahl as-Sunna. Mawu oti 'Salafiyya' sakupezeka mu buku limenelo ngakhale m'bukhu la al-Imam al-Ghazali lotchedwa **Iljam al-awam anil-kalam** mulibe. Mabuku awiri amenewa ndi bukhu la **Al-qawl al-fasl**[1], imodzi mwa ndemanga pa buku la **Al-fiqh al-akbar**, limaphunzitsa za Madhhab a Ahl as-Sunna ndi kuyankha za magulu a anthu opatuka ndi ma Filosofa. Al-Imam al-Ghazali analemba m'bukhu lake la **Iljam al-awam**: "M'bukhu ili ndidzanena kuti, mwa magulu a mu itiqad, madhhab a Salaf ndi owona. Ndidzafotokoza kuti amene angasiye madhhab awa adzakhala anthu a bida. Madhhab a Salaf akutanthauza itiqad ya ma Swahaba al-Kiram ndi ma Tabi'un. Msichi za madhhab amenewa zilipo zisanu ndi ziwiri." Monga zikuonekera, buku la **Iljam** latchula msichi zisanu ndi ziwiri za Madhhab a 'Salaf.' Ponena kuti ndi zofunikira za "Salafiyya' komwe kuli kupotoza zolemba bukulo

[1] Mabukhu a **Iljam** ndi **Al-qawl al-fasl** apangidwanso ndi a Hakikat Publications ku Istanbul.

komanso kunena molakwika za al-Imam al-Ghazali. Pafupifupi mabuku onse a In Ahl as-Sunna, mwachitsanzo, pa mutu wa "**kuchitira umboni**" za **Ad-durr al-mukhtar**, buku lofunika la Fiqh, 'Salaf' ndi 'Khalaf' zikukanidwa kuti: " 'Salaf' (oyamba kukhalapo) ndi dzina lina la Swahaba al-Kiram ndi Tabi'un. Amatchedwanso **Salaf as-salihin**. Ndipo ophunzira a Ahl as-Sunna omwe anabwera mmalo mwa ma Salaf as-salihin amatchedwa '**Khalaf.**' (olowa mmalo)." Al-Imam al-Ghazali, al-Imam ar- Radi and al-Imam al-Baydawi, anali a madhhab a Salaf as-salihin. Magulu a bida omwe analipo mu nthawi imeneyo ankasakaniza ilm al-kalam ndi mzeru za patali (Filosofe). Buku la **Al-milal-wan-nihal** lapereka mwatsatanetsatane uthenga wa zikhulupiriro za magulu opatukawa. Poteteza itiqad ya Ahl as-Sunna kwa magulu achinyengowa ndi kutsutsa maganizo awo opatuka, ma imam atatu amenewa anawayankha mozama pa maganizo awo. Kuyankha kwawo sikunatanthauze kusakaniza mzeru (Filosofe) ndi madhhab a Ahl as-Sunna; koma amayeretsa uthenga wa kalam ndi kuchotsamo maganizo ochokera mu mzeru zao. Mu ntchito ya al-Baydawi, mulibe maganizo filosopfe kapena njira za filosofe; ngakhale mu tafsir ya **Shaikh-zada**, zofotokozera zofunika kwambiri**.** Ndi mnyozo waukulu kunena kuti ma imam awa anatanganidwa ndi Filosofe. Mnyozo uwu unayamba kunenedwa pa ophunzira kwambiri a Ahl as-Sunna ndi Ibn Taymiyya m'bukhu lake la **Al-wasita**. Kuonjera apo, Ibn Taymiyya ndi omutsatira wake Ibn al-Qayyim al-Jawziyya anayetsetsa kudzutsanso Madhhab a Salafiyya ndipo izi zikuonetsa kusiyana kwa omwe Ali mu njira yoona ndi awo omwe akupatukira kosochera. Anthu awiriwa asanabwere, panalibe madhhab otchedwa "Salafiyya," kapena mawu oti 'Salafiyya.' Ndiye anganene bwanji kuti amayesera kudzutsanso Madhhab omwe chikhalirecho kunalibe. Iwo asanabwere panali madhhab amodzi okha a Salaf as-salihin omwe ngati itiqad yolondola imodzi, amatchedwa **Ahl as-Sunna wa'l Jamaa**. Ibn Taymiyya anayesera kusokoneza madhhab olondolawa ndi kubweretsa za bida zambiri. Bukhu lokhalo lomwe ndi gwero la maganizo achinyengo ndi bodza la anthu opanda madhhab mu nthawi ino komanso anthu osintha chipembezo ndi ma bida ndi la Ibn Taymiyya. Pofuna kutsimikizira achinyamata kuti akutsatira njira yolondola, iwowa anapanga njira yoopsa: anasintha dzina la "Salaf as-salihin" ndi kukhala "Salafiyya" ndicholinga choti abweretse ma bida a Ibn Taymiyya ndi maganizo a chinyengo ngati olondola ndi kuwakokera achinyamata ku njirayi. Anayetsetsa kupaka madontho a Filosofe ndi bidah Asilamu ophunzira kwambiri omwe analowa mmalo Salaf as-salihin ndi kunena kuti iwowo ndi amene anapatuka ku Salafiyya. Anamuchemerera Ibn Taymiyya ngati mujtahid, ngati ngwazi yomwe idadzutsa Salafiyya. Koma, ophunzira a Ahl as-Sunna rahmt-Allahi Taala alaihim ajmain, omwe ndi amlowa mmalo a Salaf as-salihin,

akhala akuteteza ziphunzitso za itiqad ya Ahl as-Sunna zomwe zapanga madhhab a Salaf as-salihin. Iwo akhala akulemba mabuku mpaka pano ndipo amanena kuti Ibn Taymiyya, ash-Shawkani ndi ena asiya kutsatira njira ya Salaf as-salihin ndipo akhala akukokera Asilamu ku chionongeko.

Anthu omwe amawerenga mabuku ngati **At-awassuli bin-Nabi wa bis-salihin, Ulama al-Muslimin wal-mukhalifun, Shifa as-siqam ndi Tathir al-fuad min danasil-itiqad**, mau oyamba a bukhu lomaliziralo adzawazindirikitsa kuti opanga maboza a zikhulupiriro za chinyengo "Salafiyya watsopano" akutengera Asilamu kuchionongeko ndipo akuononga chisilamu kuchokera mkati mwake.

Masiku ano ngati anthu akutchula mawu oti Salafiyya,' msilamu aliyense adziwe kuti mu Chisilamu mulibe dzina la madhhab a Salafiyya koma kuti kuli madhhab amodzi okha a **Salaf as-salihin,** omwe ndi Asilamu oyambirira a zaka mazana awiri oyambaa Chisilamu; Chsilamu chake chomwe chinachemereredwa mu Hadith sharif. Akatswiri ophunzira a Chisilamu a zaka mazana achitatu ndi achinayi amatchedwa **Khalaf as-sadiqin**. Itiqad ya anthu olemekezeka amenewa imatchulidwa kuti **madhhab a Ahl as-Sunna wa'l Jamaa**. Awa ndiye ndi madhhab a iman, kukhulupirira. Iman yomwe anali nayo ma Salaf as-salihin, awatu ndi ma Swahaba al-Kiram ndi Tabi'un inali yofanana. Panalibe kusiyana pa zikhulupiriro zao. Masiku ano Asilamu ambiri pa dziko lapansi ali mu Madhhab a Ahl as-Sunna. Magulu onse 72 opatuka a bida anayamba kuoneka pambuyo pa zaka mazana a chiwiri a Chisilamu. Ngakhale kuti ena mwa oyambitsa maguluwa amenewa analipo kale koma mabuku awo anayamba kulembedwa nthawi ya ma Tabi'un atadutsa. Ndi pomwe anayamba kupezeka mmagulu ndi kumapanga zosamvera Ahl as-Sunna.

Rasulullah "sallallahu alaihi wa sallam" anawulula zikhulupiriro za Ahl as-Sunna. Ma Swahaba al-Kiram anatengera maphunziro a Iman kuchokera kwa Mtumiki. Ndipo ma Tabi'un al-Izam (Tabi'un olemekezeka kwambiri), mu nthawi yawo anaphunzira maphunzirowa kuchokera kwa Swahaba al-Kiram. Ndipo obwera pa mbuyo pawo adaphunzira kwa iwo; poteromo ziphunzitso za Ahl as-Sunna zinafika kwa ife mu naql (uthenga wofalitsa popatsirana) ndi tawatur (kufalitsa kwa uthenga wa Chisilamu wa pachiyambi, wosakayikitsa ndi wolondola, potsatiza ndi kubwereza-bwereza kuchokera kwa odziwa kwambiri). Ziphunzitsozi sizingafufuzidwe mwa kulingalira. Nzeru sizingasinthe koma zimangothandiza kumvetsetsa. Luntha ndi lofunikira pofuna kumvetsetsa ziphunzitsozi. Luntha limathandizanso kuzindikira kulondola kwa ziphunzitsozi komanso kufunika kwake. Akatswiri onse a Hadith ankakhulupirira za Ahl as-Sunna. Ma imamu a Madhhab anayi okhudzana ndi amal (Ntchito, miyambo, kupembedza, fiqh), nawonso anali m'ma madhhab amenewa. Komanso al-Maturidi ndi al-Ashari, ma Imam athu awiri a Madhhab okhudzana ndi itiqad

(zikhulupiriro), anali mu Madhhab a Ahl as-Sunna. Ma Imamu onse awiriwa analengeza za Madhhab amenewa. Nthawi zonse ankateteza Madhhab imenewa kwa anthu ampatuko ndi okonda chuma, omwe anali osunga nzeru za Chigiriki zakale. Ngakhale kuti anali anthu a m'nthawi imodzi, iwo ankakhala malo osiyana. Kaganizidwe ndi makhalidwe a anthu owukira omwe amatsutsana nawo kunali kosiyana, kotero ma imam awiriwa njira zodzitetezera ndi zotsutsira zinali zosiyana. Koma izi sizikutanthauza kuti iwo anali a Madhhab osiyana. Akatswiri odziwa kwambiri zikwi zikwi ndi awliya omwe anabwera pambuyo pa ma imamu awiri ophunzira kwambiriwa [kwa zaka mazana ambiri] anaphunzira mabuku awo ndi kunena mogwirizana kuti onsewo anali a Madhhab a Ahl as-Sunna. Koma anthu a m'magulu ampatuko ndi opanda madhhabi sadachedwe kusintha miyambo (ibadat) ndi ziphunzitso za iman mogwirizana ndi zimene anamva kwa nzeru a Achigiriki ndi a Sayansi abodza, omwe anali adani a Chisilamu.

Boma la ma Ottoman linkateteza Chisilamu ndi akatswiri a Chisunni. Koma bomali litagawidwa, a misshoni pogwiritsa mphamvu ndi mfundo za Ufumu wa Britain anagwira ntchito zao zonyansa zaka zambiri. Iyi ndi nthawi yomwe anthu opanda madhhab anapeza mwayi wosokoneza kwambiri. Ndi mabodza awusatana ndi zinyengo, iwo anayamba kuukira Ahl as-Sunna ndi kuyamba kugwetsa Chisilamu kuchokera m'mkati mommo. Izi zinachitika makamaka m'mayiko ngati Saudi Arabia, kumwe akatswiri a Ahl as-Sunna saloledwa kuyankhula momasuka. Chipongwechi chinafalikira ponseponse pa dziko lonse chifukwa cha golide wa nkhaninkhani yemwe ma Wahabi anapereka pogwira ntchitoyi. Malinga ndi malipoti ochokera m'mayiko a Pakistan, India ndi Africa anthu ena ogwira ntchito za chipembedzo koma opanda maphunziro achipembedzo okwanira ndi osamuopa Allahu Taala anapatsidwa ma udindo ndi nyumba zogona ngati malipilo pothandizira adaniwa. Anthu osakhulupirikawa anapeza mphoto zoipazi pogwira ntchito yonyenga achinyamata ndi kuwalekanitsa kuchokera m'madhhab a Ahl as-Sunna. M'bukhu limodzi lomwe analemba ndi cholinga chosocheretse Ophunzira achisilamu m'ma madrasas (sukulu yamaphunziro achisilamu) komanso ana Asilamu, wolembayo akuti: "Ndalemba buku ili ndi cholinga chothetsa tsankho la madhhab ndi kuthandiza aliyense kukhala mwa mtendere m'madhhab awo." Munthu uyu akutanthauza kuti njira yothetsera tsankho la madhhab ndi kuukira Ahl as-Sunna ndi kuwanyoza akatswiri a Ahl as-Sunna. Akubaya Chisilamu ndi lupanga, kenako ndikumati akuchita izi kuti Asilamu azikhala mwamtendere! Pa malo ena m'bukhulo, iye anati: "Ngati munthu alingalira [za funso] ndi kulipeza yankho lolondola, adzafupidwa ka khumi. Akaphonya adzalandira mphotho imodzi." Izi zikanakhala zoona ndiye kuti aliyense,

ngakhale ali Mkhrisitu kapena Mushrik (omwe amaphatikiza zinthu ndi Allahu Taala, a shirk), akanadzalipidwa pa malingaliro awo onse. ndi kupeza thawab khumi pa malingaliro awo olondola! Taonani momwe amasinthira Hadith sharif ya Mtumiki wathu "swallaallaahu 'alayhi wa aalihi wa sallam", ndi mmene akuchitira chinyengo! Hadith sharif imanena kuti: "**Ngati mujtahid amaliza molondola pomwe akutulutsa malamulo [okhudzana ndi amal] kuchokera mu ayah karima kapena mu hadith sharif, iye adzapatsidwa thawab khumi. Ngati walakwa adzapatsidwa thawab imodzi**." Zomwe zikuwonetsa kuti mphothozi sikuti zidzaperekedwa kwa aliyense amene akuganiza ayi. Koma kwa katswiri wa Chisilamu yemwe anapita patsogolo mpaka pa mlingo wa ijtihad ndipo kuti adzapatsidwa osati chifukwa cha lingaliro lawo lililonse koma chifukwa cha ntchito yochotsa malamulo ku nasses [okhudzana ndi amal]; chifukwa ntchito yawo ndi Ibada (ntchito ya chisilamu). Thawab imaperekedwa chifukwa cha izi, monganso zimaperekedwa pa ibada iliyonse.

Mu nthawi ya Salaf as-salihin ndi ya ophunzira a mujtahid omwe anali otsatira awo, mpaka pamapeto pa zaka mazana anayi a chisilamu, pamati pakapezeka nkhani yatsopano yokudza kusintha kwa mmene anthu akukhalira, ophunzira a mujtahid ankayesetsa usana ndi usiku ndi kupeza yankho kuchokera mu magwero anayi otchedwa **al-adillat ash-Shariyya** mmene nkhaniyi ingayendetsedwere. Ndipo Asilamu onse ankayendetsanso vuto ngati lomwelo potengera mmene Imam wa Madhhab awo waonera pa nkhaniyi. Akatswiri ophunzira kwambiri omwe amachita izi amapatsidwa thawab khumi kapena imodzi. Zaka mzana anayi atadutsa, anthu anapitiriza kutsatirabe mayankho omwe ma Imam awo anapeza. Pa nthawi yayitali imeneyo, panalibe msilamu ngakhale mmodzi yemwe mavuto lake silinayankhidwa. Pa mbuyo pake, panalibe ophunzira kwambiri kapena ma mufti omwe anaphunzira ngakhale kufikira pa mlingo wa 7 wa mujtahid. Choncho, masiku ano tikuyenera kuphunzira kuchokera kwa msilamu yemwe angathe kuwerenga ndi kumvetsa ma buku a m'modzi mwa ophunzira kwambiri a ma Madhhab anayi aja, ndi mabuku omwe anatanthauzira. Tipange ibadah yathu ndikukhala moyo wathu wa tsiku lililonse ngati mmene Imam wao ankachitira kuchokera mmabukumo. Allahu Taala adapereka malamulo a chilichonse mu **Quran al-karim**. Mtumiki wake wa pamwamba, Muhammad alaihi-salam anafotokozera onse. Ophunzira kwambiri a Ahl as-Sunna, anaphunzira malamulowa kuchokera kwa ma Swahaba al Kiram ndi kuwalemba m'mabuku. Mabuku amenewa akupezeka pa dziko lonse tsopano. Mmene anthu angachitire chinthu chilichonse chomwe chingagwe kwina kulikonse pa dziko lapansi mpaka kutha kwa dziko chitha kufananizidwa ndi uthenga womwe uli mmabukuena. Kuthekera uku ndi chozizwa **(mujiza)** Cha **Quran al-karim**. Komanso ndi ukatswiri wapaderadera

(karama) wa ophunzira kwambiriwa achisilamu. Zowonadi, ndi kofunikira kuphunzira machitidwe a zinthu zomwe wakumana nazo pofunsa Msilamu wowonadi wa Sunni. Munthu yemwe angafunse munthu wachipembezo koma wosatsatira Madhhab ali wonse, adzasocheretsedwa ndi yankho losemphana ndi ma buku a fiqh.

Monga tawonera pamwambapa, achinyamata amanyengedwa ndi mbuli zosatsatira madhhab zochokera ku Pakistan ndi India. Mbuli zimenezi zimakhala zitakhala ku mayiko achiarabu kwa zaka zingapo komwe amaphunzira kuyankhula Chiarabu ndikutaya nthawi yawo kukhala moyo wa manyado, wosangalala ndi kuchita machismo. Kenako amapeza pepala losindikizidwa kuchokera kwa anthu wosakhala ndi madhhabi amene amadana ndi Ahl as-Sunna. Achinyamata omwe amaona mapepala awo abodzawa ndi kumawamva akuyankhula charabu amaona ngati iwowa ndi ozindikira pa chipembezo. Koma awa ndi anthu omwe sangamvetse angakhale buku la fiqh. Sadziwa chirichonse za chiphunzitso cha fiqh m'ma buku. Ndipo sakhulupirira maphunzira a chiphunzitso. za zi ndipo amadzitcha tsankho. Kuyambira kale, akatswiri a Chisilamu ankafufuza mayankho m'mabuku a fiqh ndipo amapereka mayankho kuchokera mu zomwe amapeza. Koma anthu osatsatira Madhhab ali wonse Chifukwa chakusatha kuwerenga ndi kumvetsa mabuku a fiqh, ankasokoneza wofunsayo ponena chili chonse chomwe chamabwera m'mutu mwake mwaumbuli ndi mwa maganizo osakwanira. Izi zomasocheretsa anthu ndikuwapangitsa kukalowa ku Gahena. Ndichifukwa chake Mtumiki "sallallahu taala alaihi wa sallam" ananena kuti: **"Katswiri wa maphunziro wophunzira bwino ndi munthu wopambana mwa anthu onse. Katswiri wa maphunziro wasaphunzira wabwino ndi munthu woyipitsitsa mwa anthu onse.** Hadith sharif iyi ikuonetsa kuti ophunzira kwambiri a Ahl as-Sunna ndi apamwamba pa anthu onse, ndipo anthu osatsatira Madhhab ali wonse ndiwo anthu oipitsitsa. Ophunzira kwambiri amatsogolera anthu kutsatira Mtumiki, komwe kuli kuwatengera anthu ku Mtendere. Pomwe Ophunzira mosakwanira ndi maganizo awo opatuka amatengera anthu ku moto.

Ibn Khalifa Aliwi, yemwe anaphunzira pa Islamic University of Jami al-Azhar, adalemba mu bukhu lake la **Aqidat as-Salafi wal-khalaf**: "As 'Allama Abu Zuhra walemba m'buku lake la **Tarikh a-lmadhahibi-l Islamiyya** kuti, anthu ena, omwe anapatuka m'Madhhab a Hanbali mu zaka mazana anayi pakutha pa Hijra anadzitchula okha **ma Salafiyyin**. Abul-Faraj ibn al-Jawzi rahmat-Allahi Taala alaih ndi ophunzira ena a Madhhab a Hanbali , analalikira kuti ma Salafi amenewo sanali otsatira a Salaf as-salihin ndikuti anali anthu opanga za bidah a m'gulu la Mujassima. pochita izi analepheretsa kufalikira kwa fitna

(zoyankhula ndi zochita zowononga asilamu ndi chisilamu) yawoyi. Mu zaka mazana asanu ndi awiri, Ibn Taymiyya adayambitsanso fitna yawoyi."[1]

Anthu osatsatira madhhab anatenga dzina la 'Salafiyya' ndi kumutchula Ibn Taymiyya 'Imam wamkulu wa ma Salafi'. Mawu awa ndi oona mu ulemu umodzi popeza mawu akuti 'Salafi' panalibe iye asanakhalepo. Panali Salaf as-salihin omwe Madhhab awo anali a Ahl as-Sunna. Zikhulupiriro za mpatuko za Ibn Taymiyya ndiye gwero la Ma Wahhabi ndi anthu ena omwe alibe madhhabi. Ibn Taymiyya anaphunzitsidwa m'Madhhab a Hanbali, kutanthauza kuti anali wa Sunni. Koma pamene amaonjezera maphunziro ake ndikufika kalasi ya fatwa, aaayamba kusilira malingaliro ake. Anadzimva kuti wafikapo pa akatswiri a Ahl as-Sunna "rahmatallahi taala alaihim ajmain" Kuwonjezeka kwa maphunziro ake kunabweretsa mpatuko. Sanalinso mu Madhhab a Hanbali, chifukwa kukhala mu imodzi mwa Madhhab anayiwa kumafunaka kukhala ndi zikhulupiriro za Ahl as-Sunna. Munthu wosakhulupirira mu Ahl as-Sunna sanganenedwe kuti ndi wa mu Madhhab a Hanbali.

Anthu osakhala madhhabi amatenga mpata uliwonse kulankhula zoipa za anthu a Sunni ogwira ntchito za chipembedzo m'dziko lawo. Amagwiritsa ntchito njiri iliyonse kutsekereza kuti mabuku a Sunni asamawerengedwe ndipo ziphunzitso za Ahl as-Sunna zisaphunziridwe. Mwachitsanzo, pakatchuladwa dzina langa, wosatsatira madhhab amati: "Kodi munthu wa za mankhwala akudziwanji za maphunziro a chipembedzo? Iye ayenera kugwira ntchito mu nthambi yake osati kusokoneza za chibembedzo zathu." Kuyankhula kwa umbuli ndi kopusa bwanji! Iwo amaganiza kuti munthu wasayansi sangakhale ndi chidziwitso cha chipembedzo. Iwo sadziwa kuti Msilamu wa Sayansi amawona mphamvu ya umulungu (Sun' al-Ilahi). Mphindi iliyonse, zindikirani Ungwiro wa Mlengi Wamkulu umene uli wawonetsedwa m'buku lotchedwa "**Creator and Creation**", ndi kuona kulephera kwa zolengedwa poyerekeza ndi mphamvu za Allahu Taala, zopanda malire, kutsimikizira pokweza mosalekeza (tashbih) Allahu Taala. Zindikirani kuti Iye ali kutali ndi zolakwa zonse (tanzih). Katswiri wotchuka wa sayansi ya nyukiliya wa ku Germany, Max Planck, anafotokoza izi momveka bwino mu buku lake **Der Strom**. Koma mbuli zosakhala m'madhhabzi, podalira pepala lomwe angakhale atapeza kwa mlendo ampatuko monga iye mwini, ali pa mpando wopatsidwa ndi ampatuko, atakomedwa ndi kukongola kwa golide wogawidwa kuchokera kunja, amaziona

[1] Aqidat as-Salafi wal-khalaf, bukhu la masamba 340, losindikizidwa ku Damasiko mu 1978/1398. Amipatuko ingapo (bidas) ya ma Salafi ndi ma Wahhabi analemba miseche yawo ya Ahl as-Sunna ndipo mayankho zomwe analembazo zayankhidwa mwatsatanetsatane

ngati iye yekha ndi amene ali ndi mphamvu pa chidziwitso chachipembedzo. Allahu Taala amutsogolere munthu wosauka nu uzimuyu ndi ife tonse. Atetezanso achinyamata osalakwa ku misampha ya mbava za chipembedzozi zomwe zikugwiritsa ntchito zolembedwa zabodza. Amina!

Ndipotu, ndinatumikira mtundu wanga modzichepetsa kwa zaka zoposa 30 monga wa Famase ndi Chemical engineer (munthu wopanga makina ofunikira pa kupanga mankhwala). Komabe kuti ndipeze maphunziro a chipembedzo, ndinagwira ntchito usana ndi usiku kwa zaka zisanu ndi ziwiri, ndipo ndinalemekezekadwa ndi ijaza (diploma yochitira umboni kuti mwiniwakeyo ali ndi Chidziwitso cha Chisilamu) yomwe inaperekedwa ndi katswiri wamkulu wa Chisilamu, Sayyid Abdulhakim Arwasi, rahmat-Allahi Taala alaih. Pakumva ukulu wa chidziwitso cha sayansi ndi chipembedzo, ndinawona kupelewera kwanga. Pakumva kumeneku ndinayesa kukhala kapolo woyenerera wa Allahu Taala. Mantha anga akulu ndi nkhawa zanga zinali kuwopa kugwa mmayeselo odzitama chifukwa cha ma dipuloma anga mu ijaza komanso mu Sayansi. Ndikuziona ngati ndi ine odziwa mu zonsezi. Mantha angawa atha kuoneka mu zolemba zanga. Sindinalembe maganizo anga m'mabuku anga onse. Nthawi zonse lembera azichimwene wanga zolemba za phindu za ophunzira akuluakulu a Ahl as-Sunna zomwe zinali zosililidwa ndi anthu omwe ankamvetsa kufunika kwake, pomasulira kuchokera ku Chiarabu kapena chi Persia. Chifukwa cha mantha anga, ndinalibe maganizo olemba buku; nditaona Hadith sharif pa tsamba loyamba la **As-sawaiq al- muhriqa**, "**fitna ikakula ndi kuwanda, yemwe akudziwa akuyenera kudziwitsa ena za chilungamo. Akapanda kutero, atha kutembereredwa ndi Allah komanso anthu onse!"** ndinayamba kuganizira. Mbali ina, pamene ndimaphunzira za kupambana mu nzeru ndi kumvetsa kwa ophunzira akuluakulu a Ahl as-Sunna, kukwima mu ubongo kwawo m'maphunziro achipembedzo ndi kudziwa kwawo za sayansi mu nthawi yawo komanso kupirira kwao pa ibadah ndi taqwa, ndinachita manyazi. Ndidawona kuti zomwe ndinkadziwa zinali ngati dontho limodzi mu nyanja yaikulu poyerekeza ndi ophunzira akuluakuluwo. Komanso ndidamva chisoni poona kuti anthu ochepa okha opembeza Allahu Taala ndi amene ankatha kuwerenga ndi kumvetsetsa mabuku olembedwa ndi ophunzira a Ahl as-Sunna; ndipo kuti mbuli za anthu, opatuka analowerera mwa anthu ogwira ntchito ya achipembezo ndipo anali atalemba mabuku awo achinyengo ndi opatuka. Chiwopsezo cha chiwonongeko chomwe chinalengezedwa mu Hadith ash-sharif chinandichititsa mantha. Komanso chifundo ndi chisoni chomwe ndidali nacho pa achinyamata okondeka chinandipangitsa kuwatumikira. Ndinayamba kusankha zoti ndimasulire kuchokera m'mabuku a ophunzira akuluakulu a Ahl as-Sunna. Pambali pa makalata osawerengeka othokoza ndi kuyamikira omwe

ndanalandira nthawi ndi nthawi, Ndinakumana ndi ondidzudzula ndi kunyoza kuchokera kwa anthu osatsatira madhhab alionse. Chifukwa sindinkakayikira cholinga change chabwino pa ikhlas ndi kukhulupirika mwa Mlengi wanga, kudzidalira ndekha kwa Allahu Taala komanso kupanga tawassul (kufuna kupembedwerera) ndi mzimu wodalisika wa Mtumiki “sallallahu taala alaihi wa sallam” ndi asilamu onse ozipereka, ndinapitiriza ndi utumiki wanga. Allahu Taala atisunge tonse m'njira yoona yomwe amakondwera nayo! Amin

Katswiri wamkulu wa Hanafi, Muhammad Bahit al-Mutii, pulofesa wa pa yunivesite ya Jami al-Azhar ku Egypt, analemba m'buku lake lotchedwa **Tat'hir al-fuad min danisil-i'tiqad**: “Mwa anthu onse, Atumiki alaihimus-salatu wassalam ali ndi miyoyo yapamwamba komanso yokhwima kwambiri. Anatetezedwa ku kulakwa, kulakwitsa, kusazindikira, kusakhulupirika, tsankho, kukakamira, kutsatira nafs, mkwiyo ndi udani. Atumiki amalumikizana ndi kufotokozera zomwe zinawululidwa kwa iwo ndi Allahu Taala. Ziphunzitso, malamulo ndi zoletsa zomwe anauzidwa iwo, zonse ndi zoona. Palibe cholakwika kapena chachinyengo. Pambuyo pa Atumiki, anthu apamwamba komanso okhwima kwambiri anali sahaba (abwenzi) awo popeza anaphunzitsidwa, anali okhwima ndi woyeretsedwa mu suhba (ubwenzi wa Mtumiki kapena wali) wa Mtumiki. Nthawi zonse amalankhula ndi kufotokoza zomwe anamva kuchokera kwa Atumiki. Zonse ankanena, zinali zoona, iwo ali kutali ndi zoyipa zomwe tazitchulazi. Sankatsutsana chifukwa cha tsankho kapena kukakamiea chabe, ndipo samatsatire nafs zawo. Kufotokoza ma Ayat ndi Hadith kwa ma Sahabat al-Kiram ndi kugwiritsa ntchito ijtihad podziwitsa za chipembedzo cha Allahu Taala kwa anthu Ake anali madalitso Ake aakulu pa Umma uwu (Asilamu) ndi chisoni Chake pa Mtumiki wokondedwa, Muhammad Alaihi-salam **Quran al-karim** ikunena kuti ma Sahabah al-Kiram anali olusa kwa osakhulupirira koma odekha komanso opirira kwa wina ndi mzake. Amapemphera Swala mwakama; ndi kuti amayembekezera chilichonse ndi mParadiso kuchokera kwa Allahu Taala Mwa ma Ijtihad awo, onse amene amavomerezana (Ijma) anali olondola. Onse anayenera kupeza thawab (malipiro pa tsiku lomaliza) koma Choonadi ndi chimodzi.

"Anthu apamwamba kwambiri pa mbuyo pa Sahabat al-Kiram ndi Asilamu omwe anawona ndi kuphunzitsidwa ndi suhba awo. Amatchedwa **Tabi’un**. Anapeza chidziwitso chawo cha chipembedzo chonse kuchokera ku Sahabat al-Kiram. Anthu apamwamba omwe ali pafupi ndi Tabi’un ndi Asilamu omwe anawona Tabi’un ndipo anaphunzitsidwa mu suhba yawo. Amatchedwa **Tabi’ al-Tabi’un**. Mwa anthu omwe akubwera zaka mazana pa mbuyo pawo, mpaka tsiku lofunsidwa, Wapamwambamwamba ndi abwino ndi omwe amatsatira ndikuchita monga iwo. Omwe amaphunzira chiphunzitso chawo ndi kutsatira

mapazi awo. Pakati pa anthu antchito zopembedza obwera pambuyo pa **Salaf as-salihin** (mibadwo itatu yoyambirira ya Asilamu yomwe ndi Sahaba, Tabi'un ndi Tabi' al-Tabi'un), Munthu wa luntha ndi wanzeru yemwe mau ndi zochita zake ndi zogwirizana ndi chiphunzitso cha Rasulullah ndi Salaf as-salihin, amene sasiya njira yawo m'chikhulupiriro ndi zochita zawo; ndipo sapyola malire a Chisilamu, saopa ena kunena zoipa za iye. Posatsatira anthu otere (onena zoipa za iye ndi chipembedzo chake) sakusiya njira yoongoka. Iye samamvera mawu a mbuli. Iye satsatira chifuniro chake ndipo potero satuluka m'madhhab anayi a ma imamu mujtahid. Asilamu ayenera kupeza katswiri wotero, kumufunsa ndi kuphunzira zomwe iwo sakuzidziwa ndipo ayenera kutsatira malangizo ake m'chilichonse chimwe amachita. Chifukwa katswiri ngati ameneyo, amadziwa ndi amadziwitsa anthu mankhwala auzimu (chidziwitso chochiritsa mzimu) chomwe Allahu Taala analenga kuti choteteza zolengedwa Zake kuti zisalakwe. Komanso kuti zolengedwazo zikhale zolondola nthawi zonse. Iye akhoza kuchiritsa amene miyoyo yawo ikudwala ndi amene kumva kwawo kuli ndi malire. Chilichonse chomwe katswiri wotero anganene, kuchita kapena kukhulupirira kuti ndi chogririzana ndi Chisilamu. Amamvetsa chilichonse molondola. Amayankha funso lililonse molondola. Allahu Taala ndi radi (kupereka chilolezo kwa, kukondwera, kukhutitsidwa) ndi zonse zomwe amachita. Allahu Taala akusonyeza njira zopitira ku rida Yake (chilolezo cha Allahu Taala). Allahu Taala amapulumutsa amene ali ndi Iman ndi omwe amakwaniritsa zofunika za iman, kuchoka ku kuponderezedwa ndi mavuto. Iye amapanga kukhala ndi nur (kuwala), chisangalalo ndi chipulumutso. Nthawi zonse, ndi mu zonse zomwe amachita, amakhala omasuka ndi otonthozedwa. Pa tsiku la kuuka kwa akufa adzakhala pa mbali pa Atumiki siddiq (amene ali okhulupirika kwa Mtumiki; abwino, onena zoona nthawi zonse), ofera chikhulupiriro ndi salih (oopa Mulungu, kupewa machimo) Asilamu.

"Ziribe kanthu kuti iye amakhala mu zaka zana ati, koma ngati munthu wa udindo wa chipembedzo sakutsatira zonena za Mtumiki ndi Sahaba, ngati mawu ake, zochita zake ndi zikhulupiriro zake sizikugwirizana ndi zophunzitsa zawo, ngati akutsatira nafs zake ndi maganizo ake ndipo akupyola malire a Chisilamu, kapena ngati iye, akutsatira nzeru zake, kutsutsa zinthu zosakwima za Chisilamu ndi kudutsa malire a Madhhab zinayi m'ziphunzitso zimene iye sangazimvetse,iye adzaweruzidwa kukhala munthu wa udindo wa chipembedzo woyipa. Allahu Taala wamata mtima wake; maso ake kuona njira yolondola ndipo makutu ake sangamve mawu oyenera. Kudzakhala kuzunzika kowawa kwa iye pa Tsiku Lomaliza. Allahu Taala sakumukonda. Anthu otere ndi adani a Mtumiki. Iwo amaganiza kuti ali m'njira yoyenera. Amakonda khalidwe lawo. Koma iwo ndi otsatira a Satana. Ochepa mwa iwo amazindikira ndi

kuyambanso ku njira yolondola. Zonena zao zimawoneka za ulemu, zosangalatsa kapena zothandiza, koma zonse zomwe amaganiza ndi kukonda ndi zoipa. Amanyenga zitsiru ndi kutsotsogolera ku mpatuko ndi chitayiko. Mawu awo amawoneka owala ndi opanda banga, koma, akayikidwa pa mbalambanda –pa chowonadi, amasungunuka. Anthu oyipa a m'maudindo achipembedzo amenewa, omwe mitima yawo yadetsedwa ndi kumatidwa ndi Allahu Taala, amatchedwa **ahl al-bida** kapena **anthu osatsata madhhabi** achipembedzo. Ndi anthu omwe zikhulupiriro ndi zochita zawo sizigwirizana ndi **Quran al-karim**, ndi Hadith sharif kapena ndi Ijma al-Umma. Popatuka kuchokera ku njira yolondola, Iwo amasokeretsanso Asilamu. Anthu omwe angatsatira iwo, adzakatera ku Jahannama. Kunali ampatuko ambiri otere m'nthawi ya Salaf as-salihin ndi mwa anthu a udindo wa chipembedzo omwe anabwera pambuyo pawo. Kupezeka kwawo pakati Asilamu kuli ngati chotupa [kapena kansa] pa mbali ina ya thupi. Pokhapokha mbali iyi itathetsedwa, mbali za thanzi sizidzathawa chionongeko. Iwo ali ngati anthu amene akudwala matenda opatsirana. Anthu omwe amakumana nawo adzatengera matendawo. Tiyenera kutalikirana nawo kuopera kuti angatipweteke nawo." M'modzi mwa anthu ovunda, ampatuko a maudindo achipembedzo amene wakhala akuwononga kwambiri ndi Ibn Taymiyya. M'mabuku lake, makamaka **Al-wasita,** sakugwirizana ndi **ijma al-Muslimin**, akutsutsana ndi zomveka bwino zolengeza mu **Quran al-Karim** ndi Hadith sharif ndipo satsata njira ya Salaf as-salihin. Kutsatira malingaliro ake olakwika ndi maganizo oipa, iye analowa mu mpatuko. Iye anali munthu wa kudziwa zambiri. Allahu Taala anapanga kudziwa kwake chiyambi cha kumpatuka ndi kutayika kwake. Adatsata zofuna za Nafs yake. Ayesa kufalitsa maganizo ake olakwika ndi ampatuko m'dzina la choonadi.

Katswiri wophunzira wamkulu, Ibn Hajar al-Makki rahmat-Allahi Taala alaih analemba m'buku lake **la Al-fatawa al-Hadithiyya**: "Allahu Taala anamupangitsa Ibn Taymiyya kugwa mu mpatuko ndi chiwonongeko. Anamupanga kukhala wakhungu ndi wogontha. Akatswiri ambiri anadziwitsa ndi kutsimikizira polemba kuti zochita zake zinali za chinyengo zoyankhula ndi zolemba zake zinali za bodza. Anthu amene anawerenga mabuku akatswiri wa chisilamu Abul Hasan as-Subki, mwana wake Taj ad-din as-Subki ndi Imam al-Izz ibn Jamaa, ndi omwe anawerenga mawu omwe ananenedwa ndi kulembedwa pomuyankha iye, Shafii, Maliki ndi Akatswiri a maphunziro a Hanafi okhala mu nthawi yake, adzawona bwino kuti tikulondola.

"Ibn Taymiyya anayankhula zoipa ndi kunyoza akatswiri a Tasawwuf (kuyeretsa mtima, kukula mu uzimu). Komanso sanazengereze kuukira Hazrat Umar ndi Hazrat Ali, omwe anali mizati yayikulu ya Chisilamu. Mawu ake

Anapyola malire ndi ulemu, ndipo adaponya mivi ku ‘ma phompho otsetsereka’ (anthu aja odziwika kwambiri). Iye ananena akatswiri a njira yolondola kuti anali a bidah’, ampatuko ndi mbuli.

Iye anati, ‘Maganizo oipa a anzeru aChigiriki osagwirizana ndi Chisilamu anayikidwa m'mabuku a akuluakulu a Tasawwuf,’ ndipo anayesa kutsimikizira izi ndi maganizo ake olakwa ndi achinyengo. Achinyamata Asilamu omwe sadziwa choonadi angathe kusocheretsedwa ndi zolemba zake za makani ndi zachinyengo. Mwachitsanzo, iye analemba kuti:

‘Anthu a Tasawwuf akunena kuti akuona **Lawh al-mahfuz**[1] yomwe imatchedwa **an-nafs al falakiyya** ndi ma Filosofa monga Ibn Sina(Avicenna). Iwo amanena kuti moyo wa munthu, ukafika pa ungwiro, mzimu umalumikizana ndi an-nafs al-falakiyya kapena **al-aql al-faal** pamene munthu ali mmaso kapena ali mtulo ndipoziwirizi zikalumiikizana, zomwe zimayambitsa chili chonse kutichitika pa dziko la pansi, mzimu wa munthu umadziwitsidwa za zinthu zomwe zilipo mwa iwo. Izi sizinanenedwe ndi ma Filosofa aChigiriki koma ndi Ibn Sina ndi ena omwe anabwera pambuyo pake. Komanso, Imam AbuHamid al-Ghazali, Muhyiddin ibn al-Arabi ndi Andalusian Filosofa Qutb ad-din Muhammad ibn Sabin ananenapo zimenezi. Ndi mawu a ma Filosofa. Zinthu zoterozo mulibe m’Chisilamu. Ndi mitsutso imeneyi iwo anapatuka kuchoka m’njira yowona. Iwo anakhala ma mulhid, monga ma mulhid wotchedwa Shiis, Ismailiyya, Qaramitis ndi Batinis. Anasiya njira yoyenera yotsatiridwa ndi akatswiri a Ahl as-Sunna, ndi akatswiri a Hadith ndi anthu a Sunni a Tasawwuf ngati Fudayl ibn Iyad. Pamadzama ndi Filosofe, iwo analibana motsutsa magulu monga a Mutazila ndi Kuramiyya mbali inayi. Pali magulu atatu a anthu a Tasawwuf: gulu loyamba amatsatira Hadith ndi Sunna; gulu lachiwiri ndi anthu ampatuko ngati a Kuramiyya; gulu lachitatu ndi otsatira za mabuku a **Ikhwan as-safa** ndi mawu a Abul Hayyan. Ibn al-Arabi ndi Ibn Sa’bin ndi ena otengera nzeru za ma Filosofa koma omwe anaonetsa ngati mawu a anthu a Tasawwuf. Buku la Ibn Sina **Akhir al-isharat ala maqamil-arifin** lili ndi ziganizo zambiri zotero. Komanso al-Imam al-Ghazali anakambanso zofanana ndi mawuwa m'mabuku ake ena, monga **al-Kitab al-madnun** ndi **Mishkat al-anwar.** Ndipotu mnzake Abu Bakr ibn al-Arabi anayesa kuti amupulumutse ku zimenezo pomuchenjeza kuti wasokonezedwa ndi Filosofe, koma chenjezo lake silinaphule kanthu. M'malo mwake, al-Imam al-Ghazali ananena kuti ma Filosofa anali osakhulupirira. Chakumapeto kwa moyo wake anawerenga **[Sahih** ya] al-Bukhari. Ena akuti izi zinamupangitsa kusiya malingaliro omwe analemba. Ena ena akuti mawuwo ananenedwa ndi al-Imam al-Ghazali kuti

[1] Kuti mumve zambiri za Lawh al-mahfuz, onani mutu 36 mu **Endless Bliss**, ndime yachitatu.

anyozeke. Pali malipoti osiyanasiyana okhudza al-Imam al-Ghazali pa nkhaniyi. Muhammad Mazari, katswiri wa Maliki yemwe anaphunzira ku Sicily, Turtushi, katswiri wa maphunziro a Andalusi, Ibn al-Jawzi, Ibn Uqail ndi ena ananena zambiri.'

"Zonena zomwe zili pa mwambazi zochokera kwa Ibn Taymiyya zikuwonetsa poyera kuipidwa kwake ndi akatswiri a Ahl as-Sunna. Amayankhulanso motere ngakhale kwa akuluakulu a Swahabah al- Kiram. Adawasala akatswiri ambiri a Ahl as-Sunna kuti ndi ampatuko. Pamene iye amanyoza Walii wamkulu ndi **qutb al-arifin** Hazrat Abul-Hasan ash-Shadhili chifukwa cha mabuku a **Hizb al-kabir** ndi **Hizb al-bakhr** ndi kuwanyozetsa ndi mawu oipa, akuluakulu a tasawwuf monga Muhyiddin Ibn al-Arabi, Umar ibn al-Farid, Ibn Sabin ndi Hallaj Husain ibn Mansur, akatswiri a m'nthawi yake mogwirizanaanamutcha kuti iye anali wochimwa ndi wa mpatuko. Ndipo analiponso omwe anatulutsa fatwa zonena kuti iye adali kafiri.[1] Kalata yolembedwa kupita kwa Ibn Taymiyya m'chaka cha 705 A.H (1305) inati: 'Ee, m'bale wanga wa chisilamu, amene amadziona kuti ndi wophunzira wa mkulu komanso imamu wa panthawiyi! Ndikukusilirani chifukwa cha Allah Ndimawada ophunzira omwe amakutsutsani inu. Koma ndinadabwa nditamva mawu anu osayenera kusirira. Kodi munthu wa nzeru amakayikira zoti usiku umayamba dzuwa likamalowa? Mumati muli m'njira yoongoka ndi kuti mukuchita **al-amru bil-maruf wan-nahyi anil-munkar**. Allahu Taala akudziwa chomwe mukuchita ndi cholinga chanu. Koma ikhlas ya munthu imamveka m'zochita zake. Zochita zanu zachotsa chivundikiro cha mawu ako. Kunyengedwa ndi anthu amene amatsatira ma nafs awo ndi omwe mawu awo anali osadalilika, simunangonyoza anthu a m'nthawi yanu koma mwayikanso anthu akufa kuti ndi osakhulupirira. Pokhutitsidwa ndi kuukira amlowa m'malo a Salaf as-Salihin, mwanyozanso ma Sahabat al-Kiram, makamaka akuluakulu. Kodi munaganizirapo momwe dzikakhalire pa tsiku lachimaliziro, anthu akuluakuluwo akadzafuna ufulu wawo wolemekezedwa? Mutayima pa minbar (guwa mu mzikiti) wa Jami al-jabal mu mzinda wa Salihiyya, munati Hazrat Umar "radiyallahu taala anh" anali ndi mawu olakwika ndi achisokonezo. Kodi chisokonezocho chinali chotani? Ndi chisokonezo chiti choomwe munamva kuchokera kwa Salaf as-Salihin? Mukunena kuti Hazrat Ali "radiyallahu taala anh" anali ndi zolakwa zoposa mazana atatu (300). Zikadakhala zoona kuti izi ndi zoona, kodi inu mukadakhala ndi mawu olondola? Tsopano ndayamba

[1] Katswiri wozama wa chisilamu, Abd al-Ghani an-Nablusi analemba mayina a akuluakulu awa a Tasawwuf pa tsamba 363 ndi 373 m'Bukhu lake la **al-Hadiqat an-nadiyya** ndi kuonjezera kuti aliyense wa iwo aali wali ndi kuti anthu onena zoipa za iwo anali mbuli ndi osadziwa.

kuchita zinthu motsutsana nanu. Ndidzayesetsa kuteteza Asilamu ku zoipa zanuzo, pa kuti mwapyola malire oyenera. Kuzunza kwanu kwafika kwa amoyo ndi akufa omwe. Okhulupirira ayenera kupewa zoipa zanu.'

"Taj ad-din as-Subki anayika mndandanda wa zinthu zomwe Ibn Taymiyya samagwirizanirana ndi Salaf as-Salihin motere:

1- Iye Anati: 'Talaq (kusudzulana monga mwa malamulo a Chisilamu) siyimamveka. Ndikofunikira kulipira kaffara (chilango cha chitetezero, apa chinkatanthauza kuletsa kuthesa banja) polumbira.' Palibe ophunzira wamkulu wa chisilamu yemwe ananenapo kuti kaffara izilipiridwa.[1]

2- Anati: Kumuyankhu mkazi pomwe akusamba (haidh) ndi kosavomerezeka.'

3- Anati: – Adati: 'Qadha (kubweza ibadah nthawi yake itadutsa) ya salat yoyisiya ukudziwa ndi kosafunikira.'

4- Anati: 'Ndi mubah (zololedwa) kwa mkazi kupanga tawaf (kuzungulira Kaba ku Mecca) a kusamba. Sakuyenera kupereka kaffara.'

5- Talaq yofotokozedwa ngati ma talaq atatu ndi talaq imodzibe. Komabe, kwa zaka zambiri asananene zimenezo, anali atanena mobwerezabwereza kutsutsa umodzi wa asilamu (ijma al-Muslimin).

6- Anati: 'Misonkho yosagwirizana ndi Chisilamu ndi halal kwa iwo omwe amatolera.'

7- Anati: 'Misonkho yotoleredwa kuchokera kwa amalonda imakhala ngat zakat ngakhale kuti siyinaperekedwe ndi cholinga cha zakah'

8- Anati: 'Madzi sakhala najs (odetsedwa),ngati mwaferamo mbewa kapena zina zotero.'

9- Anati: 'Ndi zololedwa kuti munthu yemwe ali mu janaba (nthawi yomwe Msilamu akufunika kuziyeretsa, kusamba thupi lonse mwamwambo) kuswali nafila (Ntchito zabwino zowonjezera) ngakhale asanasambe usiku.'

10- Anati: 'Zofunika zoyenera kutsatidwa zonenedwa ndi waqif (wopereka chuma ku bungwe) sizimalabadilidwa.'

11- Anati: 'Munthu yemwe sakugwirizana ndi mngwirizano wa Asilamu (ijma' al-umma) sakhala kafiri kapena wochimwa..'

[1] 'Talaq' yatanthauziridwa ndi kufotokozedwa mwatsatanetsatane m'mutu wakhumi ndi chisanu wa fascicle ya chisanu ndi chimodzi, ndi m'mutu wa chisanu ndi chimodzi wa fascicle ya chisanu m'bukhu la **Endless Bliss**.

12- Anati: ‘Allahu Taala ndi mahall-i hawadith ndipo wapangidwa ndi tizidutswa.’

13- Anati: ‘**Quran al-Karim** inalengedwa mu Dhat (umunthu) wa Allahu Taala’.

14- Anati: ‘Alam, ndiye kuti, zolengedwa zonse ndi zamuyaya ndi mitundu yawo.’

15- Anati: ‘Allahu Taala ayenera kulenga zinthu za bwino.’

16- Anati: ‘Allahu Taala ali ndi thupi ndipo ali ndi mbali; Iye amasintha malo Ake.’

17- Anati: ‘ Gahena si yamuyaya; idzatha kumapeto kwake.’

18- Anatsutsa zoti Atumiki wopanda machimo.

19- Anati: ‘Rasulullah “sallallahu taala alaihi wa sallam” ali ngati wina aliyense. Ndi kosaloledwa kupemphera kudzera mu kupembedzera kwake.’

20- Anati: ‘Ndi kulakwa kupita ku Medina ndi cholinga chokaona manda a Rasulullah.’

21- Ananenanso kuti: ‘Ndi haram kupita kumeneko ndi cholinga chakupembedzera (shafaa).’

22- Anati: ‘**Tawrat** (buku lenileni la **Torah**) ndi **Injil** (**chipangano cha tsopano chenicheni)** sizinasinthidwe mu mawu koma m’matanthauzo,’

“Akatswiri ena ananena kuti zambiri mwa zomwe zanenedwa pa mwambazi sizinali za Ibn Taymiyya, koma palibe yemwe anatsutsapo zoti anena kuti ‘Allahu Taala ali ndi mbali’ ndi kuti ‘Iye anapangidwa ndi tinthu ting'onoting'ono’, [koma samayenera kunena mawu awa]. Palibe kukanira kuti kuzindikira kwake, ukulu wake ndi udindo wake mchipembedzo unali wawukulu. Munthu amene ali ndi maphunziro a fiqh, chilungamo ndi kuganiza, ayenera kuyamba ndi kufufuza pa nkhani kenako ndi kuilingalira mwanzeru. Makamaka, kuweruza Msilamu kuti ndi wosakhulupirira, wa mpatuko kapena wampatuko kapena kumuweruza kuti akaphedwe ndi zofunika kufufuza ndi kusamala kwambiri.”

Masiku ano zakukhala ngati ndi zinthu zapamwamba kutsanzira Ibn Taymiyya. Ena amateteza zolemba zake za chinyengo ndikusindikiza mabuku ake, makamaka bukhu lake la **al-Wasita**. Kuyambira pa chiyambi mpaka ku mapeto, bukuli ladzaza ndi malingaliro ake osagwirizana ndi **Quran al-kerim**, Hadith sharifs ndi ijma al-Muslimin. Zimayambitsa fitna zazikulu ndi kugawikana pakati pa owerenga ndi kuyambitsa chidani pakati pa abale. Ma Wahhabi ku India ndi mbuli za chipembedzo zomwe zidagwidwa mu misampha yake m'maiko ena achisilamu amupanga Ibn Taymiyya kukhala wapamwamba wawo

ndipo ampatsa mayina monga 'Mujtahid Wamkulu' ndi 'Shaikh al-Islam.' Iwo amavomereza malingaliro ake opatuka ndi zolemba zake zonyenga m’dzina la chipembedzo ndi chikhulupiriro. Kuti tithetse mafunde owopsawa, omwe amabweretsa kugawikana pakati pa Asilamu ndi kugwetsa Chisilamu,, tiyenera kuwerenga mabuku amtengo wapatali olembedwa ndi akatswiri a Ahl as-Sunna omwe amatsutsa zolemba zake. Mwa mabuku ofunikirawa, pali bukhu la **Shifa as-siqam fi ziyarati khayri lanam** lolembedwa ndi imam wamkulu komanso katswiri wophunzira kwambiri Taqi ad-din as-Subki rahmat-Allahi Taala alaih. Bukhuli likuwonongeratu malingaliro ampatuko a Ibn Taymiyya, kuchotsa gulu lake ndi kuwulula kukakamira kwake. Linapewetsa kufalikira kwa zolinga zake zoipa ndi zi khulupiriro zolakwika.

# MATANTHAUZO A MAWU ENA

Zolemba zokhuza Tasawwuf (Sufism) zitha kuphunziridwa bwino kuchokera kwa Hazeat Ahmad al-Faruqi as-Sirhindi's (Imam Rabbani) **Maktubat.**

**abdast**: wudhu.

**abid**: munthu yemwe amayesetsa kupanga ma ibadat onse.

**ada:** kupanga magawo atatu a mapemphero mu nthawi yake.

**adab:** makhalilidwe abwino a chisilam

**adala**: chilungamo, chimodzi mwa makhalidwe a aneneri

**adam**: zolengedwa zonse panalibe izo zisadalengedwe

**adat**: miyambo.

**adat-ilahiyya**: Chifukwa.

**adhab**: chilango.

**adhan**: kuitanira ku(salat).

**Adilla Al-Shariyya**: nkhani za chisilamu zotengedwa ku magwero anayi (Quran al-Karim, Sunna, qiyas al-fuqaha, ijma al-Umma).

**af'al al-mukallafin**: malamulo, zoletsedwa komanso zoleledwa

**afw:** chikhululuko.

**ahadith ash-Sharif**: zoyankhula, zochita ndi zokonda za Mtumiku Muhammad (salallah alaihi-wasalam).

**Ahkam ash-Shar'iyya**: malamulo a chisilamu.

**ahadith qudsi**: matanthauzo a mu Quran al-Karim a Allahu Taala koma a mawu a Muhammad (salallahu alaihi-wasalam).

**Ahkam fiqhiyyah**: malamulo a chisilamu, zomwe zalamulidwa ndi zomwe zaletsedwa.

**Ahkam Ilahiya**: malamulo a Allahu Taala.

**Ahkam Islamiya**: zoyenera kuchita ndi zoletsedwa mu chisilamu.

**ahkam ijtihadiyya**: ahkam yomwe ingamvetsetsedwe kudzera mu ijtihad.

**ahkam**: malamulo opangidwa utaona zinthu

**ahl al-bida**: anthu opatuka ku njira ya Ahl as-Sunna.

**Ahl al-Kitab**: anthu a mabuku ovumbulutsidwa.

**Ahl al-qibla:** omwe amapembeza poyang'ana ku kaaba.

**Ahl as-Sunna wa'l Jamaa:** chikhulupiriro cholondola cha Chisilamu

**Ahl as-Sunna**: zikhulupiriro za mawu a Allahu Taala, zopangitsa munthu kukhala msilamu.

